# *Khristu Ndi Chinsinsi Cha Mulungu Woululidwa*

Zikomo inu, M'bale Neville. Ambuye akudalitseni inu. Tiyeni tingotsala chiyimire kamphindi pamene ife tikuweramitsa mitu yathu ku pemphero.

2 Atate Akumwamba achisomo, ife tikukuyandikirani Inu kachiwiri mmawa uno pofuna chifundo ndi pofuna kutsogolera kwa Mzimu Woyera lero, pamene ilo latulukira pa ife, kuti ife tikhoze kukomana limodzi mmawa uno ndi kudzaphunzitsa Mawu Anu, ndi kuti ife tikhoze kudziwa momwe tingakhalire moyo mu tsiku liripo ili, ndi yomwe ili nthawi ya tsiku limene ife tiri nkukhalamo. Ife tikupempha kutsogolera Kwanu kopatulika ku malingaliro athu, mitima yathu lero, kuti Inu mutilondolere ife ku Mawu aliwonse amene ali ofunikira kwa ife kuti tiwadziwe; kuti Inu mutsegule kamwa zathu momasuka, ndi mitima yathu, nayonso, kuti ilandire, icho chimene Inu muti muyankhule kwa ife, ndi kuti mutseke kamwa zathu ku zinthu zimene siziri zolondola, podziwa kuti Inu nokha mukhoza kuwulula Mawu a Mulungu.

3 Ndipo tsopano pamene ine ndiyenera kuti ndiwusiye mpingo waung'onowu pomwe pano tsopano waku mbali zina za dziko lapansi, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, Ambuye. Chimene, iwo ali mtima, apulo ya mtima wanga, mwa kuyankhula. Iwo ndiwo—amene abalidwira kwa Inu, mwa Mzimu ndi mwa Mawu a Choonadi. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo, Ambuye, ndipo muwasunge iwo olukana mothinana limodzi ndi zimango za chikondi cha Khristu.

4 Mdalitseni m'busa wathu wokondedwa, wolishya. Ife tikupemphera kuti Inu mumudzoze iye ndi Mzimu Woyera, wa Mawu Anu, ndipo muwululire kwa iwo ndi kulidyetsa gululi.

5 Ndipo kamodzi, basi kanthawi kapitako, pamene Inu munasonyeza masomphenya, kachisi wamng'ono pano, akuti ndisunge Chakudya, kuti pakanati padzafike nthawi yomwe ichi chonse chikanati chidzafunikire. Pamene ife tinamuwona M'bale Sothmann ndi M'bale Woods atakonzeka kuti awolokere ku dziko linalo, kuti. . .Koma Inu munati, "Sunga Chakudya ichi pano kwa kanthawi." Ambuye, molemekeza ine ndayesetsa kuti ndichite zimenezo.

6 Ndipo tsopano, mmawa uno, mu phunziro ili limene ife talilingalira, ine ndikupemphera kuti Inu mutseke ilo lonse, Ambuye, kuti musonyeze kuti Ndinu Mulungu, ndipo awa ndi Mawu Anu ndi Choonadi Chanu. Perekani izi, Ambuye, kuti

anthu akhoze kumadya kuchokera pamenepo ndi kumakula monenepa, monga izo zinkakhalira, mu chisomo cha Mulungu, kuti iwo akhoze kuwona kuti ndi chifundo chachikulu cha Mulungu kwa ife mu tsiku lino. Muwadalitse onse amene alipo ndi iwo amene akanafuna kuti akhalepo, Atate. Ndipo mudzitengere ulemelero kwa Inumwini, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

Ambuye adalitse wina ndi aliyense wa inu tsopano.

7 Ndipo ine ndikukhulupirira, basi ife tisanayambe, ife tiri ndi mwana wamng'ono pano, Collins. Ine ndinakomana nawo abambo ake mphindi zingapo zokha zapitazo, ndipo—ndipo iwo anali ndi mwana wamng'ono yemwe iwo amafuna kuti adalitsitsidwe. Ndipo ife tikufuna kuti tichite zimenezo tsopano, ngati M'bale kapena Mlongo Collins, mmodziyo, angamubweretse wamng'onoyo kutsogolo kuti tikhoze kukhala ndi utumiki wodalitsitsa mwana wamng'ono uyu.

8 Pochoka, inu mukudziwa, bwanji, izo zimayambitsa... monga awa ali mamembala odzipereka kapena, ali, a Thupi la Khristu. Inu mukuzindikira, ine sindinati konse "a kachisi." "A matupi a Khristu," a... thupi ili pano, gawo la Thupi Lake.

9 Ndipo iwo ali ndi mwana wamng'ono pano yemwe iwo akufuna adalitsitsidwe. Ndipo—ndipo iyi nthawizonse imakhala ntchito imene ndikuganiza wanga—mkazi wanga amandisirira ine, ndikamanyamula ana. Uh-huh. Ndipo M'bale Neville, ngati mungabwere patsogolo, ngati inu mungatero.

10 Kodi dzina lako loyamba ndi ndani, m'bale? [Bambo akuti, "Clyde."—Mkonzi]. Uyu ndi M'bale ndi Mlongo Clyde Collins, ndi mchimwene kwa m'bale wathu wofunika pano, M'busa Collins, Willard. Ndipo iwo akhala nako kuwonjezereka kwa chiwerengero cha a Collins pano, ine ndikuwona, ndi kamunthu kokongola kwambiri kakang'ono.

11 Ndi wamkulu bwanji iye, Mlongo Collins? [Amake akuti, "Pafupifupi miyezi foro."—Mkonzi]. Pafupi miyezi foro. Ndipo kodi dzina lake ndi ndani? ["Mark David."] Mark David. Ilo ndi dzina labwino kwambiri. Iye akuwoneka ngati mnyamata wabwino kwambiri. Titi, iye ali ngati mnyamata wamkulu, naponso.

12 Tsopano ine ndikudziwa azimayiwa pano akhoza kumuyamikira mwana wamng'ono uyu pano. Kodi icho si chidole?

Chabwino, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu tsopano.

13 Atate Akumwamba, pamene bambo wamng'ono uyu ndi mayi abwera ndi wamng'ono uyu, chinthu chofunika cha mnofu waumunthu amene waperekedwa ku chilumikizano chawo, wayikidwa mmanja mwawo kuti amusungire kwa Ambuye Mulungu. Iwo molemekeza akumubweretsa Mark

David wamng'ono uyu pano kudzamudalitsitsira kwa Wamphamvuzonse, Yemwe wawapatsa mnyamata wamng'ono wofunika uyu, wathanzi labwino ndi mnyamata wabwino, mu chisamaliro chawo, kuti aleredwere kwa ulemelero wa Mulungu.

14 Ambuye, muwadalitse abambo ndi amake. Mulole mbiya isamathe konse, ku nyumba, kapena msupa isamawume konse. Mulole bambo azikhala abwino bwino ndi othekera, Ambuye, kuti azigwira ntchito ndi kupanga chakudya cha mwana wamng'ono uyu; mulole amayi ake akhale abwino bwino ndi wokhoza kumachikonza icho; ndi mitima yawo yokonzeka, Ambuye, kuti azimuphunzitsa mwana wamng'onoyu, kuti amulere iye mwa kuwopa Mulungu. Perekani izi, Ambuye.

15 Tsopano kuchokera mmikono yawo, kupita ku yanga, mwabwera mwana wokondeka uyu, Mark David wamng'ono. Ndipo ine ndikumupereka iye, limodzi ndi eledara wa mpingo pano, kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu, ku moyo wa utumiki. Perekani izi, Ambuye. Mulandire ulemelero kuchokera mmoyo wake. Mulole iye akhale moyo wautali, ngakhale mpaka Kudza uku kwa Ambuye Yesu, ngati icho chingakhale chokondweretsa kwa Inu. Ndipo, ngati ziri chomwecho, mulole iye afike poti adzanyamule Uthenga wa Ambuye Mulungu, mu m'badwo umene uli nkudza. Perekani izi. Musungeni iye wathanzi, wokondwa, ndipo mulole mtima wake nthawizonse uzikhala utakhazikitsidwa pa kuchita zinthu zimene ziri zolondola, pamaso pa Mulungu. Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikumupereka mwanayu kwa Inu, mwa kumudalitsitsa. Ameni.

16 Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, Mlongo Collins, ndi mnyamata wabwino uyu, ndi inu M'bale Collins. Mulungu akhale ndi inu.

*Abweretseni Iwo Abwere,* tonse ife limodzi:

> Abweretseni iwo abwere, abweretseni iwo abwere,
> Abweretseni iwo kuchokera kuminda ya tchimo;
> Abweretseni iwo abwere, abweretseni iwo abwere,
> Abweretseni aang'onowo kwa Yesu.

17 Ine ndimaikonda imeneyo. Mukuona, abweretseni iwo kwa Khristu mdierekezi asanakhale nawo konse mwayi. Iwo aperekedwa kale kwa Iye pamenepo kwa moyo wa utumiki.

18 Pali aliyense akudziwa ngati banja la a Dauch, aliyense wa iwo, afika kuno lero, kapena ayi, Mlongo Dauch? M'bale Brown, kodi inu muli pano, M'bale Brown? Inde, ndine wokondwa. Ndipo. . .M'bale Dauch akadali ndi ife? Zodabwitsa! [M'bale Tom Brown akuchitira ndemanga za momwe M'bale William Dauch aliri—Mkonzi]. M'bale Dauch anatsala pang'ono kuti atisiye ife. Mwaona, ife sitingakhoze kunena zochuluka

kwambiri kapena kupempha mochuluka kwambiri, iye ali kale zaka twente wani kudutsa nthawi imene Mulungu anamuuza iye kuti adzakhalire moyo. Ndiyo nthawi ya moyo wamba, kupitirira nthawi imene Mulungu anamuuza iye kuti angakhoze kukhalira moyo.

19 Koma ife tinaitanidwa tsiku lina, kuti iye anali—iye anali akufa, ndipo ife tinathamangira kumeneko. Ndipo Ambuye Mulungu anali wabwino kwenikweni kwa iye, amusunga iye. Basi, ine ndikuganiza iye—iye ndi wokonzeka ndipo akungoyembekezera Kudza kwa Ambuye. Koma, inu mukudziwa, ife tonse timagwiriirabe kwa wina ndi mzake. Ife basi. . .Munthu wachikulireyo ali ngati—ngati bambo kwa ine pano.

20 Ine ndikukumbukira iye atakhala pansi momwe muno mu Kachisi wakale, gawo lakale, pamene iye. . .Kuwala kuja kunawalira modutsa, pa ubatizo wa mmadzi uja mu Dzina la Yesu Khristu, kuchokera pamenepo iye anabwera. Ndipo pafupifupi eyite-seveni kapena usinkhu wa zaka eyite-eyiti, akuyendera ndodo, anabwera pomwe pano ndipo anati, "Ine ndikufuna kuti ndilowe mmenemo ndi kubatizidwa." Winawake anapita ndipo anakamutengera iye zovala zina. Iye sakanakhoza kudikirira mpaka nthawi ina; iye anayenera kuti abwere nthawi yomweyo, nthawi yomweyo. Chotero ine—ine ndimazikonda zimenezo.

21 Iye anati, tsiku lina, ine ndinali kuyankhula ndi iye; iye anati, "Kodi inu mukuganiza kuti ine ndiri bwino bwino tsopano, M'bale Branham?"

22 Ine ndinati, "Kodi inu munayamba mwapita kwa dokotala kukapimidwa mthupi?"

Iye anati, "Inde, bwana."

23 Ine ndinati, "Dokotala amaika zomverera mmakutu ake, ndi kuziyika izo pa mtima wanu, kuwona ngati mtima wanu ukugunda moyenera; ndi chowonera chamagetsi, ndipo kenako kuthamanga kwa magazi, kudzayeza mikodzo, ndi zina zotero, zipangizo, kuti apeze pamene umunthu wanu uli. Tsopano, momwe iye amachitira zimenezo, iye amayang'ana mmbuyo—bukhu apa, pamene akatswiri pa maphunziro osiyanasiyana awa amalembapo, 'Ngati *ichi* chichitika, ichi ndi chimene chavuta.'"

24 Ndipo ine ndinati, "Tsopano, chomvererera chokha chimene ine ndiri nacho ndi Baibulo, mwaona, kwa solo." Ndipo ine ndinati, "Ine ndikupimani inu." Ine ndinati, "Yohane Woyera 5:24, anati, 'Iye amene amva Mawu Anga.'" Ine ndinati, "Kumeneko si kungokhala ndi kumamvetsera kwa Iwo. Uko ndi kuwalandira Iwo, mwaona, kuwalandira Iwo; iweyo kuwakhulupirira Iwo. Chinachake mkati mwako chimakuwuza iwe kuti Iwo ndi olondola. Iweyo wawalandira Iwo, iweyo ukuwakhulupirira Iwo, Iwo ndi ako. 'Iye amene awamva,' Iwo

ndi ako kale, 'Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene ananditumа Ine.' Inu mukukhulupirira zimenezo?"

Iye anati, "Ine ndikutero."

25 Ine ndinati, "Ndiye ine ndikuuzani inu chimene Dokotala Wamkulu ananena, 'Iye wachoka ku imfa wapita ku Moyo, ndipo sadzabweranso konse ku chitsutso kapena chiweruzo.'" Ine ndinati, "Monga momwe ine ndikudziwira, malingana ndi Mabuku, inu mwapambana mayeso."

26 Bambo wokalamba uyo, wa pafupifupi usinkhu wa zaka handiredi, osati munthu wa tchalitchi nkomwe; koma basi nthawi yoyamba imene Kuwala kunadzang'anima kudutsa panjira yake, iye anakulandira Iko. Mukuona mbewu yokonzedweratu ija inali itagona mmenemo? Uh-huh. Inde, bwana. Mwaona, mwamsanga pamene Kuwala kuigunda iyo, iyo imabwera ku Moyo mwamsanga ndithu.

27 Tsopano, ine ndikudziwa kwatentha lero, ndipo ine, ndikuwona ngati kuti ndi zovuta kuti ine ndikuitanireni inu anthu pamodzi ku msonkhano kumene mudzakhale mothinana monga chomwechi. Komabe ine—ine ndinaganiza, mwa chisomo cha Mulungu, kuti ndikanati ndidzakhale ndi msonkhano wina ndisanakusiyeni inu nonse; kwa nyengo ya yaifupi, ine ndikudalira.

28 Ndipo ndiyenera kuti ndizipita tsopano mawa usiku, ku Chicago, kuti ndikayambe Lachitatu. Ine ndinaganiza kuti ndikafike kumeneko molawirira pang'ono, ngati nkotheka, ndi kukapumula pang'ono tisanayambe mndandanda wa msonkhano. Ndipo ine ndikukhulupirira iwo ali nayo iyo. . . Apa, ine ndinali kuyang'ana pa zimenezo apa pomwe. Izo—izo zalengezedwa kumeneko. Iko kumatchedwa Marengo. . . [Wina akuti "Marigold."—Mkonzi.] . . . deralo, eya, Marigold, Marigold, eya, deralo, bwalo. Marigold Arena ndi kumene ikukachitikira, kuyambira Lachitatu usiku, kudutsa Lamlungu. Ndipo a Full Gospel Business Men akakhala ndi kadzutsa, nawonso, pa—Loweruka mmawa. Ndipo ine sindikudziwa ndendende basi kumene iwo alengezera izo, kuti. Ayi. Kenako Loweruka madzulo ku Lane Tech. Ine ndikuwona apa—izo zalengezedwa.

29 Tsopano, ngati inu muli cha ku dera limenelo, kapena kumtunda uko, iwo ukakhala wachizolowezi, msonkhano wachizolowezi basi wa uvangeli monga timakhalira nawo pa nthawi iliyonse. Ochuluka a Mauthenga akakhala moyambirira pa chinachake chimene chaphunzitsidwa pano, chifukwa kuno ndi kumene ife timapanga matepi athu, inu mukuona. Kunja uko iwo akhoza kumatsutsa. Koma ngati iwo atenga matepi amene apangidwa kuchokera pano, zimenezo zikakhala ndi iwowo ngati iwo akufuna kuti amvetsere ku tepi iliyonse. Iwo amabwera kuchokera pano. Ili ndi guwa lathulathu.

30 Chotero kunja uko, kawirikawiri ine ndimayesetsa kuti nditenge chinachake chimene chisali chakuya kwambiri, chifukwa ambiri a iwo ndi osaya mu zowachitikira ndi zimene zimabwera mmenemo. Koma pano ine ndimamverera kuti ndiri nawo ufulu wonena chirichonse chimene Mulungu angayike pa mtima wanga, kuti ndichinene icho kuchokera pomwe pano. Chotero matepi athu onse amapangidwa kuchokera pomwe pano. Mukuona? Ndipo iwo ali mchipinda umo pakali pano, inu mukhoza kuwona mitu yawo mmwamba pa galasi la mdimalo mmenemo, momwe iwo akhala ndi marekoda awo.

31 Tsopano, ndipo ngati inu mukufuna kuti mudzabwere ku msonkhanowo, ife tidzakhala okondwa kwambiri kudzakhala nanu. Basi, ngati mudzafike kumeneko, simukudziwa basi koti mupite, bwanji, mudzangofunsa aliyense wa anthu a Full Gospel, kapena—kapena M'bale Carlson, ndipo iye adza—iye adzakuuzani inu kuti. . .Iye akhoza kudzakulangizani inu, kapena Mpingo wa Filadefia, kapena aliyense wa iwo, iwo akhoza kudzakuuzani inu momwe mungakafikire ku malowo.

32 Ndiye ine ndidzabwerera Lolemba lotsatira usiku, nthawiyina, madzulo kapena usiku. Ndipo Lachiwiri ife tidzabwerera ku Arizona kuti—kuti tikawaike ana ku sukulu, ndi zina zotero. Ndiyeno ine sindikudziwa ndendende basi kuti ndidzabwerereranso liti, chifukwa, Ambuye, ine ndikufuna kuti Iye anditsogolere ine basi choti ndichite.

33 Chinthu chachirendo kwambiri chinachitika. Ine mwina ndikhoza. . .ine ndikudziwa izi zikujambulidwa, ndipo ine mwina ndikhoza kungoziyika izi apa. Ndipo pamene masomphenya ndi kutsogolera kwa Mzimu Woyera kukusuntha, ine ndimakonda kungogunda ndendende basi pamene Iwo ukusuntha. Ndizo. . .Tsopano, mu chaka chathachi icho chakhala chimodzi, motsatira kumene ndi imodzi ya nthawi yopambana kwambiri ya masomphenya amene ine ndinayamba ndakhalapo nawo, mu utumiki wanga wonse, chakhala chiri chaka chatha ichi, pa zinthu zimene zachitika, zimene anthu in mukudziwa kuti zinanenedweratu izo zisanachitike, ndipo izo zinadzachitika basi mwanjira imene izo—izo zinanenedwera.

34 Tsopano, ife tabwerera kuno, ndi—ndi kuti tidzacheze. Nyengoyi ku malo ano, ine ndithudi sindimaikonda, chifukwa ine. . .zimangondiswa ine mwamsanga basi pamene ine ndifika kuno. Ndipo ine basi. . .Ine ndikhoza kuwoloka pamwamba pa zitunda kumtunda uko ndi kubwera kuno mu chigwa ichi, ndipo ndikakhala kuno pafupifupi maminiti teni ndipo ine ndimatenga chimfine, ndimadwala. Nyengoyi, chizungulire-chamutu, chirichonse chimawoneka mwachimbuuzi, chamdima, ndipo ine—ine ndimangoyenera kuti ndichokeko. Mukuona? Ndipo tsiku lina ine ndinali kuyankhula ndi mkazanga. . .

35 Koma chimene chimandibweretsa ine kuno, choyamba,

chimene chimandibweretsa ine kuno, ndi anthu inuyo, mwaona, mpingo uno. Ine ndikukuuzani inu, mwa malo onse amene ine ndinayamba ndapitako mmoyo wanga, ano ndi malo anga amene ndimawakonda kubwerako kudzalalikira Uthenga. Ndipo zimawoneka ngati kuti ife tikhoza kupanga tepi kuchokera pano imene ili yabwino ka teni kuposa kwina kulikonse. Mukuona? Mwaona, ndi chifukwa chake ine ndikuti, "Kumene Mulungu akuchita chinachake, ndiye uzikhala kumene ndi chimenecho." Koma ine ndikuganiza, kumene kuli chinthu chopambana, chimenecho chinali ine kulephera kuti ndipite kunja pa nthawi yoyamba pamene Iye anandiyitana ine, ndipo chotero Iye amazipanga izo kukhala ngati zovuta pa ine pamene ndibwera kuno. Kumvera ndi kwabwino kuposa nsembe.

36 Ndiyeno ine ndikhala ndikumabwera kuno ndi kumapitanso, nthawi zonse, kudzalalikira mu kachisi. Ndipo anthu inu amene muli ochokera kunja kwa tawoni, inu muzidziwitsidwa. Billy Paul akhala ali kuno, mu ofesi momwemu, ndipo—ndipo ndikhoza kufikiridwa pa nthawi iliyonse, kudutsira mwa iyeyo. Ndipo tizikhala tikubwerera kuno, kudzachititsa. . .Ndiyeno Malipenga Asanu Ndi Awiri akubwera apo pomwe, Ambuye akalola, Miliri Isanu Ndi Iwiri Yotsiriza, ndi Mbale, ndi zina zotero, basi monga ife tingathere, kutenga nyengo yozizirira pang'ono, mwinamwake, kapena chinachake, mulimonse Ambuye angatsogolere.

37 Ndipo tsopano, tsiku lina, ndikubwera kuno, panali funso limene linabweretsedwa la chinachake, za wina yemwe anandipatsa ine che—cheke, ndipo icho chinati "chawekha," ndendende kwa ine ndekha, ndipo ine ndekha, "chosalipitsidwa msonkho, chaulere," china chirichonse. Chabwino, ife tinapita, ndipo Billy ankadziwa kuti ine ndimachisowa cheke chimenecho, pamenepo.

38 Iye anapita ndipo anakawafunsa azamalamulo ngati ife tingakhoze kukachikasha icho. Iye anati, "Bwanji, iye ndi mbadwa ya Amereka. Chifukwa chiyani kuti iye asachikashe icho? Mukuona, chikuti 'cholipiriridwa msonkho,' ndi china chirichonse, 'chaulere.' Mbadwa iliyonse ikhoza kuchita zimenezo."

39 Chotero ndiye iye samakhutitsidwa nazo zimenezo, Billy, chotero iye anapita kwa owerengera chuma cha anthu. Iye anati, "Bwanji, ndithudi, iye akhoza kukasha icho." Anati, "Iye ndi mbadwa ya United States."

40 Chotero, chabwino, iye amalephera kuti amverere bwino za zimenezo, chotero iye anamuimbira Merle Miller, ameneyo ndi mkulu wa—gulu la msonkho laku—laku Indianapolis uko, anali wotiyimira pa mulandu wathu, ndipo chotero Ice ndi Miller. Chotero, "Zedi, izo ziri bwino. Mukuona? Zedi, iye akhoza kutenga cheke chimenecho. Icho—icho—icho chalembedwera

kwa iyeyo, 'wolembedwera yekhayo.'" Ine ndikhoza kokha, ndine ndekha ndingakhoze kulemba pa icho, zina zotero, ndipo icho sichikanakhoza kudindidwa ndi chathu. . .

41 Mukuona, ine sindimakasha macheke. Ndicho chimene iwo anandipezeketsera nacho ine nthawi ina. Winawake anandibweretsera mulu wa macheke, ndipo anati, "Apa, M'bale Branham," pa msonkhano. Ine ndimati, "William Branham, William Branham. . . " Chabwino, boma linali kusamalira za izo zonse, nthawi zonsezo. Ndipo ine ndimasainira iwo kwa mwiniwanga ndipo ndimakalipirira ngongole kunja uko, koma iwo anati ine ndinali ndi ngongole ya kusasamala pa izo zonse, mulimonse, madola firii handiredi sauzande. Chotero—chotero ndiye ndi pamene panabwerera mkangano.

42 Chotero ndiye mwamsanga pamene ine ndinachiyika cheke ichi mmenemo, phamu, apa inadzabwera nthumwi pomwepo, inati, "Ife timutseguliranso iye mulanduwo tsopano." Chotero izo zinapangitsa izo kukhala ngati zovutirapo.

43 Ndipo M'bale Lee Vayle ali pano, ine ndikulingalira zonse ziri bwino kuti ndizinene izo, ife basi. . .Iye anabwera kuno, ndipo sikolala wabwino uyu wa Chibaptisti pano anali. . .Ine ndinamubatiza iye mu Dzina la Yesu Khristu, kuno mu dziwe tsiku lina, M'bale Lee Vayle. Ndipo chotero iye ndi munthu wabwino kwenikweni, m'bale mwa Khristu. Iye anatilalikirapo ife pano, ndi wophunzira mwaluntha lapamwamba, ndipo, pambali pa zimenezo, munthu wotsogozedwa ndi Mzimu. Pamene Kuwala kunang'anima kudutsa pa iye, iye anati iye anayesetsa kuti achokepo, koma sakanakhoza basi kuchita zimenezo, chotero ine ndinamubatiza iye pomwe pano mmawa wina. Sakanakhoza kupirira izo kenanso, chotero ife tinangobwera kuno ndi kudzavala zovala zathu ndipo tinalowa mmenemo, ndipo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.

44 Chabwino, ine ndinaganiza, pokhala kuti iye anali atadya chakudya chabwino chauzimu chimenecho, mwinamwake kuti tiyankhule pang'ono pokha ife tikadye chakudya china chathupi. Chotero ife tinapita uko ku Blue Boar, ndipo tinakakhala pansi, tinali kuyankhula, ndipo phunziro linabwerapo, "Bwanji inu mumawalola anthu kuti aziyankhula za inu monga chomwechija?"

45 Tsopano, M'bale Vayle ndi mmodzi wa anthu abwino kwambiri amene ine ndinayamba ndawadziwapo, koma iye "amakhala waphuma kwambiri pang'ono pa chokhethemulira," ine nthawizonse ndimamuuza iye, inu mukudziwa. Ndipo chotero, iye, chotero ine ndinati. . .ine ndikuyembekeza izo zonse ndi zabwino bwino, M'bale Vayle. Chotero iye. . .ine ndinati, "Usamanyanyuke nazo pakamodzi. Uzikhala modekha. Mulungu ndi Yemwe amachita zimenezo."

46 Iye anati, "Ah, izo zikhoza kukhala zabwino kwa inu," iye anati—iye anatero. Koma, chabwino, iye—iye. . .ine ndikukhulupira iye—iye ndi wanzeru kwambiri mpaka ndi zimene iye amakomana nazo, anthu aluntha anzeru amenewo; chotero iye amangodziwa momwe angatsanulire izo mmenemo, ndipo iwo samakhala ndi malo aliwonse oti ayimepo. Ndizo zonse.

47 Chotero ine ndinati, "Taona, M'bale Vayle." Ife tinali titakhala ku Blue Boar. Ine ndinati, "Davide, tsiku lina, atachotsedwa pa mpandowachifumu ndi mwana wake yemwe, anamuthamangitsa pa mpandowachifumu, kugalukira, Israeli atagawanika, ndipo Davide anachotsedwa pa mpandowachifumu ndi mwana wake yemwe, ndipo anali akupita kunja kwa mzindawo, akulira. Ndipo mwamuna yemwe sanaukonde uthenga wake wa tsiku lotsiriza, inu mukudziwa; iye sankasamala za iye; bambo wokalamba pang'ono, wokhala ngati wolumala, akupita cha kumeneko, akumutonza iye, ndipo iye anamulavulira Davide. Ndipo mlonda uja anasolola lupanga lija, anati, 'Ine ndisiye mutu wa garu ameneyo ukhale pa iye, yemwe walavulira pa mfumu yanga?' Davide anati, 'Msiye iye yekha. Ambuye wamuuza iye kuti achite zimenezo.' Mukuona? Atalavulira pa iye, kupanga zomutonza iye, ndipo kenako nkulavulira pa iye. Anati, 'Ambuye amuuza iye kuti achite zimenezo.'" Chabwino, ife tikuidziwa nkhaniyo, momwe iyo inabwererera. M'bale Vayle anaganiza kuti izo zinatengera chisomo chochuluka kwambiri kuti uchite zimenezo.

48 Chotero ndisanabwerere nkomwe ndi kukalowa mu ofesi, wowerengera chuma cha anthu anamuimbira Billy Paul ndipo anamuuza iye za izi. Chotero M'bale Vayle anapita ku nyumba ndi ine. Pamene ndimalowa, ine ndinati kwa mkazanga. . . Mochedwa pafupifupi nthawiyina kumadzulo. Ife tinapita mchipinda. Ine ndinati, "Ine ndiri ndi chinachake choti ndikuuze iwe, Wokondedwa."

49 Ife tinali titangoyankhula ine ndisanachoke. Iye anati, "Bill, ine ndikudziwa kuti Mulungu anakutuma iwe kunja uko; ife tonse tikudziwa zimenezo, koma iye sanakuuze konse iwe kuti ubwerere. Iye anati. . .Tsopano, ndipo pamene ine ndikudandaula napo."

50 Ine ndinati, "Chabwino, ine ndikuganiza izo ndi chifukwa cha iwe ndi ana. Palibe vuto kwa ine. Ine ndipita ndikamutumikire Iye, Ambuye akalola, kulikonse kumene ine ndingapite." Ndipo chotero ndinabwerera, ndipo ndinamuuza iye za zimenezo monga choncho. Chotero ine ndinangotembenuka pamenepo, ndinakhazika chipewa changa pamenepo.

51 Ndipo winawake ananena chinachake, chakuti, "Oh, wosonkhetsa msonkho uyu! Ife tiyenera kuti tizipita. . ."

Anangokhala ngati waukira chinachake monga choncho.

52 Mopanda kuganiza za chimene ine ndinali nditamuuza M'bale Vayle, ine ndinati, "Msiyeni iye yekha. Mwinamwake Ambuye amuuza iye kuti achite zimenezo."

53 Ine ndisananene mochuluka zimenezo, Kuwala kunadzang'animira pa khoma ndipo kunalemba pamenepo, M'bale Vayle ndi mkazanga atakhala pamenepo, "Bwerera ku Arizona." Ndi zilembo zitalembedwa pa khoma, "Bwerera ku Arizona." Ndiko kulondola. Chotero apa ine ndikupita, ameni, kubwerera ku Arizona.

54 Tsopano, sabata ino yakhala sabata ya madalitso aakulu. Ife tinali ndi kuyankhulana kwapadera sabata ino, ndi anthu amene akhala akuyembekezera chiyambireni *Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri*. Ndipo ine sindikukaika koma ena a iwo, ndithudi, anaitanidwira mmenemo kuchokera kunja kwa tawoni, kudutsa fukoli. Koma mmawa zoyankhulanazo zisanayambike, nditakhala mchipinda, Mzimu Woyera unandirola ine kuti ndilembe ndendende chirichonse chimene iwo amachidziwa, chirichonse chimene iwo ankafuna kuti andifunse, kuwazungulitsa mafunsowo basi mwanjira imene iwo amafuna kuti achitire, ndi kuwauza iwo maloto awo ndi matanthauzo iwo asanandiuze konse ine.

55 Tsopano, anthuwo ali mchipinda muno, uko. Ndipo ine ndimangopitirira ndi kuwalola iwo kuti ayankhule. Iwo amati, "Chabwino, M'bale Branham, ine ndinadzera *chakuti-ndi-chakuti*."

56 Ine ndimati, "Tsopano, kumbukirani, ife tasonkhana muno osati kuti tikhale ndi chiyanjano. Ife sitinabwere muno kuti tidzayanjane wina ndi mzake. Muli funso mmalingaliro mwanu, mu mtima mwanu, limene—limene munapunthwamo ndipo simukudziwa chimene ilo liri. Ndipo mwinamwake ine ndikhala wokhoza, mwa kuthandizidwa ndi Mulungu, kuti ndichite zimenezo."

57 Ine ndinati, "Kumbukirani, mfumukazi ya Kummwera inali ndi mafunso ena, nayonso, pamene iye anabwera kwa Solomoni. Ndipo Baibulo linati panalibe kalikonse kanaululidwa kapena kanabisidwa kamene Solomoni sakanakhoza kuyankha." Ndipo ine ndinati, "Wamkulu kuposa Solomoni ali pano. Mukuona? Ndiko kulondola. Ambuye Yesu analonjeza, 'Paliponse pamene awiri kapena atatu adzasonkhana mu Dzina Langa, pamenepo Ine ndidzakhala pakati pawo. Ndipo chinthu chirichonse chimene iwo angakhoze kuchiganizira, kapena kuchikhumba, ndipo—ndipo akadzapempha, icho chidzapatsidwa kwa iwo.' Ndipo tsopano funso lanu ndi chinachake chimene inu simukuchidziwa, chinachake chimene simukudziwa momwe mungachiyandikirire, chinachake chimene inu simukudziwa momwe mungachitire nacho."

58 Ndipo ine ndinati, "Kachiwiri, Lemba linanena izi, kuti, 'Angelo a Mulungu amazungulira pa iwo amene amamuwopa Iye,' chotero mdziko lina kumene zokhudzira faivi sizimatha kufotokozera."

59 Zokhudzira faivi zimakhudza dziko lino lokha. Ngati mukanati musakhale ndi kumverera, inu simukanati muzimverera kalikonse. Kumverera sikukanati kukhale kanthu kwa inu; limenelo likanakhala liri dziko lina. Ngati mukanati musakhale mulibe kupenya, chimene mukuyang'anapocho chikanakhala chiri dziko lina, inu simukudziwa kanthu za limenelo. Chotero mphamvu faivi izi ndizo chinthu chokhacho chimene Mulungu anatilola ife kuti tizimasukirako.

60 Tsopano pali china chotchedwa chikhulupiriro. Koma ndi chikhulupiriro inu mumayenda chokwera makwerero, ndipo potsiriza inu mukhoza kukafika pamwamba kwambiri mpaka inu nkubowoleza kukalowa mdziko lina, limene liri masomphenya. Pamenepo inu mukhoza kumapenya.

61 Chimodzimodzi basi ngati inu mukanati musamadziwe konse chimene ichi chinali chimene inu munali kuchimverera ndi chokhudzira chanu cha kumvererera, simunayambe mwachiwonapo icho; ndiye maso anu nkutseguka, inu mukanakhoza kumachiwona icho. Icho chikanakhala chonsecho chinsinsi kwa munthu ameneyo yemwe sangakhoze konse kuchiwona. Icho chingakhale chinsinsi kwa iye, komabe ndi zimenezo.

62 Ndipo mmenemo, Ambuye. . .Ife tisanafike kuno, kwa anthu ochokera kudutsa dzikoli, konsekonse, ochokera kumpoto, kummwera, kumadzulo, kubwera kuno kudzafuna zoyankhulana izi. Ndipo mwamsanga iwo akatsiriza kuyankhula, ndendende basi mafunso amene iwo akanati afunse, chinthu chimene iwo akanati achifunse, ine ndimati, "Yang'anani apa," nkusudzumirapo, ndipo pamenepo pamakhala kachidutswa ka pepala kali ndi funso lirilonse, ndi kuzungulira ndendende basi momwe iwo akanafunsira iwo, momwe akanati afunsire iwo, yankho lawo liri pansi apa kwa funsolo, chimodzimodzi basi momwe ilo linayankhidwira. Ambuye ndi wamkulu. Iye amadziwa zinthu zonse. Koma, apobe, zinanditengera ine pafupifupi masiku atatu kuti nditulukemo madzulo amenewo, chimene izo zinali, kung'ambika koteroko. Ndipo tsopano ine ndimaganiza zoti ndidzazitenge izo, chonchobe, ife tisanachokepo.

63 Ndipo ilipo njira yoyenera, njira yeniyeni yake, kwa munthu aliyense. Tsopano, ziripo zinthu zimene zingakhoze kunenedwa.

64 Ndipo ngati anthuwo ali pano, amene akudziwa zinsinsi za mmitima zimene zinaululidwa, izo zingakhale mwamtheradi . . . Izo zingakhale zowopsya; izo zingakhoze kuyambitsa mulandu, izo zingampangitse wina kumuwombera mzake, kapena

chinachake, ngati izo zitawululidwa pomwe pano pa nsanja monga chonchi, pa gulu, pamaso pa gulu. Izo zingayambitse milandu yokakhala mndende, ndi china chirichonse, chimene chingati . . .

65 Koma pamene inu mukhala limodzi monga chomwecho, Mzimu Woyera, awiri okha a inu limodzi. Koma ife timamvetsa izi, kuti zimene iwo amandifunsa ine zimakhala za mseri. Ine sindimanena kanthu za zimenezo. Ndipo zimene ine ndimanena kwa iwo, zimakhala kwa iwowo kaya iwo afuna kuti anene izo kapena ayi. Mukuona? Koma izo zimakhala zakuti zidziwike pakati pa ife, mzoyankhulanazo. Zimakhala kumutenga munthuyo, mmodzi pa nthawi, ndi kukhala pamenepo mpaka chirichonse chitakhazikitsidwa kwathunthu, mwaona, Mzimu Woyera.

66 Ndiyeno kuganizira za chisomo, Mzimu Woyera kumandiuza ine zonse za zimenezo, kwa mmodzi aliyense, mzere wonsewo wa iwo, iwo asanafike konse kuno; kudutsa dzikoli, akubwera, anthu amene ine sindinayambe ndawawonapo mmoyo. Ndi kuzilemba izo pamenepo kuti iwo adzakhoze kudziwa, basi mondondozana molingana ndi momwe mafunsowo akanadzakhalira, nkuwayankha iwo.

67 M'bale wina anali ndi mafunso pa mbewu ya serpenti, amene ine sindinathe kuwayankha molondoloza basi, chifukwa theka la ora lawo linali litatha. Ine ndikuyembekeza kuti iye anazimvetsa izo bwino bwino, mayankho a izo, pa pepala. Ine . . . Iye anali atawalemba iwo, ndipo iye sanapeze mayankho ake onse, chotero ine ndinangomupatsa iye zolembazo nkumubwezera, mayankhowo pa pepalapo. Ngati iye alibe, Billy Paul ali nawo iwo. Ine ndikudziwa bamboyo ali muno; ine ndinangoyang'ana pa iye mphindi zingapo zapitazo. Chotero ngati iye—ngati iye akufuna kuti apeze izo, izo zalembedwa pa chidutswa cha pepala, mayankho anu kwa funso lanu.

68 Tsopano, oh, momwe Ambuye aliri wabwino! Ine ndikuyembekeza aliyense akumverera bwino. Uh-huh.

69 Ndipo tsopano tiyeni ife tikumbukire, ndipo tsopano pamene ine ndikupempherera mipango iyi, kuti timukumbukire M'bale Dauch. Iye ndi m'bale wofunikira, ndipo ife tikufuna kuti timukumbukire iye mu pemphero.

70 Ndipo ine—ine ndikumuwona M'bale Ungren, koma ine—ine sindikukhoza kumuwona Mlongo Ungren paliponse, kaya iye ali bwino tsopano. Inde, wakhala cha kumanja kwa iye komwe. Zedi. Eya. Ndine wokondwa. Chifukwa ife tinaitanidwa usiku wina, mu . . . basi vuto la msanga la iye ndi mwana wake wamkazi, Mlongo . . . Ine . . . Downing, Downing. Inathamanga nkusiya msewu, ndipo basi chisomo cha Mulungu, kapena awiri onsewo akanaphwanyidwa mzidutswa apo pomwe. Ndipo

apa iwo abwera mpaka ku tchalitchi, anakwera sitima ndi kumabwera.

71 Ine sindidzakuiwalani nkomwe inu nonse. Ine ndimakukondani inu. Mulungu akudziwa zimenezo. Ine—ine ndimakukondani inu. Momwe, kudutsa mdzikoli, kudutsa mu nyengo yoterera!

72 Pamene ine ndiyang'ana pa abale ena pano ochokera ku Georgia, ndi Alabama, ndi malo osiyanasiyana, ndi Tennessee, ndi kozungulira, kumene iwo amakwera galimoto yawo chotsika mu msewu, kumene chisanu, kumaterereka, ndipo mmbuyo ndi mtsogolo monga chomwecho, kuti abwere kuno ku msonkhano umodzi.

73 Pamene ndinaitanidwa mwadzidzidzi kwa M'bale Dauch tsiku lina, ine sindimadziwa kuti Lima, Ohio, anali kutali kwambiri. Basi. . .ine ndinkaganiza iko kunali kulumpha pang'ono, kungolumpha, ndi kulumpha. Koma, mai, ine ndinachoka kuno molawirira kwenikweni mmawa umenewo, sindinakafike uko mpaka wani koloko madzulo amenewo, kuyendetsa mulimonse—chirichonse chimene malire a liwiro akanaloleza, ndipo pa msewu waukulu wapawiri. Ndipo ine ndimaganiza momwe uko kuliri koyandikira, kupita mpaka Kummwera kumene anthu ena awa amachokerako, kutali uko Kumpoto ndi Kumadzulo, kumene iwo amachokerako.

74 Ine ndimakukondani inu, ndipo ndi chifukwa chake ine ndimayesetsa kuti ndikhale woonamtima kwenikweni pano.

75 Ndipo anthawi-zakale! Ine ndikumuwona M'bale Creech ndi iwo akhala kumbuyo uko tsopano, ndi iwo amene akhala ali ndi ine zaka zonse izi ndi zinthu, ndi momwe ife tabwerera limodzi. Ine ndinali kuyang'ana pa chithunzi cha Mary Jo, ine ndikukhulupirira awo anali mausiku angapo apitawo. Kanthu kakang'ono kwambiri basi pamene ife tinakomana koyamba, ndipo tsopano iye ndi wokwatiwa, ine ndikuganiza, ndipo ali ndi ana. M'bale Creech ndi Mlongo Creech, aang'ono, atsitsilakuda, ndipo Meda ndi ine, ndipo pano ife tiri ndi imvi ndi mapewa okugwa. Mwaona, pamakhala chinachake cha anthu monga amenewo, chimene—chimene chimakugwira iwe. Mwaona, iwe—iwe—iwe umafuna kuti uzikhala ndi iwowo. Mukuona? Pamakhala chinachake chimzake chimene—chimene nthawizonse chimapangitsa malingaliro ako kukokera mmbuyo. Kungowaperekera ngati chitsanzo kwa ena amene ali pano. Aang'ono ndi aakulu, ife tikuyembekezera ku Kudza kwa Ambuye.

76 Chotero mmawa uno ine ndaziyika izo. . .Mulungu, ine ndikukhulupira, waziyika izo mu mtima mwanga kuti ndiphunzitse phunziro la Sande sukulu kuno mmawa uno, Mulungu akalola, kwa nthawi yotalikirapo. Ine. . .Ndipo

tsopano, uno pokhala msonkhano wanga wotsiriza kwa kanthawi pang'ono, monga momwe ine ndikudziwira, a . . .

77 Ndipo ine ndikufuna kuti inu muzikumbukira kuti M'bale Neville pano, amasiyidwa pa mpingo, kuti aziyang'anira kachisi uyu, pansi pa Mzimu Woyera, kuti iye amasiyidwa pano, ndipo iye amawukhulupirira Uthenga uwu ndipo—ndipo amawuphunzitsa Iwo chimodzimodzi basi monga ine ndimachitira. Kulondola. Ndipo nthawi iliyonse imene inu mungafune kutero, inu mungakhoze kuchiwona choyenera kuti mubwere kudzamumvera M'bale Neville, iye ndithudi angakuchitireni inu ubwino, ine ndikutsimikiza. Iye ndi wantchito wopambana wa Yesu Khristu.

78 Ine ndamudziwa Orman Neville chiyambireni ine ndiri mnyamata wamng'ono, ndipo iye sanasinthe chidutswa chimodzi, kupatula kuti wangoyandikirapo kwa Mulungu. Ine ndikukumbukira pamene ine ndinamuwona iye koyamba pa . . . ine ndinaitanidwira ku nsanja yake ya Methodisti. Ndipo pamene ine ndinabwerera kuno ku Kachisi, ine ndinati, "Tsiku lina, ine ndidzamubatiza iye mu Dzina la Yesu Khristu." Ndipo ndi uyu pano ali ndi Uthenga tsopano, akupitirira, wantchito weniweni wochirimika.

79 Ndipo M'bale Neville amadutsa mu zopsyinja zambiri ndi zopweteketsa mtima, zimene iye samazisonyeza izo pano pa Kachisi. Koma pokhala kuti Ambuye amandirola ine kukhala ndi kupenya pang'ono mu miyoyo ya anthu, ine ndimadziwa zimene iye amadutsamo; zochuluka zonse za izo, mwaona. Ndipo iye ndithudi amapita pansi pa kuvutika kochuluka ndi kupsyinjika, ndi zinthu. Ndipo inu, anthu inuyo pano, muzimugwirizira iye monga Yoswa ndi Kalebu ankagwirizira mmwamba manja a Mose, pamene iye akubweretsa Mawu.

80 Zikondananani wina ndi mzake, pamwamba pa chirichonse. Zikondananani wina ndi mzake. Musati . . . Ziribe kanthu zimene mdierekezi aziyesetsa kuti anene! Tsopano ndinu nonse gulu limodzi lokoma lalikulu kwambiri tsopano, koma kumbukirani chenjezo langa, mwaona, Satana salola kuti izo zizikhala mwanjira imeneyo. Ayi, bwana. Iye adzawombera chirichonse, ngati iye angati amubweretse wina muno kuti amupange akhale chandamale chake. Iye adzabweretsa wotsutsa wina kapena wosakhulupirira umo, ndi kudzamukhazika iye pansi, ndi kumupangitsa iye kuti aziyanjana ndi inu mwakachetechete ndi zinthu, ndipo kenako nkudzamubayira munthu ameneyo ndi mtundu wina wa chiphe, ndipo iye adzayamba kudutsa mu mpingo ndi zimenezo. Inu musadzatenge mbali ndi zimenezo. Inu musadzakhale ndi chinthu chochita ndi china chirichonsecho. Inu mudzakhalebe okondana ndi okoma ndi achifundo kwa wina ndi mzake. Mudzamupempherere mwamuna ameneyo, kuti iye adzapulumutsidwe nayenso, kapena mkazi ameneyo, kapena yense yemwe iye ali,

mudzangowapempherera iwo. Ndi kudzamamatirana wina ndi mzake.

81 Ndipo zikhalani ndi m'busa wanu. Mwaona, iye ndi m'busa, ndipo muzimpatsa iye ulemu. Iye adzakutsogolerani nakudutsitsani inu, ndipo, chifukwa iye anadzozedwa ndi Mulungu kuti azichita chomwecho.

82 Tsopano kodi inu mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mdani adzabwera. Ndipo pamene iye adzatero, mudzangomamatirana mothinana limodzi chomwecho. Ndipo yemwe mdierekezi akumugwiritsa ntchitoyo ngati mdani mwina adzatuluka panja kapena adzabwera mkati ndi kudzakhala mmodzi wa inu. Ndizo zonse.

83 Musadzapange konse timagulu ta mtundu pakati panu. . . kapena—kapena kumayankhula, kudzipanga nokha mwakamtundu. Ife ndife amodzi. Ine sindinganene kuti, "Dzanja lamanzere, ine—ine ndakulusira iwe, ine ndikuchotsapo iwe chifukwa iwe sindiwe dzanja lamanja." Iye ndi dzanja langa lamanzere. Ine ndikufuna iye kuti azikhala pamenepo. Ngakhale nsonga yaing'ono ya chala changa, ine ndikufuna kuti izikhala pomwepo, gawo laling'ono lirilonse la thupi langa lizikhala pomwepo. Ndipo Mulungu amafuna ife, monga thupi la okhulupirira, kuti tizikhala ndendende wina ndi mzake, mogwirizana wina ndi mzake.

84 Ndipo tsopano inu muli nawo matepi a zimenezo. Inu muli nawo matepi pa zimene ife timakhulupirira. Inu muli nawo matepi pa khalidwe la mpingo, momwe tingamadzikhalitsire tokha mu mpingo wa Mulungu, momwe ife tiyenera kumabwerera muno limodzi ndi kukhala limodzi mmalo Ammwambamwamba. Musamakhale kunyumba. Ngati Mulungu ali mu mtima mwanu, inu simungakhoze konse kudikirira kuti zitseko zimenezo zitsegulidwe uko, kuti mudzalowe muno kudzayanjana ndi abale anu. Ngati simukutero—simukumverera mwanjira imeneyo, ndiye ine ndikuuzani inu, ndi nthawi yoti muyenera kumapemphera.

85 Chifukwa, ife tiri mmasiku otsiriza, pamene Baibulo linatikweza, kapena, linatilimbikitsa ife kuti—kuti, "Mochuluka kwambiri pamene ife tidzawona tsiku limenelo likuyandikira," kuti tidzakondane wina ndi mzake ndi chikondi cha Chikhristu ndi chikondi Chaumulungu, "kuti tidzazisonkhanitse tokha pamodzi mmalo Ammwambamwamba ndi—ndi—ndi Khristu Yesu," ndi kukondana wina ndi mzake. "Potere anthu onse adzadziwa kuti inu ndinu ophunzira Anga, pamene inu mudzakhala ndi chikondi wina kwa mzake." Ndiko kulondola. Kumakhala kumene limodzi.

86 Ngati m'bale, inu mukuganiza kuti iye akulakwitsa pang'ono, kapena mlongo, mudzanene kuti, "Ambuye, musadzandirole konse ine ndidzakhale ndi muzu wa kuyipidwa

ukutumphukira mmwamba, chifukwa iwo—iwo umukhudza iye, ndipo iwo udzamuchotsa Khristu kumuchotsa mmoyo wanga." Chiphe cha asidi chija cha kuipamtima, ndi nsanje, ndi udani, zimene ziti zidzangowuchotsa Mzimu Woyera pomwepo kuchokera mwa inu. Izo zidzamuthamangitsa Iye kumuchotsa pa kachisi pano. Izo zidzapha Mzimu wa Mulungu, kapena kuwuthamangitsa Iwo kuwuchotsa pano, kumupweteka m'busa wanu. Izo zidzachita chirichonse. Mukuona? Inu musadzachite zimenezo.

87 Inu mudzangomamatirana moyandikirana pamodzi kwambiri. Mudzakokere. . .Mudzatenge lamba, monga m'bale anachitira umboni, mtumiki pano usiku wina, zakukhala ndi lamba, anaziwona izo mmasomphenya. Basi, amene amamangira pa zida zonse za Mulungu. Kudzangomukokera iye, mothinitsa chokweza, kudzasunthira moyandikira kwa wina ndi mzake. Kukondana wina ndi mzake, mulimonse. Kuyankhula zabwino za wina ndi mzake, kunena zinthu zabwino za wina ndi mzake, ndipo mukadzatero Mulungu adzakudalitsani inu.

88 Tsopano mmawa uno, Ambuye akalola, mwa thandizo Lake ndi chisomo, ine ndiri nawo ndithu mulu wa mafunso pano, wa Malemba, kani. Ndipo tsopano ife tisanawayandikire Iwo . . . Ine ndikuganiza ine ndinawamva marekoda akuyatsidwa umo. Ife tikuti tibweretse Uthenga tsopano, mwa chisomo cha Mulungu.

Choyamba, mawu a pemphero.

89 Ambuye Yesu, kuyankhula kwa thupi ili la Mpingo, kuti iwo ayenera kugwirana limodzi ndi dzanja losasintha la Mulungu, mtheradi wawo, Mawu; kuwachenjeza iwo, monga Paulo anachenjezera gulu lake, kuti, "kudzakhala mimbulu idzalowe mmenemo." Ndinu Mulungu yemweyo lero monga Inu munali nthawi imeneyo, ndipo mdani ameneyo ali yemweyo. Mulole chiyanjano ichi ndi zimango za chikondi nthawizonse zizikhalapo pakati pa anthu awa, mwa Khristu Yesu.

90 Tithandizeni, mmawa uno, Ambuye, pamene ife tikuwerenga Mawu. Mulole Mzimu Woyera uwaululire Iwo kwa ife, kuti Mpingo ukhoze kukhala wokhazikitsidwa kwathunthu mu "Chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera mtima," kuti chiwagwire iwo. Ndipo mulole, monga Inu munaperekera masomphenya zaka zina ziwiri zapitazo, "kuti ndisunge Chakudya," chabwino, masamba owoneka-mwathanzi amene ine ndinawawona mmasomphenya, chikusungidwa mu kachisi muno, mulole ife lero tilandire mbiya yonse yodzaza ndi Icho (Perekani izi, Ambuye.), Kapena, yodzadza ndi tepi: kuti Icho chikakhoze kuwulula Yesu Khristu kwa ife mu ora limene ife tiri kukhalamo, kuti chitipatse ife mphamvu zotisunga, mphamvu zauzimu ku ntchito imene ili mtsogolomu. Perekani izi, Atate.

91 Adalitseni awa, ana Anu. Iwo ali muno mmawa muno kuchokera ku mbali zambiri zosiyanasiyana za fukoli. Mmawa wotentha, womata, komabe ife tikumverera Kukhalapo kwa Mzimu Woyera, mu zonse izi.

92 Ife tikuganiza za John Wesley, ndi Calvin, ndi Sankey, ndi Knox, Finney, ndi ochuluka a iwo, ngakhale popanda chokupizira mphepo chamagetsi, kumene anthu ankakhala mu maholo, ndipo thukuta likuyenderera pansi pa nkhope zawo. Akazi, atadziphimba bwino ndipo atavala, ankakhala mwa omvetsera ndipo akuchita thukuta mpaka zovala zawo kumanyowa khwelephethe, akumvetsera ku Mawu a Mulungu, kumadyetsa miyoyo yawo. Tsopano, ife tikumverera, Ambuye, kuti iwo ali pa mpumulo kwinakwake uko, akuyembekezera Kudza kwa Ambuye.

93 Tisungeni ife limodzi, Atate. Mulole Mzimu Woyera uzititsogolera ife ndi kutilondolera ife. Mutipatse ife moyo wautali wa utumiki kwa Inu. Mutipatse ife Uthenga wopambana uwu mmawa uno umene ife tiri kuwuyembekezera kuchokera m'Mawu Anu, kuti Iwo ukhoze kupita ku mtima uliwonse. Mupange milomo imene iyankhule, Ambuye, iyankhule Choonadi. Muwupange mtima umene utamvetsere ukhale wachonde kuti ulandire Choonadi, ndipo mulole Icho chikule nkukhala mitengo yaikulu ya Moyo Wamuyaya, kuti zidzakhale nyali zowala ndi akalata owerengedwa ndi anthu onse; iwo akhoze kudziwa kuti Yesu Khristu waukitsidwa kwa akufa ndipo akukhala moyo pakati pathu. Tipangeni ife odzaza kwambiri ndi chikondi ndi chipatso cha Mzimu mpaka amuna ena ndi akazi, anyamata ndi atsikana adzakhoze kumawona zotsatira za Moyo wa Khristu ukukhalabe moyo mwa ife, zitatha zaka thuu sauzande kuchokera ku chochitika chachikulucho. Perekani izi, Atate, kuti zilemekeze Inu. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

94 Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge zina kuchokera Mmalemba. Ndipo ine ndikudalira tsopano kuti inu mwatenga mapensulo anu ndi mapepala, ndi chirichonse, mwakonzeka.

95 Ndipo, M'bale Neville, inu mwangokhala duu. Ine ndingochotsa chikhotho changa. Ndizo. . . [M'bale Neville akuti, "Ziri bwino bwino. Ameni."—Mkonzi]. Ndizo. . . Mundikhululukire ine chifukwa chochotsa chikhotho changa koma uku—kukutentha mowonjeza kuntunda kuno.

96 Tsopano ine ndikufuna kuti inu mutembenuzire ku Bukhu la Akolose, mutu wa 1 wa Akolose. Ndiyeno pamene ife tikuwerenga izi, kuyambira ndi. . . Ine ndikufuna inu, mukapita kwanu, mukawerenge mutu wonsewo wa Akolose uwu. Koma ndikufuna kuti inu muwerenge mmawa uno, ndi ine, kuyambira pa ndime ya 15, ya 29, kuphatikiza.

97 Ndipo tsopano mungokhala opirira monga inu mungathere, pakuti ine ndikumverera kuti mu izi apa, ngati Mulungu ati andithandize ine, ziwulula ndi kubweretsa mmalingaliro mwanu zinthu zina zonse izi zimene ine ndazikambapo monse kudutsa mmasiku a pa kachisi; chifukwa chimene ine ndanena zimene ine ndanena, ndi chifukwa chimene ine ndachita zimene ine ndachita. Ichi ndi chifukwa chake.

98 Tsopano kuyambira ndime ya 15.

*Yemwe ali fanizo la Mulungu wosawonekayo, woyamba kubadwa wa cholengedwa chirichonse:*

*Pakuti mwa iye zinthu zonse zinalengedwa, zimene ziri mmwamba, ndi zimene ziri mu dziko lapansi, zowoneka...zosawoneka, kaya izo zikhala ziri mipando yachifumu,...maufumu,...maukulu,... mphamvu: zinthu zonse zinalengedwa ndi iye, ndi kwa iye:*

*Ndipo iye ali woyamba wa zinthu zonse, ndipo mwa iye zonse zigwirizana.*

*Ndipo iye ali mutu wa thupi, mpingo: yemwe ali chiyambi, woyamba kubadwa kwa akufa; kuti mu zinthu zonse iye akhoze kukhala nawo* uyambiriro.

*Pakuti icho chinamkondweretsa Atate kuti mwa iye mukhoze* kukhala *chidzalo chonse chikukhalamo—mukhoze chidzalo chonse kukhalamo;*

99 Mundirole ndiyike kutsimikizira pang'ono pa zimenezo kachiwiri, ndime ya 19 iyi.

*Pakuti icho chinamkondweretsa Atate kuti mwa iye mukhoze kukhala chidzalo chonse;*

*Ndipo, atapanga mtendere kupyolera mmagazi a mtanda wake, mwa iye kuti akayanjanitse zinthu zonse kwa iyemwini; mwa iye, ine ndikuti, kaya izo zikhale zinthu mdziko lapansi, kapena zinthu kummwamba.*

Muwone kumene chiyanjanitsocho chinapita.

*Ndipo inu, amene munali* nthawiyina *ngati alendo ndi adani mmalingaliro anu mwa ntchito zoipa,* inu *tsopano iye* wakuyanjanitsani

*Mu thupi la mnofu wake kupyolera mu imfa, kuti akakuperekeni inu oyera...opanda chilema...* otsimikizika *pamaso pake:*

*Ngati* inu *mupitirira mu chikhulupiriro ozikika ndi okhazikika, ndipo* osakhala *muli kusunthidwira kutali ndi chiyembekezo cha uthenga, umene inu mwawumva, ndi umene unalalikidwa kwa cholengedwa chirichonse chimene chiri pansi pa kumwamba; umene ine Paulo ndapangidwa mtumiki wake;*

*Yemwe tsopano ndikukondwera mu zowawa zanga chifukwa cha inu, ndi kudzazitsa icho chimene chiri* chomangidwa*. . .kuseri kwa* kutunduzidwa *kwa Khristu mu. . .thupi chifukwa cha thupi lake, limene liri mpingo:*

*Kwa lomwe ine ndapangidwa mtumiki, malingana ndi nyengo ya Mulungu imene yapatsidwa kwa ine chifukwa cha inu, kuti mukwaniritse mawu a Mulungu;*

*Ngakhale chinsinsi chimene chakhala chiri* chobisika *kuchokera ku* m'badwo *ndi kuchokera ku timibadwo, koma tsopano chapangidwa chiwonetseredwe kwa oyera ake:*

100 Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge ndime imeneyo kachiwiri.

*Ngakhale chinsinsi chimene chakhala chiri chobisika kuchokera ku mibadwo ndi kuchokera ku timibadwo, koma tsopano chapangidwa chiwonetseredwe kwa oyera ake:*

*Kwa omwe Mulungu akanati adzawapangitse kudziwa chimene chiri kulemera kwa ulemelero wa chinsinsi ichi pakati pa Amitundu; amene ali Khristu mwa inu, chiyembekezo cha ulemelero:*

*Yemwe ife tikumulalikira, kuchenjeza munthu aliyense, ndi kuphunzitsa munthu aliyense mwa chidziwitso chonse; kuti ife* tikhoze *kumupereka munthu aliyense wangwiro mwa Khristu Yesu:*

*Kwa chomwe inenso ndikugwiritsa ntchito, kulimbikira molingana ndi kuchita, kumene kukuchita mwa ine mwamphamvu.*

101 Tsopano kwa mutu ine ndikufuna kuti nditenge kuchokera pamenepo, uwu ngati mutu, kukhazikitsira iwo pa Baibulo lonse, koma ine ndikufuna ife tiwutche uwu: *Khristu Ndi Chinsinsi Cha Mulungu Woululidwa*. Khristu kukhala chinsinsi cha Mulungu woululidwa! Tsopano, ine ndawutenga iwo mwa phunziro la Sande sukulu, kuchitira kuti ife tonse tikhoze kuwerenga limodzi ndi—ndi kukhala ndi chiyanjano ichi limodzi.

102 Tsopano, chinsinsi cha Mulungu chobisika, Iye anali nacho dziko lisanayambe. Tsopano, mmbuyo ku nkhongo kwa malingaliro a Mulungu, kunali chinachake chimene Iye anali kuyesetsa ndipo anali woti achikwaniritse, ndipo Iye anali nacho cholinga pa kuchita izo, polinga kuti Iye adzadzifotokoze Yekha. Chifukwa, choyamba, kunalibe nkomwe mwezi, nyenyezi, atomu, molekyulu, kapena chirichonse. Iye anali Mulungu. Koma kwenikweni Iye sanali Mulungu pa nthawi imeneyo, chifukwa *Mulungu* ndi "chinthu chopembedzedwa," ndipo kunalibe kanthu koti kazimupembedza Iye.

103 Chotero, mmalingaliro Ake aakulu, Iye ankafuna zikhumbo izi kuti zidzafotokozeredwe. Ndipo mwa Iye munali chikondi; mwa Iye munali kuti adzakhale Atate; mwa Iye munali kuti adzakhale Mwana; mwa Iye munali kuti adzakhale Mpulumutsi; mwa Iye munali kuti adzakhale Mchiritsi. Ndi zikhumbo zonse zazikulu izi zimene ife tikuziwona zikuwonetseredwa kale, izo zinali mwa Mulungu.

104 Chotero, lingaliro langa, chinthu choyambirira chimene Iye anachipanga chinali Angelo. Ndipo zitatero iwo ankamupembedza Iye, ndipo icho chinamupanga Iye "Mulungu." Ndipo Iye anayambira pamenepo. Monga mu Mauthenga ammbuyomu ine ndayesetsa kuti ndizifotokoze zimenezo, kuziswa izo motsika. Ndipo tsopano, ndiye, pamene Angelo anayamba kumupembedza Iye, apo panali nkuti pasanakhale ngakhale molekyulu pa dziko lapansi. Panalibe kanthu kena. Paliponsepo panali mdima. Panalibe dzuwa, panalibe mwezi, panalibe nyenyezi, panalibe kalikonse, ndiye Iye anali Mulungu. Monga Iye anamufunsa Yobu, "Unali kuti iwe pamene ine ndinkaika maziko a dziko lapansi, mwaona, pamene nyenyezi zammawa zinkaimba limodzi, ana a Mulungu ankafuula mwa chisangalalo? Mukuona? Tsopano, unali kuti iweyo?" Mukuona? Zimenezo zinali mmbuyo kutali lisanakhalepo dziko lapansi.

105 Tsopano, Mulungu anali ndi cholinga ndi chinsinsi chobisika. Ndipo ndizo zimene ine ndikufuna kuti ndiyankhulepo kwa Mpingo mmawa uno, chinsinsi chobisika cha Mulungu chimene Iye anali nacho mmalingaliro Ake dziko lapansi lisanayambe nkomwe, ndi momwe icho chadzadzifutukula chokha mpaka mmusi ku ora la pakali pano limene ife tiri nkukhalamoli. Mukuona? Ndiye inu mumvetsa bwinobwino pamenepo, inu muwona, pa, ine ndikukhulupira, chimene chiri kuchitika.

106 Chinsinsi chachikulu cha Mulungu, cha momwe, icho ndi chinsinsi. Iye anachisunga icho mwachinsinsi. Palibe munthu ankadziwa kanthu za icho. Ngakhale Angelo samamvetsa icho. Mwaona, Iye sanachiwulule icho. Ndi chifukwa chake, pansi pa chinsinsi chathu chachisanu ndi chiwiri, pamene Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri chinatsegulidwa, uko kunali chete. Yesu, pamene Iye anali padziko lapansi, iwo ankafuna kuti adziwe pamene Iye akanati adzabwere. Iye anati, "Siziri . . . Ngakhale Mwana Mwiniwake sakudziwa pamene izo ziti zidzachitikire." Mwaona, Mulungu ali nazo izi zonse kwa Iyemwini. Icho ndi chinsinsi. Ndipo ndi chifukwa kunali chete Kumwamba kwa danga la theka la ora, ndipo mabingu asanu ndi awiri anayankhula maliwu awo, ndipo Yohane mpaka analetsedwa kuti alembe izo, mwaona, Kudza kwa Ambuye. Ndicho chinthu chimodzi chimene Iye sanachiwulule panobe, za momwe Iye ati adzadzere, ndi pamene Iye ati adzadze. Ndi

chinthu chabwino kuti Iye sakutero. Ayi.

107 Iye wazisonyeza kapena waziwulula izo mu choyimira chirichonse chimene chiripo mu Baibulo. Chotero, Baibulo lonse ndiro vumbulutso la chinsinsi cha Mulungu mwa Khristu. Hum! Baibulo lonse ndiro kufotokoza kwa cholinga chimodzi chimene Mulungu anali nacho, cholinga chimodzi chimene Iye ankafuna kuti achikwaniritse mu Baibulo lonse. Ndipo zochita zonse za—za okhulupirira mu Baibulo zakhala ziri mwa choyimira, ndi kufotokozera chimene cholinga chachikulu cha Mulungu chiri, ndipo tsopano mu tsiku lotsiriza lino Iye wachiwulula icho ndipo akuchisonyeza icho. Ndi thandizo la Mulungu, ife tikuchiwona icho apa pomwe mmawa uno, chimene Ambuye wakhala ali nacho mmalingaliro Ake nthawi yonseyi, ndipo wachifotokoza icho.

108 Chotero, inu mukhoza kuwona tanthauzo lalikulu la chimene chakhala chiri kuti tidziwe ichi, ndipo kenako nkuyesera kuti tichibweretse icho kwa anthu. Mukuona? Ndiyeno iwe sungati . . . Ine sindinapite mwatsatanetsatane kuti ndiyesere kuchifotokoza Icho monga Mulungu wachiwululira icho kwa ine.

109 Tsopano, ngati inu mukufuna kuti muzilembe izi pamenepo. Ine ndiri nawo malo ochuluka kwambiri amene ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokerapo. Ndipo tsopano mu—mu Bukhu la Luka Woyera, mutu wa 24 wa Luka Woyera, ife tikupeza kuti ndi . . . Ndi awiri a ophunzira ali pa njira yaku Emmau. Ndipo Yesu anatulukira, chitachitika chiwukitsiro Chake, ndipo iwo anali pa yawo—njira yawo waku Emmau, akupita chotsatira njira, akuganiza ndi kumayankhula, ndipo akulira, pa nkhani ya Yake—imfa Yake, ndi momwe iwo anamuwonera Iye akuzunzika pa chimene iwo ankaganiza kuti sichinali choyenera nkomwe; iwo anamutenga Ambuye wawo ndipo anamupachika Iye. Ndipo—ndipo iwo anali akupita motsatira pamenepo, akulira.

110 Ndipo Iye anatulukira kuchokera ku mbali ya msewu ndipo anayamba kuyankhula nawo iwo zokhudza Khristu. Iye anati, "Oh, opusa ndi ochedwa kumvetsa. Kodi inu simukudziwa kuti aneneri onse ndi Masalmo . . . " Mwaona, kodi Iye anali akuchita chiyani? Amazidzindikiritsa Yekha kwa ophunzira awa, kuti aneneri onse, ndi Masalmo onse, ndi chirichonse, zinali Iye, akufotokozedwa. Mukuona?

111 Ndipo tsopano chifukwa chimene ine sindinatenge kuti ndilalikire mmawa uno, chinali chifukwa, ine ndinaganiza, po kuphunzitsa, ife tikanati tizimvetse izo bwinoko kuposa kungotenga mutu ndi kulumpha pa izo. Ife tikufuna kuti tingophunzitsa izo.

112 Tsopano, Iye anali akunena kuti Masalmo onse ndi aneneri onse ankayankhula za Iye. Chabwino, mmenemo, chotero, izo zikusonyeza kuti zonse za Chipangano Chakale, zonse

za Chipangano Chatsopano, ndi zonse za Masalmo, kuyimba, nyimbo zimene zinali kuimbidwa, zinkaimbidwa za Iye.

113 Mutenge Salmo la 22, ndipo muliyimbe ilo, ndi kulifanizitsa ilo ndi mmawa wa kupachikidwa. Mukuona, "Mulungu Wanga, Mulungu Wanga, ndi chifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine? Mafupa Anga onse, iwo akuwonekera pa Ine. Iwo alasa mapazi Anga ndi manja Anga." Komabe, zinthu zonse izo pamenepo, iwo akuimba Salmo limenelo kumusi uko mu kachisi, ndi kumupachika wofunikira Yemweyo. Mukuona? Mwaona, atsogoleri aakulu a chipembedzo amenewo, anthu aakulu amenewo, aphunzitsi aakulu amenewo, ndipo komabe anachititsidwa khungu kwambiri, amene anali kuwawerenga aneneri ndipo anali akumaziimba nyimbozo, ndi kumachita mulandu umene iwo amati iwo akanati adzauchite.

Chinthu chomwecho chikuchitika mmawa uno!

114 Tsopano mvetserani mwatcheru, chifukwa. . . Tsopano ine sindipereka nkomwe tcheru chirichonse ku zomwe wotchiyo izinena. Ine ndikufuna inu kuti muzimvetse izi. Mukuona? Ine ndikufuna inu, mumvetse zimenezo. Mukuona? [Osonkhana akusangalala, ati, "Ameni."—Mkonzi].

115 Chotero inu mukhoza kuwona pano, mwamaziko, pa chiyambi, ganizo lomwe limene Mulungu anali nalo mmalingaliro Ake, Iye analibisa ilo kwa masikolala onse amenewo. Ndipo. . . Chiwerengero chokha, chiwerengero chosankhidwa chokonzedweratu, anthu okonzedweratu, anali okhawo amene anazimva izo. Ndipo tsopano mufufuze mmbuyo Lembalo chotsika kudutsa m'badwo wa aneneri, ndipo muwone ngati icho sichinali chinthu chomwecho. Mukuona?

116 Tsopano, ndipo Yesu apa akuwalozera iwo kwa aneneri ndi Masalmo, Iye anati iwo onse ankayankhula za Iye. Mukuona? Ndipo apa aphunzitsi Achiyuda awa, marabi, madokotala a lamulo, maprofesa, anali atachita ndendende monga iwo anali atachita mbuyomo.

117 Tsopano zindikirani, kachiwiri, Iye anati, "Fufuzani Malemba, pakuti Iwo ali Amene akuchitira umboni za Ine." Fufuzani Malemba, Malemba, Malemba onsewo. Kodi ine ndikuyesetsa kuchita chiyani? Kuti ndikusonyezeni inu kuti Baibulo ili ndiro chinthu chomwe chiri cholondola.

118 Tsiku lina, nditaima mchipinda cha chipatala, ndikuyankhula, mlongo anali atandifunsa ine kuti ndifotokoze za zipembedzo, chifukwa chimene ife tinali—timatsutsana ndi zipembedzo, ndi anthu ena achipembedzo.

119 Inu mukuona, izo ziyenera kubwerera ku Mawu, chifukwa Mawu ndiwo Mulungu. Mukuona? Ndipo Yesu akulongosola chomwecho apa, kuti Mawu ndiwo Iye. Inu simungakhoze kulipanga Lemba kudzitsutsa Lokha. "Pa chiyambi panali

Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo, Mawu, anapangidwa thupi!" Mukuona?

120 Tsopano apa Iye akuti, "Fufuzani Malemba, Iwo akuchitira umboni za Ine. Mwa Iwo inu mukuganiza kuti inu muli nawo Moyo Wamuyaya," ndipo izo nzoona, "ndipo Iwo ndiwo amene akuchitira umboni za Ine. Ndipo ine ndikuchitira umboni za Iwo. Ndipo ngati Ine sindichita ntchito zomwe zinalonjezedwa kuti Ine ndikanazichita, ndiye musati mundimvere Ine. Koma ngati Ine ndikuchita ntchitozo, ndipo inu simungakhoze kundikhulupirira Ine, khulupirirani ntchitozo, chifukwa izo zikuchitira umboni kuti Iye ndi Mawu." Oh, izo zikuwoneka ngati sizingakhoze kukhala zomveka bwino kuposerapo. Mukuona? Chabwino. Tsopano, "Fufuzani Malemba." Iye anati Mose ndi malamulo onse, ndi zina zotero, ndi aneneri, ndi Masalmo, ankayankhula za Iye. Ndipo, kachiwiri, Iye anati Malemba amachitira umboni za Iye.

121 Iye ndi pachimake pa nkhani ya Baibulo lonse. Ngati mutawerenga Baibulo, ndipo nkusamuwona Khristu mu ndime iliyonse ya Ilo, mubwerere ndipo mukaliwerenge Ilo kachiwiri. Mukuona? Ngati inu simungakhoze kumuwona Khristu mu ndime iliyonse ya Baibulo, ndiye inu muliwerenge Ilo kachiwiri, chifukwa inu mwaphonya chinachake. Baibulo ndiro Khristu. Iye ndiye Mawu. Pamene inu muwerenga, "Pachiyambi Mulungu analenga," pamenepo ndi Khristu. Mukuona? Aliwonse… Kuchokera pamenepo, mpaka ku "Ameni" mu Chivumbulutso, ndi Mawu aliwonse akuchitira umboni za Yesu Khristu.

122 Ndi chifukwa chake mabuku owonjezera awa amene iwo amawatcha *Bukhu Lachiwiri la Daniele*, ndi—*Bukhu la Maccabees,* amawonjezera purigatorio ndi zinthu zonga zimenezo, mwaona, izo sizinayankhulidwe mu Lemba. Mukuona? Iwo samagwirizana ndi lonse la Ilo. Palibepo malo oti uyikepo purigatorio mmenemo. Mulibemo malo oti muyikepo kupembedzera kwa oyera, ndi zinthu. Mulibemo malo mmenemo a zimenezo. Mulibemo malo a chipembedzo. Mulibemo malo a—a tizikhulupiriro kunja kwa—kwa Baibulo. Mukuona? Chotero pamene inu muwona zinthu zimenezo, izo—izo sizimabwera nkomwe mu chithunzicho. Ndipo ndi chifukwa chake anthu awonjezera zimenezo, ndipo ali nato tawo—tawo—tizidutswa tawo tonse tolumikizidwa mosokonezeka. Mukuona? Iwo akulephera kudziwa kuti ndi chiyani, "yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

123 Koma, ngati chinthucho chitayikidwa pamodzi molondola, pamenepo pakhala chithunzi chonse cha kugwa ndi kusinthika. Chithunzi chonse cha chirengedwe, ndi dongosolo lonse la Mulungu likuwululidwa molondola mwa Yesu Khristu. Ameni! Ndicho chithunzi chonse chitaikidwa pamodzi, popindika papang'ono paliponse ndi ngodya. Izo zangokhala ngati… Tsopano, ine sindikutanthauza kuti ndikhale wosinjirira ndi

izi, koma izo zimangokhala ngati kuika tizidutswa topanga chithunzicho pamodzi.

124 Ndi chifukwa chake tiri ndi zithunzi lero zimene zikuwoneka moyipa. Mukuti, "Ife ndife okhulupirira," ndipo ng'ombe ikudya udzu pamwamba pa mtengo. Izo sizimagwira ntchito. Ndi pamene iwo amati, "Eya, Iye ali njira iliyonse, koma basi motsimikiza...Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, zonse kupatula chinthu chinachake." Mukuona? Mukatero muwononga chithunzi chanu.

125 Baibulo linati Iye ali yemweyo! Yohane Woyera 5, kapena Yohane Woyera 14:12, Iye anati, "Iye," iye, aliyense, "iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iye adzazichita nayenso."

"Chabwino, izo zinali za m'badwo wina."

126 Pamenepo chithunzi chanu chalakwika kachiwiri. Inu muli ndi munthu akuwedza mchipululu, akufuna nsomba, pa mulu wa mchenga wotentha pamene palibepo nsomba. Mukuona? Mwaona, inu muyenera kumubweretsa iye mmbuyo kumene iye akuwedza, ku Galileya, kumene kuli nsomba zambiri, inu mukuona. Mukuona?

127 Inu—inu muyenera kuchipanga chithunzicho kuti chiwoneke molondola. Ndi chithunzi chachikulu cha Mulungu. Ndipo ilipo njira imodzi yokha yomwe mungati muchiwonere icho, ndi pamene inu mumuwona Yesu Khristu. Pamenepo pali Baibulo lonse. Iye ndi pachimake pa nkhani ya Baibulo.

128 Tsopano inu mukuzindikira kuti aliwonse a malo awa pano inu mukhoza kutengapo mutu, ndipo izo ndi zovuta basi kwa mlaliki kuti akhale chete. Iye amawoneka ngati iye amafuna kuti azipitiririrabe ndi izo, koma inu muyenera kuti mubwerere ku zomwe ife tiri kuphunzitsapo.

129 Iye ndi pachimake pa nkhani ya Baibulo. Iye anali mwa aneneri. Iye anali mu Masalmo. Iye anali mu mbiriyakale ya Baibulo. Baibulo ndi Bukhu la uneneri. Ilo ndi Bukhu la mbiriyakale. Ilo ndi Bukhu la chikondi. Ilo ndi Bukhu la—la masalmo. Ilo ndi Bukhu la Moyo. Ndipo mmenemo inu mumapezamo Khristu. Iye anali mwa aneneri. Iye anali mu Masalmo. Iye anali mu mbiriyakale. Ndipo Iye aponso, mu Baibulo, ali zinthu zomwe ziri nkudza. Chotero, Iye anali mmbuyo ndi mpaka patsogolo. Kodi zimenezo zikumupanga chiyani ndiye Iye? "Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

130 Ndipo inu mukabairamo chinachake Mmenemo, chimene sichikumupanga Iye "yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," M'bale Lee, kodi inu mupita kuti? Inu mukhala ndi chithunzi choipa pamenepo. Pakuti, Iye anali mbiriyakale, mwaona, ndipo Iye ndi Mneneri. Iye ndi Masalmo. Iye ali chirichonse. Ndipo ngati inu simungakhoze kumupanga Iye chirichonse, ndi yemweyo, malo, kodi chithunzi

chanu chiwoneka motani? Kodi inu mukuziwona zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino.

131 Iye ali chinthucho! Iye anali aneneri. Iye anali mwa iwo. Iye anali mu Masalmo. Iye anali mu mbiriyakale, ndipo Iye ali zinthu ziri nkudza, "yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Ahebri 13:8, ngati inu mukulemba zimenezo. Iye ayenera kukhala, ndiye, Iye ayenera kukhala chimake, ngati ndicho chimene Iye ali. Ndipo ife tikukhulupirira zimenezo, sichoncho ife? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi]. Ndiye, ngati Iye ali chimenecho, ndiye Iye ayenera kukhala chimake cha nkhani ya kuyankhula kwathu, cha kuganiza kwathu, cha kuyimba kwathu, cha mayendedwe athu. ["Ameni."] Iye ayenera kukhala chimake cha nkhani ya moyo wathu. Ngati Iye ali chimake cha nkhani ya Baibulo, ndipo Baibulo liri mwa ife, ndiye Iye ayenera kukhala chimake cha nkhani ya chirichonse chimene ife tikuchita, kunena, kapena kuganiza; ayenera kukhala Khristu. Nkulondola uko? ["Ameni."] Chabwino.

132 Pakuti, ife timaganiza izi, kuyambira pamene Iye wakhala atapangidwa—wapangidwa kukhala Mutu wa "zinthu zonse," kwa ife. Akolose wanena chomwecho apa. Iye ali Mutu wa "zinthu zonse," kwa ife. Pakuti Iye anapangidwa... chifukwa cha ife, chimene ife tikuganizidwa "zinthu zonse." Inu mukuti, "Nanga bwanji wochimwa?" Iye anapangidwa kuti adzakhale Woweruza wa wochimwa ngati iye salandira Zimenezo. Iye anapangidwa ulemelero kwa wokhulupirira yemwe alandire Zimenezo. Chotero pamenepo, chinthucho, "zinthu zonse zinapangidwa ndi Iye, ndi kwa Iye."

133 Ndipo izo zimatengera usiku, kuti ufotokoze ulemelero wa usana. Zimatengera chotengera chamanyazi, kuti chifotokoze—chikondi ndi chisamaliro cha chotengera cha ulemu. Zimatengera mkazi woyipa, yemwe angavale zovala zamakhalidwe oyipa ndi—ndi kumagulitsa makhalidwe ake, kuti afotokoze ukoma wa dona weniweni wamakhalidwe. Mukuona? Zimatengera tambwali ndi wakuba, mwa munthu, kuti zifotokoze chenicheni cha wokhulupirira weniweni, Mkhristu weniweni. Zimatengera wachinyengo, kuti zimusonyeze wokhulupirira, chimene iye ali.

134 Chotero, "Zinthu zonse zinapangidwa ndi Iye." Ndipo pakuti Iye anapangidwira zinthu zonse... anapangidwira, tonse a ife, zinthu zonse zinapangidwira, ndi Iye. Ndiye, pakuti izo ndi zoona, ife tiyenera kupanga kuzindikiritsidwa kwathu (kuyenera kukhala) ndi Iye. Ife tiyenera tizizindikiritsidwa, ifeeni, ndi Iye, chifukwa Iye wadzizindikiritsa Iyemwini ndi ife. Ife tiyenera kukhala ozindikiritsidwa ndi Iye. Motani? Pomukhalira moyo Iyeyo; osati zongonena.

135 Anthu ochuluka kwambiri amatenga zongonena, amati... ine ndikuti izo zafika pa malo awa tsopano. Kodi ndinu

Mkhristu? "Ndine wa Methodisti." Chabwino, zimenezo ndi ulendo wautali kuti ukhale, kudzipangitsa wekha kuti akudziwe ngati Mkhristu. Chabwino, taonani zimene a Methodisti amachita. "Ndine wa Baptisti." Chabwino, taonani zimene Abaptisti amachita. "Ndine Mkatolika." Taonani zimene iwo amachita. Mukuona?

136 Koma njira yokhayo imene iwe ungakhoze kukhala kwenikweni Mkhristu ndi kuti Khristu azidzizindikiritsa Yekha mwa iwe. Momwe ife tiriri ndi china, chobaya pamenepo! Ine ndikuyembekeza aliyense pa tepi akumvetsa zimenezo, nawonso. Mukuona? Mukuona? Mukuona?

Inu mukuti, "Ndine wa Chipentekoste." Zimenezo sizitanthauza kanthu.

137 Ndi Khristu akuzindikiritsidwa mwa inu. Ndi pamene Iye wakuzindikirani inu.

Mukuti, "Ine ndinayankhula ndi malirime." Adierekezi amatero, nawonso.

138 "Ine ndinafuula." Achimuhamadi, Achibuddha, ndi chirichonse amafuula. Amwenye amafuula pa dansi ya njoka. Mukuona? Zedi. Iwo onse amatero. Mipingu, magulu, ndi china chirichonse, amakuwa ndi kufuula. Iwo amakuwa ndi kufuula pa masewero a mpira.

139 Koma pamene Khristu azindikiritsidwa mwa iwe, akuzidzindikiritsa Yekha, zikatero ndiwe wonga-Khristu. Chimene, mawu *Mkhristu* amatanthauza kukhala "wonga Khristu." Uko ndiko kuzindikiritsidwa kwanu. Chabwino. Tsopano, ndipo pakuti Iye ndiye wotizindikiritsa wathu, ndiye ife tiyenera kumazindikiritsidwa ndi Iye, pakumukhalira moyo Iye.

140 Zindikirani, Mulungu wakhala ali nacho cholinga chofutukuka patatu mu chinsinsi chobisika chachikulu ichi. Mulungu, mu chinsinsi Chake chobisika chachikulu chimene Iye anali nacho dziko lisanayambe, Iye ali nacho cholinga chofutukuka patatu mu icho. Ndipo tsopano chimene ife tikufuna kuti tipitepo, mmawa uno, ndicho, cholinga chofutukuka patatu chimenecho ndi chiyani? Mukuona? Tsopano, ine ndikukhulupirira, mwa kuthandizidwa ndi . . . Mulungu, Yemwe ali pano, ndipo Iye—Iye asonyeza izo kwa ife. Tsopano, ngati Iye anali nacho cholinga chofutukuka patatu ichi, ife tikufuna kuti tipeze chimene cholinga chofutukuka patatu ichi chiri.

141 Chinthu choyamba chinali, kuti, Mulungu ankafuna kuti adziulule Iyemwini kwa anthu.

142 Iye sakanakhoza kuchita izo monga Mulungu Yehova wamkulu Yemwe amaphimba danga lonse, nthawi, ndi Umuyaya. Iye sakanakhoza kutero. Iye ndi wamkulu

kwambiri kuti awululidwe konse kwa anthu, chifukwa icho chikanakhala chachinsinsi kwambiri. Chikanakhoza bwanji chinthu chachikulu icho chimene sichinachite kuyamba . . . kuti mutapita kudutsa mkombero wa mazana a mabillioni ndi matrillioni ndi matrillioni a zaka za danga la kuwala, ndi kumapitirira mpaka kukafika kopandamalire, mpaka mu Muyaya, ndipo Cholengedwa chachikulu chimene chinali zonsezo, ndipo chikadalipobe.

143 Koma chimene Iye ankafuna kuti achite, Iye ankakonda utate, pakuti Iye anali Atate. Ndipo njira yokhayo imene Iye akanakhoza kufotokozera izo inali kuti adzakhale Mwana wa Munthu. Ndi chifukwa chake Yesu ankapitirira kumati, "Mwana wa munthu." Mukuona, iwo sankadziwa chimene Iye anali kuchiyankhula, ambiri a iwo. Koma tsopano inu mukumvetsa zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mukuona? Iye ankafuna kuti adzifotokoze Yekha. Icho chinali Chake, chimodzi cha zolinga Zake zofutukuka patatu, chinali kuti adzadzifotokoze Yekha, adzadzizindikiritse Yekha ndi anthu okhalapo, kuti adzadziwulule Yekha mwa Khristu.

144 Chachiwiri, kuti adzakhale nawo uyambiriro mu Thupi Lake la okhulupirira, amenewo ndi, Mkwatibwi Wake, kuti Iye adzakhoze kumakhala mwa anthu.

145 Tsopano, Iye akanakhoza kuchita zimenezo mwa Adamu ndi Eva, koma tchimo linawalekanitsa iwo, chotero tsopano pamayenera kukhala njira ina kuti adzabwezeretse zimenezo kachiwiri. Oh, mai! Oh, pamene ine . . . Izi, izi ndi zolemera, kwa ine, basi ngakhale kuti ndingolingalira za zimenezo. Mukuona? Mukuona chimene cholinga cha Mulungu chinali? Tsopano ndi chifukwa chiyani Iye sanangomusunga Adamu ndi Eva monga chomwecho? Ndiye Iye sakanadzakhoza kukwanitsa kuti afotokoze chidzalo Chake, chikhumbo Chake chathunthu. Chifukwa, Iye akanakhoza kukhala Atate kumeneko, izo nzoona, koma paja Iye ndi Mpulumutsinso. Inu mukuti, "Inu mukudziwa bwanji kuti Iye anali?" Iye ali, chifukwa ndinakhalapo nacho chondichitikira. Mukuona? Mukuona? Iye ndi Mpulumutsi, ndipo Iye ankayenera kuti adzachifotokoze chimenecho. Ndipo Iye akanakhoza kuchichita icho motani? Kokha kudutsira mwa Khristu. Iye akanakhoza bwanji kukhala Mwana? Kokha kudutsira mwa Khristu. Iye akanakhoza bwanji kukhala Mchiritsi? Kokha kudutsira mwa Khristu. Mukuona, zinthu zonse zikudzathera mwa Munthu mmodzi ameneyo, Yesu Khristu. Oh, mai! Pamene ine—pamene ine . . .

146 Pamene ine ndiganiza za zimenezo, ine—ine ndimangowona zipembedzo zikuchoka powonekera, ndi china chirichonse chikupita basi, mwaona, pamene ine ndiwona cholinga chachikulu cha Mulungu. Akudziwulula Yekha, ndi kukhala nako, poyamba, kuti adziwulule Yekha mwa Khristu, "chidzalo cha Umulungu mthupi." Ndipo, kenako, kuti adzabweretse

icho “chidzalo cha Umulungu mthupi” kubwera mwa anthu, kuti Iye adzakhoze kukhala nawo uyambiriro, kupenyeratu, kutsogolera.

147 Imodzi ina, usiku, ngati inu simunaipeze tepiyo, ine ndinalalikira pano usiku wina, pa “Wamndende wa Yesu Khristu.” Paulo, wamndende! Mukuona? Pamene Mulungu akutenga iwe kuti ukhale wamndende Wake, ndiye iwe sungakhoze kuchita kanthu koma chimene Mzimu ukunena kuti uchite. Paulo, ndi luntha lake lonse lalikulu, iye anaphunzitsa. . .iye anaphunzitsidwa ndi Gamaliele kuti adzakhale wansembe wamkulu kapena mphunzitsi, tsikulina. Ndipo iye anali ndi zokhumba zapamwamba. Iye mwaluntha anali munthu wamkulu, ulamuliro waukulu, munthu wamkulu mu fukolo. Koma iye ankayenera kupereka nsembe chidutswa chirichonse cha zimenezo, mwaona, kuti akhale gawo la Mawu, kuti adzamuwonetsere Yesu Khristu. Iye ankadziwa chimene icho chinali kufika ponena kuti . . .

148 Iye anali ndi lingaliro kuti apite ku malo enaake, abale enaake anali atamuitana iye, koma iye amaletsedwa ndi Mzimu kuti achite zofuna zake zomwe. Oh, ngati—ngati anthu auzimu mwatheka akanakhoza kuzimvetsa izo! Mukuona? Iye amaletsedwa kuti achite zofuna zake zomwe. Iye amakhoza kokha kuchita . . . “Mzimu wandiletsa ine.” Mukuona? Iye anali wamndende kwa Khristu.

149 Ndiye, wambwebwe wamng’ono uyu tsiku lina, yemwe iye ankamudziwa, Paulo ankadziwa kuti iye anali ndi mphamvu yoti atulutse mdierekezi ameneyo, koma iye akanakhoza kokha kuchita zimenezo pamene Mulungu aloleza izo. Tsiku ndi tsiku iye ankamutsatira iye, akufuulira pa iye, koma tsiku lina Mzimu unamupatsa iye chilolezo. Ndiye iye anamudzudzula iye, mzimu umene unali mwa iye. Mukuona? Iye ankadziwa chimene chinali kukhala wamndende.

150 Mose, luntha lake, iye ankayenera kuti azitaye zimenezo ndi cholinga chakuti amupeze Khristu, kuti akhale wamndende. Ndiye pamene Mulungu anapuntha chidziko chonse mwa iye, ndi umamuna wamphamvu wonse umene iye anali, ndi kudzaima mu Kukhalapo kwa Lawi la Moto tsiku lija, iye anapezeka basi wopanda chonena. Iye sanati nkomwe, sankakhoza ngakhale kuyankhula, iye anati. Mulungu anali ndi wamndende pamenepo. Mukuona? Inu simungati muziyesa izo mwa kufufuza kwanu kwanu. Ndiye Mulungu anachita kumupatsa munthu uyu, kapena, kumuveka iye ndi mphamvu zokwanira kuti iye azikhoza kupita kumeneko.

151 Ndipo iye anati, “Ambuye, ine ndamuuza Farao zimene Inu munanena, ndipo iye sakukhoza kuchita izo.”

152 Iye anati, “Ndiye tenga iyi, ndodo yako,” Mulungu akuyankhula, amenewo ndi Mawu a Mulungu, “pita kunja

uko ndipo ukailozetse iyo cha Kummawa, ndipo ukaitanire ntchentche." Ndipo ntchentche zinabwera polengedwa, chifukwa Iye anali ndi wamndende yemwe Farao sakanakhoza kumugula ndi kanthu. Palibe munthu wina aliyense akanakhoza kumutembenuzira iye njira iliyonse. Iye anali wamndende kwathunthu mu unyolo wa Mawu a Mulungu, wongomangidwira ku PAKUTI ATERO AMBUYE yekha.

153 Oh, ngati Mulungu angakhoze kudzipezera Iye amndende onga amenewo! Tsopano, ndi pamene Iye angakhoze kufotokozera uyambiriro, inu mwaona, Iye—Iye wamupeza mwamuna, kapena munthuyo, mwakuti iye sakudziwa kanthu kena koma Khristu. Inu mukumvetsa zimene ine ndikutanthauza? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino. Ndicho chachiwiri.

154 Choyamba, kuti adzadzifotokoze Yekha kwathunthu, Mulungu mwa Khristu.

155 Chachiwiri, kuti adzakhale nawo uyambiriro, mwa ichi, mu Mpingo Wake, limene liri Thupi Lake, Mkwatibwi, kufika pakuti Iye azikhala ndi uyambiriro kuti adzifotokoze Yekha kudzera mwa iwo. Chabwino.

156 Ndipo, chachitatu, kuti adzabwezeretse Ufumu ku malo ake oyenera, umene unagwa ndi tchimo ndi Adamu woyamba, kubwerera kumene Iye ankayenda madzulo ozizira ndi anthu Ake, kumayankhula nawo iwo, kumayanjana nawo iwo.

157 Ndipo tsopano tchimo ndi imfa zinali zitawalekanitsa iwo kuchoka ku Kukhalapo Kwake ndi chifotokozero Chake chonse. Kodi mukuwerenga zimenezo? Asanaikidwe maziko a dziko lapansi, kuti adzafotokozere Zake zonse—Zake—zikhumbo Zake, chimene Iye anali.

158 Chotero, ngati Wautatu aliyense pano ngati mutangoti mungodzisiya nokha momasuka miniti yokha, inu mukhoza kuwona kuti Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera si Amulungu atatu. Ndi zikhumbo zitatu za Mulungu yemweyo. Mukuona, ndi kufotokoza. Atate, Iye anali, ankafuna kuti akhale Atate. Iye anali Atate, Iye anali Mwana. Ndipo Iye ndi Mzimu Woyera. Ndipo Atate ndi Mzimu Woyera ndi Mzimu womwe womwewo. Kodi inu simukuwona? Inu mukumvetsa izi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Osati Amulungu atatu. Mdierekezi anakuuzani inu zinthu zimenezo, kuti akupangeni kukhala wopembedzamafano. Mukuona? Ndi Mulungu mmodzi akufotokozeredwa mu zikhumbo zitatu. Kuti adzakhale Atate, kuti adzakhale Mpulumutsi, kuti adzakhale Mwana, kuti adzakhale Mchiritsi, mukuona, ndizo zifotokozero Zake.

159 Ine ndikufuna kuti ndiyende pang'ono pang'ono kuchitira kuti ngakhale anthu odzamvetsera pa tepiyi adzakhoze kuligwira lingalirolo, kuti adzakhoze kuwona. Zinganditengere ine kuzungulira, kuzungulira wotchi imeneyo, basi lirilonse

la maphunziro amenewo. Koma ine ndikuyembekeza kuti ndikuzipanga izo momveka bwino kuti inu mukhoza kuwona chimene ine ndiri kubwerapo. Mukuona?

160 Mulungu, anafotokozedwa mwa Yesu Khristu, Yemwe anali zonse Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, "chidzalo cha Umulungu mthupi."

161 Tsopano "chidzalo chathunthu cha Umulungu mu thupi" chikukhala mu Mpingo Wake, uyambiriro. Zonse zimene Mulungu anali, Iye anazitsanulira mwa Khristu; ndipo zonse Khristu anali, zinatsanuliridwa mu Mpingo, okhulupirira.

162 Osati chipembedzo! Ife tifika kwa izo mu maminiti pang'ono, ndipo icho chichotsa izo mmalingaliro anu kwanthawizonse, mwaona; kukusonyezani inu chimene chimayambitsa izo, mwa thandizo la Mulungu, ngati Iye ati angoziloleza izo kwa ife.

163 Cholinga Chake ndi chiyani tsopano? Kudzifotokoza Yekha ngati Mwana, mwaona, ndipo, tsopano, kuti mwa Iye mukakhoze kukhala "chidzalo cha Umulungu mthupi." Ine, ine ndiri ndi Akolose ali apa, patsogolo panga pomwe. Mukuona? Kuti, monse kudutsa Lemba, ndicho chimene cholinga cha Mulungu chinali. Ndiye, kudutsa mu Moyo uwu wa Mwana uyu, mtanda Wake, "Magazi," zikunenedwa apa, "a mtanda Wake," kuti Iye akakhoze kuyanjanitsa kwa Iyemwini Thupi, Mkwatibwi; yemwe ali Eva, Eva wachiwiri. Ndipo Mulungu anapereka izo mwa choyimira, monga Iye anachitira ndi Mose ndi onse amenewo. Chinthu chomwecho chimene Iye anachita mwa Adamu ndi Eva, kupereka choyimira, kuti iwo anali Khristu ndi Mkwatibwi. Iye ndi Adamu wachiwiri; Mpingo ndi Eva wachiwiri.

164 Ndipo bola ngati Eva wachiwiri akunyengerera motsutsa Mawu, kodi iye sakuchita chinthu chomwecho chimene Eva woyamba anachita? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Kuyesetsa kuti aziti, "Chabwino, izo zinali za m'badwo wina." Ndipo ife tifika kwa izo mu maminiti angapo, ngati Iye ananena kuti izo zinali za m'badwo wina. Kodi izo zingakhoze bwanji kukhala m'badwo wina, pamene Iye ali "yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse"?

165 Koma Mulungu analinga izo ndipo "anazibisa izo kwa maso a luntha ndi anzeru, ndipo anaziwulula izo kwa makanda okonzedweratu" amene anakonzedweratu kuti adzazilandire izo.

166 Ndi chifukwa chake, penyani mmusi kudutsa m'badwo, nthawizonse pamene Kuwala kumeneko kuwagunda ena, iwo amakutembenukira Iko nkuchokapo, ndipo Iko kumakawalira kutali. Ndipo aluntha aakulu ndi ansembe aakulu awo ataima pamenepo, uko kunali marabi ochokera kwa aphunzitsi aakulu ndi maulamuliro, monga ena osiyanasiyana, monga Nikodimo

ndi iwo, munthu wopukutidwa mwa usikolala, ndipo iye sankakhoza nkomwe kumvetsa Zimenezo.

167 Ndipo uko kunali ansembe aakulu awo amene anaima apo, ndi marabi amene anaphunzitsidwa mu Mawu amenewo. Mai, iwo ankawadziwa Iwo, mwaluntha! Ndipo Iye anati, "Inu ndinu wa atate anu, mdierekezi, ndipo ntchito zake inu mukuzichita." Taganizani za zimenezo, anthu oyera, iwe sukanakhoza kuyika chala chako pa moyo wawo, kapena moyo wa abambo awo, kapena moyo wa agogo awo, kapena moyo wa agogo-agogo-agogo-agogo-agogo aamuna. Ngati iwo atero, iwo amafa mwa manyazi, iwo ankagendedwa mpaka afe. Koma apa pakuima Yesu, kumalitcha gulu limenelo, "mulu wa adierekezi," anthu achipembedzo.

168 Tsopano, oh, vumbulutso lalikulu tsopano! Tsopano kuti adzabwezeretsenso chibale Chake, kuti adzabweretsenso... Tsopano, Iye anachita kuwalola iwo kuti ataike. Inu mukumvetsa zimenezo? Iye anachita kuwalola iwo kuti achimwe, anawaika iwo pa kudzisankhira...Iye—Iye sakanakhoza kuwapangitsa iwo kuti achimwe, ndi kukhalabe Mulungu, ndipo kenako nkuwalanga iwo pa chinachake chimene Iye anawapangitsa iwo kuti achite.

169 Koma pamene Iye anamuika munthu pa ubwanawe ndi Iyeyo, kenako anamulola munthu kumachita monga mwa kudzisankhira, mwaona, chinthu chomwecho Iye wakutengeranipo inu lero. Mukuona? Mukuona? Inu muzichita mwanjira iliyonse imene inu mukuifuna; ndinu odzisankhira. Chotero, ndiye, ngati Iye anamuika woyambayo monga chomwecho, Iye ayenera kumuika wachiwiri monga chomwecho, Iye ayenera kuti amuike aliyense monga chomwecho, kapena Iye anachita molakwika poyamba. Mukuona? Koma aliyense ali pa maziko ofanana amenewo.

170 Tsopano pozindikira, pobweretsanso zimenezo; ndi kumulola munthu ameneyo kuti achite zimenezo, ndi kumadziwa kuti iye akanati adzachite zimenezo, ankadziwa kuti iye akanati adzachite izo. Koma kodi izo zinachita chiyani? Izo zinawonetsera chikhumbo Chake monga Mpulumutsi. Ndipo cholinga chonse ndiye chinasiyidwa mwa Yesu Khristu, kuti akhale...Mulungu Mwiniwake kuti adzatenge chilango cha lamulo Lake Lomwe, imfa, kuti adzafe, kuti adzamuwombole mkazi yemwe anali atataika pomukana Iye.

171 Pamene Eva anapita kutali ndi Mawu, iye anapita kutali ndi mwamuna wake. Ndipo pamene mpingo upita kutali ndi Mawu, kupita ku chipembedzo, iwo umakana ndipo umachita ziwerewere ndi dziko la nzeru za munthu, kuwukana ulamuliro wa Mawu a Mulungu. Izo zikumveka bwino? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Baibulo linati, "Kuchita ziwerewere zauzimu." Mawu aliwonse mu Baibulo, amene akanidwa,

kapena ngati kutanthauzira kulikonse kwanokha kuikidwa pa Iwo, ndiko mwamtheradi kuwakana ndi kuchita chigololo molakwira Mawu amene ali Mwamuna wanu. Wachigololo sadzalowa konse Ufumu wa Kumwamba, ife tikudziwa zimenezo. Mukuona? Tsopano, mwaona, ndizo zimene Eva anachita pa malo oyambirira.

172 Tsopano zindikirani kachiwiri, tsopano, kodi cholinga Chake chofutukuka patatu ndi chiyani? Kudziwonetsera Yekha mwa Yesu Khristu; kuti adzabwere mu Thupi, mwa Yesu Khristu, kuti adzakhale nawo uyambiriro; ku (chiyani?) kudzabwezeretsanso Edeni, kudzabweretsanso chijachi chimene chinataika. Icho chinali chinthu chokhacho chimene chinachoka mu dongosolo. Zinthu Zake zina zonse zinali mu dongosolo.

173 Koma Iye ankayenera kuti amulole, amuike munthu pa kudzisankhira, kuti adzagwe, kotero kuti Iye adzakhoze kukhala Mpulumutsi, kuti adzawonetsere chimene chiri mwa Iye, mwaona, chikhumbo Chake cha Mpulumutsi. Chinachake chinkayenera kuti chidzataike. Ndipo chinthu kumene, chimene munthu anagwako ndi kukhala wotayika, Iye anadzakhala Mpulumutsi wa chimenecho, anatenga lamulo Lake Lomwe. Ndipo Iye sakanakhoza kuzichita izo monga Yehova wamkulu uja yemwe ankaphimba danga lonse, nthawi; mwaona, Iye sakanakhoza kuchita zimenezo. Ndipo Iye ankayenera kuti adzakhale Munthu. Ndipo Iye anatenga ubale ndi munthu yemwe anali atatayika, ameni, ndipo anadzakhala Munthu: Mulungu, anapangidwa thupi!

174 Aleluya! Mukuganiza kuti ine ndatengeka; koma ine sindinatero. Chinachake mkatimu!

175 Mulungu anadzakhala, kuchokera kwa Mulungu, anadzakhala ine, kuti adzatengere tchimo langa pa Iye, kuti Iye adzakhoze kundipanga ine kukhala Iyeyo, ameni, kubwerera ku Cholinga Chake chachikulu cha ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, pakuti Iye ndi Atate Wamuyaya. Chikhumbo chimenecho chinali mwa Iye, mwaona, chotero icho chinkayenera kuti chidzawonetseredwe.

176 Tsopano mukuona cholinga chonse chofutukuka patatu? Mwaona, kuti adzadzifotokoze Yekha, Iye akufuna kuti adzakhale . . . Tsopano, a—dziko latayika, tsopano Iye anayenera kuti adzadzifotokoze Iyemwini mwa Munthu, kuti adzakhale Mpulumutsi, kudzera mu chiyanjanitso cha Magazi kuchokera pa mtanda Wake. Tsopano, Iye ankayenera kuti adzakhale chimenecho, kuti adzafe, ndi cholinga chakuti adzapulumutse ndi kudzadzibweretsa Iyemwini mu Mpingo, kuti adzakhale nawo uyambiriro mu Mpingo Wake.

177 Tsopano kumbukirani, izo sizingakhoze, ndipo sizidzakhoza, ndipo sizidzakhala konse, ndipo sizinayambe zakhalapo ziri chipembedzo! Iye ayenera kukhala nawo uyambiriro, ndipo Iye

ndi Mawu. Ameni! Zingatheke bwanji kuti kachikhulupiriro kalikonse kabairidwe mkati Mmenemo? Izo ndi . . . izo zingawusandutse mpingo kukhala wachiwerewere, ukamatenga mawu a munthu aliyense a kachikhulupiriro kalikonse kapena chipembedzo chirichonse. Izo mwamsanga zimapatsidwa chilemba, mu Chivumbulutso 17, ngati hule ndi timahule; Mpingo wa Roma Katolika pokhala hule, ndi Achiprotestanti pokhala timahule. Zimenezo ndi ndendende zomveka monga munthu aliyense angakhoze kuziwerenga izo. Ife tinadutsa mu Mibadwo ya Mpingo, ndipo inu mukhoza kukaziwona izo mmenemo—matepi amenewo ngati inu mukuwafuna iwo. Ndendende. Ndiye, chirichonse chimene chimadzilumikiza chokha ndi kachikhulupiriro kunja kwa Baibulo, ndi hule pamaso pa Mulungu. Ndipo achita chinthu chomwecho chimene Eva anachita; achoka ku Mawu, amene ali Khristu. Oh, mai! Chabwino.

178 Tsopano ife tikuwona chinsinsi Chake Iye anali atachibisa mmalingaliro Ake asanaikidwe maziko a dziko lapansi. Tsopano kodi inu mungafune kuti tiwerenge pang'ono za zimenezi? Tiyeni tingoziwerenga izo. Kodi inu muli nayo nthawi yochuluka? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ife ti—ife tiwerenga izo. Tsopano tiyeni tonse titembenuzire, basi ku kuwerenga kumodzi, mulimonse, ku Bukhu la Aefeso, ndipo tiyeni tiyambire pa—mutu wa 1 wa Aefeso, kuti tiwerenge. Ndipo tsopano pamene phunziro la Sande sukulu likupitirira tsopano, mu mawonetseredwe ofutukuka patatu a Khristu awa, tiyeni tiwerenge.

> *Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu, . . .*

179 Tsopano penyani, izo siziri kulembedwera kwa dziko, koma:

> *. . . kwa oyera amene ali ku Efeso, ndi kwa okhulupirika mwa Khristu Yesu:*

180 Kodi inu mumalowa motani mwa Khristu Yesu? Mwa kujowina mpingo? [Osonkhana akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Mwa Kubadwa! "Mwa mzimu umodzi," Akorinto Woyamba 12, "ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi." Mukuona?

181 Chabwino, ndiwo amene iye akuyankhula nawo. Izo sizinalembedwere kwa dziko lakunja. Ife sitingakhoze kuyankhula kwa wochimwa pa izi, chifukwa iye sakudziwa kanthu za izo. Paulo sanali kulembera izo kwa ochimwa. Iye anati, "Izi ndi za kwa aja—aja—Gulu lija uko limene liri mwa Khristu Yesu."

> *Chisomo chikhale* kwa *inu*, *ndi mtendere, zochokera kwa Mulungu Atate athu, ndi kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu.*
>
> *Wodala akhale Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, yemwe* wa*tidalitsa ife ndi madalitso onse*

> *auzimu* (kutiko?) *mmalo ammwambamwamba mwa Khristu:*

182 "Malo Ammwambamwamba." Oh, momwe ine ndikukhumbira ndikanakhala nayo nthawi! Apa ine ndazilemba izo pomwe pano mu Baibulo langa, zokhudza malo Ammwambamwamba, chomwe chiri malo Ammwambamwamba. *Malo Ammwambamwamba,* kwa mphindi yokha, ndiwo "malo a wokhulupirira mwa Khristu," mwaona, "pamene wokhulupirira amaima mwa Khristu," mmalo Ammwambamwamba.

> *Malingana monga iye* anati*sankha ife*. . .(mvetserani mwatcheru). . .*anatisankha ife mwa iye asanaikidwe maziko a dziko lapansi,*. . .

183 Ndi liti pamene Iye anatisankha ife? "Asanaikidwe maziko a dziko lapansi," pamene chinsinsi Chake chachikulu chobisika, chinsinsi Chake chachikulu.

> . . .Iye anatisankha *ife mwa* Khristu *asanaikidwe maziko a dziko lapansi, kuti ife tikakhale tiri oyera ndi opanda chilema pamaso pa iye mu* (chiyani?) *chikondi:*

> *Atatha* (chiyani?) *kutikonzeratu ife kuti tikalowe ku kukhazikitsidwa kwa ana ndi Yesu Khristu kwa iyemwini, molingana ndi kukondweretsedwa bwino kwa chifuniro chake,*

184 "Kukonzedweratu!" Ndi chimenecho chinsinsicho. Iye, Khristu asanati kapena china chirichonse chisanakhalepo konse pa dziko lapansi, inu mukuona chinsinsi Chake chachikulu, kuti Iye anamusankha Mkwatibwi. Akudziwa kuti Eva akanadzagwa, chifukwa cha kusakhulupirira Mawu, akudziwa kuti iye akanati adzagwe; koma Iye akanati adzasankhe Mkwatibwi yemwe sakanati adzagwe, yemwe akanati adzagwiritsitse ku Mawu amenewo mosalabadira chimene onse a mdziko lonse akanati azinena za Iwo. Iwo akanati adzagwiritsitse ku Mawu amenewo! Iwo anakonzedweratu kuti adzaime pamenepo, "kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu," anawukonzeketseratu Mpingo ku maimidwe aakulu amenewo, kwa ulemelero!

185 Tsopano inu mukuwona chinsinsi Chake? Kuti adzatani? Kuti adzamubwezeretse Eva wakugwa, monga iye anali mthunzi woyambirira wa Mpingo. Ndipo tsopano zindikirani, monga Mulungu anatsegula mbali ya Adamu ndipo anatulutsamo Eva, ndi mnofu wake womwe ndi magazi; ndipo anawugawaniza mzimu wake kuchokera ku chachimuna ndi chachikazi, kwa chachikazi, ndi kudzawuyika iwo mwa Eva. Anatenga nthiti kuchokera pansi pa mbali yake, ndipo anampanga Eva kuchokera kwa iyo; chotero Mulungu anachita chinthu chomwecho, anatenga kuchokera mmbali mwa Khristu, Magazi ndi madzi. Ndipo Khristu ndiye Mawu, ndipo anawatenga

Mawu ndipo anapangira nawo Mpingo Wake, Eva; mwaona, kubwerera kwa Iyemwini kachiwiri, kuwomboledwa ndi Magazi amene anabwera kuchokera Mthupi Lake. Inu mukuziwona izi tsopano? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

186 Chinsinsi chachikulu cha Mulungu tsopano kukhala chikufutukulidwa, chimene chakhala chitabisika chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, koma chimawonetseredweratu njira yonse kudutsa mmusi. Tsopano penyani, ife tikupeza kuti, kuti Iye—kuti Iye anachita zimenezo. Ndipo apa mu Aefeso, ndi malo ena ambiri, koma izo zikupatsani inu zokwanira kuti . . . Tsopano, kutsika kudutsa mmibadwo, Iye wakhala mwapang'onopang'ono akufutukula chinsinsi ichi. Kodi inu mukukhoza kuchiwona tsopano? Tsopano, kutsika kudutsa . . .

187 Kodi Iye amachita motani . . .? Ndi chiyani chinachitika mu mthunzi woyambirira tsopano? Iye anatsegula mmbali ya Adamu ndipo anatengamo gawo la mnofu wake, umene unali Adamu, kuti amupange Eva. Mkwatibwi ayenera kukhala Mawu, pakuti Iye ali Mawu. Iye sangakhoze kuima pa tizikhulupiriro. Iye sangakhoze kuima pa chipembedzo. Iye sangakhoze kuima pa khalidwe labwino. Iye ayenera kuti aziyima yekhayekha pa Mawu, chifukwa Iye ali gawo la Iwo. Iye anatengedwa kuchokera kwa Khristu. Mukuona?

188 Ndipo kuti akhale wotsimikiza, kuti, Mkwatulo wonse tsopano: Luther anali gawo, Wesley anali gawo, aneneri anali gawo. Ngati iwo ali—si gawo . . . Basi mu vumbulutso mmene iwo anali kupanga, thupi, mapazi, zala, mikono, ndi zina zotero, mpakana Mutu (chimene ife tifike ku zimenezo mu maminiti angapo), mwaona, izo zikupangitsa Mkwatulo wonsewo. Ndi Thupi la Mawu, limene liri Khristu. Ameni!

189 Kunja kwa Ilo, iwe wataika. Ine sindikusamala momwe iwe uliri wabwino, kapena chimene chibale chako chiri, kapena chimene chiyanjano chako chiri, kapena chimene bungwe lako liri, ndiwe wotaika, kunja kwa Mawu amenewo kukhala mwa iwe.

190 "Ngati inu mukhala mwa Ine, Mawu, Mawu Anga akakhala mwa inu, ndiye inu pemphani chimene mukufuna," chifukwa inu ndi Mawu ndinu ofanana. Iye ali nawo uyambiriro. Iye ali nawo ulamuliro. Ndinu—ndinu wamndende kwa Iye. Dziko ndi lakufa. Inu mulibe chinthu china chowonjezera . . . Inu mukuwawona anthu ena onse akumakhala momwe iwo akuchitira, komabe inu simukuchita zimenezo. Ndinu wamndende. Inu mwamangidwa gori ndi Iye. "Gori Langa ndi lophweka." Kumangidwa gori ndi Khristu, ndi Mawu Ake. "Ine ndimachita icho chokha chimene . . . chimawakondweretsa Atate. Ndipo ngati inu simungakhoze kukhulupirira kuti Ine ndine Iye, ndiye mukhulupirire Mawuwo." Zangwiro kwambiri! Zindikirani.

191 Zindikirani tsopano, kutsika kudutsa mmibadwo, Iye wakhala mwapang'onopang'ono akuzilola izo kuti zitulukire poyera, mosathamanga kumafutukula chinsinsi, kudzera mwa aneneri ndi kudzera mu zoyimira. Tsopano ife tikhoza kumangopitirira pa zimenezo, ndi, kudzifotokoza Iyemwini.

192 Iye anadzifotokoza Iyemwini mwa Mose. Tayang'anani pa Mose. Anabadwa mu nthawi ya kuzunzidwa kwa ana. Iye anabadwa kuti adzakhale wowombola. Iye anabisidwa mu mnjeza, basi chimodzimodzi monga Yesu anatengedwera uko ku Igupto. Iye anatulukako. Iye anapita pamwamba pa phiri, anabwerera ndi malamulo.

193 Yesu anapita pamwamba pa phiri, ulaliki Wake woyamba, Ulaliki wa pa Phiri, anabwerera pansi ali ndi malamulo. "Inu munawamva iwo akunena, iwo a nthawi zakale, 'Iwe usadzachite chigololo.' Ine ndinena ndi inu, yense yemwe ayang'ana pa mkazi, ndi kumusilira iye, wachita naye chigololo." Wopereka-Lamulo, Wansembe, Mfumu, Mtsogoleri, ndendende basi!

194 Iye anadzifotokoza Yekha mwa Yosefe, anabadwa pakati pa achipembedzo, abale ake. Iwo ankamuda iye, popanda chifukwa, chifukwa iye anali wauzimu. Iye ankawona masomphenya. Mulungu anali ndi iye. Iye ankakhoza kutanthauzira maloto. Ndipo abale ake ankamuda iye. Iye anagulitsidwa kwa-. . . ndi abale ake, ndi pafupifupi ndalama sarte za siliva. Ndendende basi monga Iye anagulitsidwira ndi Yudasi Iskarioti, mmodzi wa abale Ake, ndi ndalama sarte za siliva. Iye anaponyedwa mdzenje ndipo analingaliridwa kuti wafa. Uko nkulondola. Bambo ndi iwo anawuzidwa kuti iye anali atafa. Kuti iye anaponyedwa mu dzenje; anatulutsidwamo, ndipo anapita ku dzanja lamanja la Farao.

195 Mu dzenje, momwe iye anakavutikira kumeneko! Ndipo—ndipo uko kunali awiri anapulumutsidwa . . . Woperekera chikho ndi wophika mkate, mmodzi wa iwo anataika ndipo mmodzi anapulumutsidwa, kani. Ndipo—woperekera chikho . . . Mmodzi wa iwo anataika ndipo winayo anapulumutsidwa. Basi monga pa Mtanda, pamene Iye anali mnyumba ya ndende Yake, atakhomedweredwa ku mtanda chifukwa cha machimo athu, pamene Iye anadzakhala Wamndende, mbava imodzi inataika ndipo wina anapulumutsidwa. Mwaona, ndendende basi.

196 Ndiye iye anadzakhala ku dzanja lamanja la Farao, mfumu yemwe iye anamulota, yemwe anali nawo masomphenya kuti iye akanati adzakhale pa mapazi a mfumu, ndipo ulamuliro wonse mu Igupto unapatsidwa kwa iye. Masomphenya ake anayenera kufika pochitika. Iye akhoza kuti ankazitsatira izo, nthawi zambiri, pamene iye anali—mndende ija kumeneko. Ndevu zake zikukula, ndi zina zotero, koma iye anazitsatira izo. Tsiku lina masomphenya ake ankayenera kudzafika pochitika.

197 Ngakhale izo zinachedwa, ziyenera kuti zichitike! Monga ine ndinanena usiku wathawu, kapena dzana usiku, Lachitatu usiku pano pa msonkhano. Mwaona, izo ziyenera kuti zichitike. Pamene Mulungu anena chomwecho, izo ziyenera kuchitika. Iye ndi mneneri wotsimikiziridwa, ndipo izo ziyenera kufika pochitika, chifukwa ndi Mawu a Mulungu.

198 Ndipo Mawu amabwera kwa mneneri yekha. Mawu akuti *mneneri* amatanthauza "wowulula wa Mawu Auzimu olembedwa," mofanana monga zimachitikira ndi "wolosera," mwaona, kapena "mpenyi." Zindikirani. Ndipo mpenyi, momwe, mmodzi yemwe inu mukumudziwa kuti akuneneratu, iye amatsimikiziridwa Mwaumulungu pa kuwoneratu, ndipo izo zimadzachitika. "Ngati alipo mmodzi yemwe ali mneneri, akayankhula kwa inu ndi kukuuzani inu zinthu zinazake zichitika. Ndipo ngati izo sizichitika, musamumvere iye. Koma ngati izo zichitika, ndiye Ine ndiri ndi iye. Inu kulibwino muzimuwopa iye, chifukwa ine ndiri ndi iye, inu mukuona." Ndizo ndendende. Kumeneko ndiko kutsimikiziridwa, apo ndi pamene inu mumadziwa ngati chiri Choonadi kapena ngati icho sichiri.

199 Mulungu akuyankhula moyankha kudzera mu Mawu Ake, kupita kwa anthu Ake, mwa anthu. Mukuona, Mulungu amayankhula kupyolera mwa munthu basi. "Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi." Mpesa sumabala chipatso. Nthambi zimayankhula, zimabala chipatso cha Mpesa. Zindikirani, izo nthawizonse zakhala ziri mwanjira imeneyo.

200 Tsopano ife tikumupeza Yosefe, ndiye, kuti pamene panalibe munthu akanakhoza kumukhudza kapena kubwera kwa Farao popanda choyamba kumuwona Yosefe. "Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Atate, mwa Mwana yekha basi." Ndipo pamene Yosefe akuchoka pa mpandowachifumu, iwo ankawomba malipenga, "Bondo lirilonse linkagwada! Yosefe akubwera uko!"

201 Ulemelero! Ndipo tsiku lina bondo lirilonse lidzagwada, ndi lirime lirilonse lidzavomereza, pamene Iye azidzachoka pa Mpandowachifumu wa Atate Ake, mwaona, kuti azibwera. Munthu aliyense adzachitira umboni kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Inu mwina. . .Izo zidzakhala mochedwa pamenepo. Chitani izo tsopano.

202 Tsopano ife tikuzindikira kuti kupyolera mu zoyimira, Ife tikhoza kumutenga ngakhale Davide, monga ine ndinayankhulira kanthawi kapitako, akuchoka pa mpandowachifumu wake, atakanidwa ndi anthu ake omwe; akukwera pa phiri lomwelo, Phiri la Azitona, pamene iye anali akupita ku ndende yake. Iye anali akupita ku nyumba yake ya ndende chifukwa iye anali atakanidwa ndi abale ake ndi anthu ake omwe. Iye amapita chokwera, akulira. Umenewo

unali Mzimu wa Khristu mwa iye, kuti adzakanidwa pamene iye ankayang'ana pa Yerusalemu ndipo analira, ndipo anati, "Yerusalemu, mowirikiza bwanji Ine..." Mfumu yokanidwa. Zaka eyiti handiredi mtsogolo, Mwana wa Davide anadzaima pa Yerusalemu, pamwamba apo pa Yerusalemu, ndipo atakanidwa, ndipo analirira Yerusalemu, ndipo anati, "Tsopano ora lako lafika." Ndiko kulondola. Mukuona?

203 Zinthu zonsezo zinkaimira Iye, mwa choimira basi, komabe chinsinsi chinali chitabisika. Amuna amenewo sankadziwa chimene iwo anali kuchita. Iwo ankangodziwa kuti anali akutsogozedwa ndi Mzimu kuti achite zina. Tsopano, akuzisungira izo mmasiku otsiriza, ku vumbulutso lalikulu. Koma, kuzifotokoza izo, anadzifotokoza Yekha mwa Mose, ndi Davide, ndi Yosefe, ndi Eliya, ndipo mpaka mmusi kumadutsa. Inu...ife tikhoza kumutenga mmodzi aliyense wa aneneri amenewo, ndi kuibweretsa miyoyo yawo poyera ndi kusonyeza kuti iyo inafotokozera Yesu Khristu mwangwiro, ndendende. Komabe, osapereka konse chinsinsi Chake mwathunthu; kuyembekezera kuti adzachidziwitse icho mmasiku otsiriza monga Iye analonjezera, kuyembekezera kuti icho chidzamvetsedwe mwathunthu, mwaona, Iye asanachifotokoze icho. Ngati Iye akananena chinthu chonsecho...

204 Chifukwa, Baibulo linalembedwa mu zinsinsi. Yesu anawathokoza Atate chifukwa cha zimenezo, mwaona, kuti Ilo linalembedwa mu zinsinsi.

205 Tsopano, Kudza kwa Ambuye kuli mwa chinsinsi. Ife sitikudziwa pamene Iye ati adzabwere, momwe Iye ati adzadzere, koma ife tikudziwa kuti Iye akubwera. Mukuona? Ndipo chotero zinsinsi zonse za Mulungu zinali kuyembekezera tsiku lotsiriza ili. Iye atatsiriza kale, ndiye Iye akuwulula ndi kusonyeza zimene Iye wazichita. Oh, mai! Sanapereke nkomwe chinsinsi Chake mwathunthu.

206 Ziri basi monga izi, kufanizitsa Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. Tsopano, pamene Mulungu anamugwiritsa ntchito Martin Luther pa kutuluka kwa mpingo woyamba uja kapena m'badwo wa mpingo uja, ndipo pamene Iye anamugwiritsa ntchito John Wesley, ndipo Iye mwapang'onopang'ono amawatulutsa iwo powonekera, ndipo anali akuwulula mwa iwo m'badwo wa mpingo umenewo. Pamene ife... pamene zikubwerera mmbuyo kudutsa Baibulo tsopano ndi kukazifufuza. Koma mmasiku otsiriza, chifukwa chimene izo zinali chinthu chopambana chotero, kuti Iye anayankhula za izo apa ndipo anasonyeza Mabingu Seveni aja. Ndipo *Look* ndi *Life* ma-...

207 Magazini ya *Life* ndiye anaika Mkombero uja wa Mtambo ndi Kuwala pamenepo zomwe iwo sankakhoza kuzimvetsa,

ndipo sakuzidziwabe izo panobe. Koma apa anandiwuza, “Pita uko ndipo ukayembekezere zinsinsi izi zoti ziwululidwe,” ndipo kuno miyezi izo zisanachitike, ndiyeno izo zinachitika ndendende momwe Iye anati izo zikanati zidzachitikire. Kodi inu munazindikira mu chithunzi chija? Ngakhale Mngelo uja wa kumanja, pamene iye anali kukhala chogwirika, akubwera pansi, ali ndi mapiko ake mmbuyo ndi mutu wake utaikidwa cha mmbali, ndipo icho *apo* pomwe mu chithunzicho, ndendende basi. Miyezi izo zisanachitike, anatiwuza kuno, kuti, “Iye akudzabweretsa Thupi la okhulupirira pamodzi; kuti adzawulule, kudzatenga zakumapeto zotaikazo.”

208 Apa panabwera Luther anadzadutsamo, iye anangolalikira kulungamitsidwa, anangokhomerera mu m’badwo umenewo. Iye sankadziwa chimene m’badwowo unali. Apa panadzabwera Wesley anadzadutsamo, ndipo iye anakhomerera kudutsa m’badwo wakewo. Mukuona? Zolekerera zochuluka zinabwera kuchokera mwa iwo, mipingo ina inawukamo. Ndiye apa panadzabwera Chipentekoste, chinakhomerera apo, ndipo iwo anachita bungwe ndipo anapita mmbuyo momwe ku imfa kachiwiri; monga ife titi tifike kwa izo mu maminiti angapo, kubwerera mmbuyo mpaka ku “imfa.”

209 Ndiyeno nkudzabwera vumbulutso la chinsinsi, kuti lidzawulule chomwe izo zonse zimakhala ziri. Kumene, ziphunzitso zazing’ono izi, monga Luther anabweretsa katekisimu ndi china chirichonse; ndipo Wesley anabweretsa *ichi, icho,* ndi *chimzake,* ndi zinthu zina izi; ndipo kenako Pentekoste inadzabweretsa bungwe mofanana basi, ndi “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” kukhala ubatizo, ndi zinthu; osadziwa kusiyanitsa kwake, chifukwa. . .Ndiye nkudzabwerera mmasiku otsiriza ndi kudzatenga zinsinsi zonse izi ndi kudzazifotokoza izo momveka bwino, kudzaziwulula izo. Chifukwa chiyani? Zonsezo ndi masiku otsiriza pamene chinsinsi chachikulu ichi chimene Mulungu anali nacho mu mtima Mwake chiri kuwululidwa.

210 Kodi inu mukumvetsa zimenezi? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ngati mulephere, mudzabwererenso ku tepi iyi kachiwiri. Ine sindikudziwa kuti ndikhala nanu motalika bwanji. Kumbukirani, ichi ndi Choonadi, cha PAKUTI ATERO AMBUYE. Icho ndi Choonadi. Zimenezo ndi Lemba.

211 Monga zinsinsi zisanu ndi ziwiri za Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri zotsiriza, zinsinsi za izo. Zinsinsi zinali zitamatulidwa kale, ndipo m’badwo uliwonse unali utabwerapo, ndipo mmenemo iwo anali atasiya zomwazika zochuluka. Ndipo Mulungu, posalolera kuti izo zikhale zitamwazikana, Iye akubwereranso ndipo akudzatolera zinthu zimenezo, tiziphunzitso timeneto timene iwo anatiyamba, ndipo anazibweretsa izo poyera ndipo anadzawulula chinthu chonsecho. Chinthu chomwecho Iye akuchita tsopano pa

kuwulula chinsinsi cha Khristu, momwe Iye anali cholinga chofutukuka patatu cha Mulungu kwa Mpingo! Oh, mai! Kumulola Iye atulukire. Kuwulula!

212 *Kuwulula,* Webster amati, ndi "Kupangitsa kudziwika. Kupangitsa kudziwika, ndipo, makamaka," Webster akuti, "mu Choonadi Chaumulungu," *vumbulutso* limenelo limatanthauza. Vumbulutso, iyo ndi njira ya Khristu ya kudzipangitsa Yekha kudziwika kwa Mpingo Wake.

213 Tsopano ife tikunena kuti, "Tsopano, M'bale Branham, inu mukungonena izi." Tsopano, ife sitinena, *basi* mongonena izi.

214 Tsopano zindikirani, Iye anadzipangitsa Yekha kudziwika kwa Petro. Tsopano ngati inu mukufuna kuti muzilembe izi, ndipo ife. . . Ngati mukufuna kuti muwerenge zimenezo, ife—Ife tiwerenga izo, ngati mukufuna kutero, mu Mateyu Woyera 16:15 ndi 17. Ine ndibwereza izo. Pamene iwo anabwera kuchokera ku Phiri Lachiwalitsiro, Iye akuti, "Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine ndani?"

215 "Ena akuti, oh, iwo akuganiza Ndinu 'Eliya,' ndipo ena akuti Ndinu 'mmodzi wa aneneri,' 'Yeremia,' kapena ena a iwo." Koma izo sizinali zimene Iye anafunsa.

216 Iye anati, "Kodi inu mukuganiza kuti Ine ndine ndani tsopano?" Tsopano uwo ndi Mpingo umene Iye akuyankhula nawo. Mukuona?

"Kodi anthu akuganiza kuti Ine ndine yani?"

217 Lero, "Iye ndi wambalume; chipembedzo cha chitukuko ichi. Iye anali munthu wabwino. Ife timakhulupirira kuti chiphunzitso Chake ndi chabwino. Ndi koyenera kuti uzikhala moyo nacho. Ine ndikuganiza zingatipangitse ife tonse abwinoko, ngati titatero. Ife tiyenera kuti tikhale ndi matchalitchi athu, zathu—zathu zina zotere." Ndizo za Santa Claus, monga nthano ya Santa Claus.

218 Iko sindiko kufotokoza kwa mpingo wina kuti ife tizifotokoza chinachake. Ndi moyo umene iwe sumawukhala wekha, koma Iye amabwera mwa iwe ndi kumadzakhala moyo mwa Iyemwini, ndipo iwe nkusanduka wamndende; kwa munthu aliyense wa luntha lonse. Iwe umatsogozedwa ndi Mzimu. Ndipo iwe umadziwa chotani?

219 Tsopano, inu mukuti, "Ine ndikhoza kudziwa kuti malingaliro anga akusokonezeka. Mwinamwake munthu yemwe malingaliro ake akusokonezeka amachita zimenezo."

220 Koma ngati mukhala ndi lingaliro la Khristu, Khristu amadzifotokoza Yekha kudzera mwa inu, kusonyezera kuti ndi Iyeyo ndipo osati. . . inu simunasokonezeke malingaliro anu.

221 Anthu ena, pansi pa zilubwelubwe za zinthu, amatuluka ndipo amakakhala amisala. Chabwino, izo, ife tikudziwa izo ndi zolakwika. Ameneyo ndi mdierekezi akuyesetsa kuti

asanzire chinthu chenicheni icho chisanafike kuno, mwaona, nthawizonse zimakhala zonyengezera. Mukuona?

222 Koma munthu weniweni ndi woti amataya malingaliro ake ndi kuganiza kwake! Osati kungobwera pamenepo wakhungu monga chomwecho. Ayi, bwana. Iwe umabwera ndi malingaliro ako abwinobwino, ndipo Khristu amakutenga iwe ndipo amadzifotokozeramo Iyemwini. Ndipo tsopano, kwa dziko lapansi, ndiwe munthu wamisala.

223 Tsopano, ngati ndiwe wamisala, iwe ulidi wamisala, ndiye palibe kanthu. . .mdierekezi sangakhoze kukutenga iwe mu ulamuliro wathunthu. Iye adzakupangitsa iwe kuti uzichita chirichonse motsutsana ndi Mawu awa.

224 Koma pamene Khristu akutenga iwe, Iye adzawafotokozera Mawu amenewo kudzera mwa iwe, chifukwa ndi Iyeyo. Iye ndi Mawu! Mukuona? Ndiyeno iwe ukhoza kumawona kufotokozera kwa Khristu. Osati chinyengo china cha mtundu wina, koma Khristu weniweni akudzifotokozera Mwiniwake kudzera mwa iwe. Ndi zokongola bwanji!

225 Tsopano penyani. Iye anati, "Kodi inu mukuti Ine ndine yani?" Iye akuwufunsa Mpingo, thwelovu Ake. Kuchokera pa mamillioni a tsiku limenelo, Iye anawafunsa thwelovu, Mpingo Wake.

Mwa mamillioni mu masiku a Nowa, Iye anawafunsa eyiti. Uh-huh. Mukuona?

226 Ndipo Iye anati, "Monga izo zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso izo zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu, mwaona, kumene miyoyo eyiti inapulumutsidwa."

227 Ine sindikunena kuti padzakhala eyiti ati adzapulumutsidwe. Tsopano musati muzimvetse izo zonse molakwika. Ine sindinanene konse zimenezo. Ine sindikudziwa ochuluka bwanji ati adzakhale, ati adzapulumutsidwe mmenemo, kuti ndizo. . .mphindi yotsiriza imeneyo ku—kuti Adzakwatule gulu lapang'ono limenelo. Ilo lidzakhala gulu lapang'ono, ine ndikuuzani inu zimenezo. "Pakuti khwalala ndiro chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, koma apang'ono adzakhalapo omwe ati adzaipeze iyo."

228 Koma pamene Thupi lalikulu lowomboledwalo kudutsa mibadwo yonse liti lidzatulukire, ndiye umenewo udzakhala uli mpandowachifumu waukulu kumeneko! Chivumbulutso 7 amafotokoza izo, "Chiwerengero chachikulu, chimene palibe munthu angakhoze kuchiwerenga," kudutsa mibadwo yonse atabwera, iwo amene anayenda mu Kuwala kwa Baibulo momwe Iko kunawululidwira kwa iwo. Ndipo tsopano ife tikudziwa kuti Wesley anali nako Kuwala kochulukirapo kuposa Luther anali nako. Ife tikudziwa kuti Chipentekoste chinawala kumuposa Wesley. Mukuona? Ndithudi, iko kunatero.

229 Chifukwa, izo mwapang'onopang'ono akuzilola zizimasuka, monga izo zinkachitira kutsika kudutsa mwa aneneri, ndi ena otero, mpaka izo zinapangidwa kudziwika mwangwiro, "Umulungu mthupi mwa Khristu."

230 Ndipo tsopano Khristu mu Mpingo akungopangidwa kudziwika kumene. Chinthu chonsecho ndi vumbulutso la Mulungu, kuti amutengere Eva kubwerera ku malo ake oyenera kachiwiri ndi Mwamuna wake. Zindikirani, ndipo Mulungu ndi Mwamuna wa Mpingo, ndipo Mpingo ndi Mkwatibwi Wake.

231 Tsopano, Petro, pamene iye anamuuza, anati, "Inu ndinu Khristu Mwana wa Mulungu wamoyo."

232 Tsopano penyani. "Wodala ndiwe, Simoni *Bar-yona*," anatero, chimene chimatanthauza, "mwana wa Yona." Mukuona? "Wodala uli iwe, pakuti thupi ndi mwazi sizinawululire konse Izi kwa iwe. Iwe sunaziphunzire konse Izi kuchokera ku sukulu ina. Koma Atate Anga amene ali Kumwamba awulula Izi kwa iwe." Zindikirani zimene Iye ananena kwa iye, "Pa thanthwe ili. . ." Ameneyo ndi Petro, Mbewu yokonzedweratu ya Mulungu imene inali italandira Kuwala uku, ndipo anapatsidwa mafungulo aku Ufumu. "Pa thanthwe ili la vumbulutso la Yemwe Khristu ali," Iye ndi chidzalo, Mulungu wowonetseredwa. "Pa thanthwe ili. . ." Osati Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera; ndipo Iye nkukhala Munthu wachiwiri. "Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawugwedezera konse Iwo pansi, sizidzawugonjetsa konse Iwo." Mukuona? "Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga pa thanthwe ili," vumbulutso la Yesu Khristu.

233 Taonani, Khristu mwa inu zimamupangitsa Iye chirikati cha Moyo wa vumbulutso. Mukuona? Moyo wa Khristu ukakhala mwa inu zimamupangitsa Iye chirikati cha vumbulutso. Khristu, mu Baibulo, zimalipangitsa Baibulo kukhala vumbulutso lamphumphu la Khristu. Khristu akakhala mwa inu zimakupangitsani inu kukhala vumbulutso lamphumphu la chinthu chonsecho, mwaona, chimene Mulungu akuyesetsa kuti achichite.

234 Kodi Kubadwa kwatsopano ndi chiyani ndiye? Inu mukuti, "Chabwino, M'bale Branham, kodi Kubadwa kwatsopano ndi chiyani?" Iko ndi vumbulutso la Yesu Khristu likakhala lakolako kwa iwe. Ameni! Mukuona? Osati iwe kujowina mpingo, iwe kugwirana chanza, iwe unachita chinachake chosiyana, iwe unanena kachikhulupiriro, unalonjeza kukhala moyo motsatira—ndondomeko ya malangizo. Koma Khristu, Baibulo, Iye ndi Mawu amene anawululidwa kwa iwe. Ndipo ziribe kanthu zimene aliyense anena, zimene zikuchitika, ndi Khristu; m'busa, wansembe, chirichonse chimene icho

chingakhale. Ndi Khristu mwa iwe, limenelo ndiro vumbulutso limene Mpingo unamangidwirapo.

235 Inu mukuti, "Chabwino, ine ndine Wachilutera. Ine ndine wa Chibaptisti. Ine ndine Wachipresbateria." Zimenezo sizitanthauza chimodzi, sizitanthauza [M'bale Branham akukhwatchitsa chala chake—Mkonzi]. *chimenecho* kwa Mulungu, osati kanthu, osati kukhwatchitsa kwa chala chako.

236 Ndi chiyani chimenecho? Ndi Khristu kukhala akuwululidwa, ndipo Iye ndiye Mawu. Ndipo pamene Mawu awululidwa, Iwo amadzifotokoza Okha. Mukuona? Ndicho cholinga cha Mulungu kwa Yesu Khristu, chinali kuti adzadzifotokoze Iyemwini, kuti adzatenge malamulo Ake Omwe ndi kumakhala moyo ndi malamulo Akewo, ku-. . .ndi kudzakwaniritsa lamulo Lake, kudzera mu imfa. Ndipo Khristu, Mulungu, anafa mu thupi, ndicholinga chakuti adzaliweruze tchimo mu thupi, kuti Iye adzakhoze kubweretsa kwa Iyemwini Mkwatibwi waulemelero, atawomboledwanso, yemwe ati adzakhulupirire mu Mawu a Mulungu okha; ndipo osati kuwasinthanitsa Iwo, monga Eva anachitira, ndi malingaliro aluntha a munthu. Inu mukuziwona zimenezo? Limenelo ndi lingaliro la Khristu. Limenelo ndi lingaliro la Mulungu. Kubadwa kwatsopano kumaulula izi.

237 Ndipo ngati munthu anena kuti iye ndi wobadwa kachiwiri, ndi kumayesetsa kuwayika malonjezo awa a Khristu, mmasiku otsiriza ano, ku m'badwo winawake, kumupanga Iye Khristu dzulo koma osati lero, ndiye mwamuna ameneyo kapena munthu ameneyo wakhala ali mu—mu chisokonezeko ndi Satana. Ndipo ngati munthu ameneyo anena kuti iye akuzikhulupirira Zimenezo, ndipo izo sizikudziwonetsera zokha kudzera mwa iye?

238 Yesu ananena, mu Marko 16, "Zizindikiro izi zidzawatsira iwo amene akhulupirira; mu dziko lonse lapansi, ndi ku m'badwo uliwonse." Kutulutsa ziwanda, ndi kuyankhula ndi malirime, ndi—ndi mawonetseredwe aakulu onse awa a mphatso zomwe zidzatsatire, kuti, "iwo adzatero!" Osati, "iwo *mwina* akhoza; iwo *ayenera* kutero." "Iwo adzatero!" Ndipo miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Ake sadzatero.

239 Chotero ndi Khristu akudzifotokoza Yekha mwa munthu payekha, kaya ndi waluntha kapena iye ali—iye samadziwa ma ABC ake. Theka la ophunzira sankadziwa izo, ndiko kulondola, koma iwo ankamudziwa Khristu. Iwo sanazindikire konse za Petro ndi Yohane, podziwa kuti iwo anali ochokera ku seminare inayake. Iwo anati, "Iwo anazindikira ndipo anadziwa kuti iwo anakhala ali ndi Khristu," pamene iwo anamchiritsa munthu wolumala, mwaona, pa chipata. Iwo anadziwa iwo—iwo anakhala ali ndi Khristu.

240 Kubadwa kwatsopano ndi Khristu, ndi vumbulutso. Mulungu wawululira kwa iwe chinsinsi chachikulu ichi,

ndipo kumeneko ndi Kubadwa kwatsopano. Tsopano kodi iwe ungachite chiyani pamene ungalibweretse gulu lonselo pamodzi? kumene vumbulutso likumakhala mwangwiro mu chiyanjano, ndipo Mulungu akulifotokoza ilo kupyolera mu Mawu Ake mwa zochitika zomwezo, zinthu zomwezo zimene Iye anachita, kumawapangitsa Mawu kuwonetseredwa. Oh, ngati Mpingo ukanangoti udziwe malo ake! Iwo udzatero, tsiku lina. Zikadzatero, Mkwatulo udzapita pamene iwo udzadziwa chimene iwo uli. Tsopano zindikirani.

241 Inu mukuti, "M'bale Branham, koma izo—izo siziri . . ." Oh, inde, izo ziri, aponso. Izo ndi Choonadi.

242 Kodi inu munazindikira? Paulo sanamudziwe konse Yesu, mthupi. Paulo sanamudziwe konse Iye. Njira yokhayo yomwe Paulo anamudziwira Iye inali mwa vumbulutso, mwa masomphenya. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Paulo anangomudziwa Yesu mwa vumbulutso basi, chimodzimodzi monga Petro anachitira.

243 Petro anali atamuwona Iye mu thupi, koma iye sanamudziwe Iye mwa thupi, chifukwa Yesu ananena chomwecho. "Thupi ndi mwazi sizinawululire izi kwa iwe. Ngakhale moyo Wanga Womwe sunawululire izi kwa iwe. Koma Atate Anga amene ali Kumwamba awululira chinthucho kwa iwe," kuti Iye ndi Mawu a Mulungu, "ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga." Petro sanamudziwe Iye mwa thupi. Munthu ankayenda, ndipo amamugwira Iye, ndi china chirichonse.

244 Paulo anali ndi chinachake chokulirapo kuposa aliyense wa atumwi anali nacho. Mukuona?

245 Iwo anati, "Chabwino, ine—ine ndiri nalo vumbulutso lochuluka kuposa iwe, Paulo, chifukwa, iwe ukudziwa, ine ndinayenda ndi Iye. Ine ndinapita kukasodza ndi Iye, tsiku lina. Ine ndinamumva Iye akuyankhula. Iye anakhala mu ngalawa ndi ine, ndipo anandiuza kumene ine, 'Tiye tipite uko ndipo tikasodze mmalo awa, ndipo ife tikapeza nsomba zochuluka.' Ndipo ife tinachita zimenezo." Mukuona? Mukuona? "Ife tinamuwona Iye akuchita zinthu."

246 Koma Paulo anamuwona Iye atafa kale, ataikidwa mmanda, ndipo atawuka kachiwiri, ndipo anadzifotokoza Yekha mu Lawi la Moto limene linawatsogolera ana a Israeli. Podziwa . . . Paulo, pokhala Myuda, sakanakhoza konse kuchitchula icho "Ambuye" pokhapokha atawona kufotokozedwako, Iye anali atabwerera, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye anati, "Paulo," mwa kuyankhula kwina, "Ine ndine Mulungu yemweyo lero yemwe ndinalipo dzulo. Ine ndiri pano, mu Kuwala komweko, Lawi la Moto limene Mose anayankhula nalo, mu chitsamba chonyeka." Nzosadabwitsa iye ankakhoza kulekanitsa lamulo kwa chisomo, uko mu Bukhu la Ahebri; iye anakomana ndi

Lawi la Moto lomwelo. Iye anati, "Ine ndine Yesu, Yemwe iwe ukumuzunza."

247 Ndipo pano Iye ali lero, mu chikhalidwe chomwecho, mwa Lawi la Moto lomwelo, akudzifotokoza Yekha ndi kudzitsimikizira Yekha momwemo, kuwulula chinsinsi cha Mulungu chimene chakhala chitabisika chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi. Mukuziwona izi?

248 Paulo anangomudziwa Iye mwa—anamudziwa Iye mwa vumbulutso. Petro anamudziwa Iye mwa vumbulutso.

249 Iye anayenda ndi Iye, anayankhula ndi Iye. Chotero, iwe ukhoza kukhala mu Mawu awa. Tsopano, ine ndangonena kuti Iye anali Mawu. Tsopano, sikolala akhoza kukhala pansi ndi kuwerenga Mawu amenewo mpaka iye akhoza kungomanga malingaliro ako mwanjira iliyonse, mwaona, ngati iye atafuna kuti achite zimenezo, chifukwa iye ndi wanzeru, waluntha. Mumutenge wansembe wa Chikatolika, kapena, osati zochuluka zonga izo, monga wazafioloje wabwino wophunzitsidwa kwenikweni mu Baibulo. M'bale, wa Baptisti, kapena wa Chipresbateria, kapena chinachake, iye angakupange iwe kuganiza kuti sukudziwa kanthu, mwaona, pamene izo zifika pa kuyankhula. Chiyani? Mwaona, chifukwa chakuti iye wamudziwa Iye mwa thupi, Mawu. [M'bale Branham akusasa Baibulo lake—Mkonzi].

250 Koma njira yokhayo yomwe iwe umapulumutsidwa nayo ndi pa kumudziwa Iye mwa vumbulutso!

251 Ngati nditatenga, ine ndikhoza kutenga kachiphunzitso ka Chipresbateria ndi kukumangiririrani inu Achipentekoste mpaka inu osatha kudziwa. Ine ndikhoza kutenga kachiphunzitso ka Chibaptisti ndi kukusonyezani inu Achipentekoste zinthu millioni zimene inu simukudziwa kanthu ka izo. Ndiko kulondola, koma sindizo ayi. Umenewo si Mpingo Wake. Umenewo si Mpingo Wake.

252 Mpingo Wake ndi Iyemwini akamawululidwa, (Ameni! Kodi inu mukuziwona zimenezo?) ndi kumafotokozedwa mwa Mawu Iwoeni, kuti Iye ndi Mulungu. Mukuona?

253 Iwe ungakhoze bwanji kunena kuti, "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera," ndiye, ndipo nkubatizidwa mwa izo? Achikunja! Kulondola! Iwe unganene bwanji kuti ukumudziwa Yesu Khristu, Iye ndi Mawu, pamene, palibepo Lemba mu Baibulo, palibepo malo pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera"?

254 Ndipo inu—ndi inu anthu a Yesu yekha, mumangogwiritsa ntchito dzina la "Yesu" pa ubatizo! Ine pandekha ndikudziwana nawo a Yesu foro kapena faivi, mwiniwanga. Chotero inu mukuona chimene zipembedzo zanu zimakutsogoleraniko kuti mukalowe? Umenewo ndi mdima, kulongosola kwa Kaini, yemwe anabweretsa zipatso mmalo mwa magazi. Mukuona?

255 Koma vumbulutso limabwera kudzera mu Magazi, mwaona, kudzera mwa Yesu Khristu, Yemwe ali Magazi a Mulungu, Magazi olengedwa mu chiberekero cha Maria. Ndipo Paulo anamudziwa Iye mwa vumbulutso. Ndi momwe ife tikumudziwira Iye lero, ndi yokhayo njira yokha yomwe inu mungakhoze kumudziwira Iye. Osati kunena kuti, "Ine ndine wa Methodisti." Izo sizikutanthauza kanthu. "Ine ndine wa Baptisti." Izo sizikutanthauza kanthu. "Ine ndine wa Katolika." Izo sizikutanthauza kanthu. Koma mwa vumbulutso, kuti Mulungu wawulula Mawu kwa inu! Iye ndi Mawu. Ndipo Mawu, iwe ungadziwe bwanji kuti Iwo awululidwa, Iwo amadzikhala Okha moyo ndipo amadzifotokozera Okha kudzera mwa iwe. Oh!

256 Mipingo inaiwala kale vumbulutso lalikulu limenelo. Uko nkulondola. Vumbulutso la Choonadi, iwo anayiwala zimenezo. Iwo anapita ku . . .

257 Tsopano, pamene Luther anawuka, iye anali munthu wamkulu. Iye anali nalo vumbulutso la tsiku limenelo. Koma chinachitika ndi chiyani? Gulu la Maricky linadzalowa mmenemo, kumadzameta maphanke, monga ife tingazitchulire izo lero, ndi Mariketta, ndi onse a iwo, iwo ali nawo cha kumeneko. Ndi—ndi—ndipo, chinthu choyambirira inu mukudziwa, ziri pamenepo.

258 Kayankhulidwe kameneko. Ngati inu kokha—mukanangodziwa chiwerengero cha Baibulo, ndi kudziwa chimene *Elvis* kapena—kapena *Ricky* amatanthauza, kwa Lemba! Uh-huh. Basi monga, bwanji Yesu . . . Inu mukuti, "Palibe kanthu kwa izo, dzina lanu." Palibepo apo? Dzina limenelo likanakhoza kungobwera mu masiku otsiriza ano, kwa anthu a masiku otsiriza ano.

259 Chifukwa chiyani Yesu anasintha dzina la Abramu kukhala Abrahamu, kenako, Sarai kukhala Sarah? Chifukwa chiyani iye anamusintha Saulo kukhala Paulo? Chifukwa chiyani Iye anamusintha Simoni kukhala Petro, ndi zina zotero? Inu mwaona, ndithudi izo zimatanthauza chinachake.

260 Dzina limenelo silikanayankhulidwa mpaka tsiku lino. Ndi chifukwa chake ife tiri nacho chinthu cha ku gehena ichi chimene ife tiri nacho mu dziko lapansi lero, chifukwa cha zinthu zoterozo. Mtundu wonse wa anthu wasokonezedwa. Iwo—iwo unapita, mwaona, ndipo ndi chifukwa chake ziri chomwecho.

261 Zindikirani tsopano, iye anali wabwino, iye anali mmasiku ake, Luther, ndipo iye anali nalo vumbulutso; koma mwamsanga pamene iye anachoka, penyani chimene iwo anachita. Wesley anali nawo uthenga; penyani zimene iwo unachita. Achipentekoste akale oyambirira anali nawo uthenga; penyani chimene iwo anachita. Iwo anaika gulu la amuna pamodzi, basi chimodzimodzi monga chinthu chomwecho chimene . . .

262 Mulungu, mwa chisomo, anamtumizira Israeli Lawi la Moto, mneneri, nsembe, ndipo anadzisonyeza Yekha pakati pa iwo, ndipo anawatulutsa iwo kuchokera ku Igupto, kuwoloka Nyanja Zofiira. Ndipo iwo anafuna lamulo, kuti iwo akhoze kukhala nawo olemekezeka aakulu, iwo azikhoza kukhala ndi chinachake choti azichita mmenemo. Ndipo kodi iwo anachita chiyani? Iwo anasiyidwa mu chipululu kwa zaka forte, kuti aziyendayenda, ndipo palibe mmodzi wa bungwe limenelo anapita nkomwe kumeneko.

263 Kalebu ndi Yoswa, awiri okhawo amene anaima pamenepo ndipo anati, "Ife tiri okhoza kuti tilitenge ilo, kuti tiziyang'ana pa Mawu a Mulungu."

264 Mmodzi aliyense wa iwo anafera mu chipululu. Ndipo Yesu anati iwo anali atapita Mwamuyaya, kulondola, Iye atasonyeza kale madalitso Ake ndi mphamvu mu mibadwo yawo; monga Luther, Wesley, ndi ena otero. Anatero Iye?

Anati, "Makolo athu anadya mana mu chipululu."

265 Iye anati, "Ndipo iwo ali, mmodzi aliyense, anafa." Ndiko, kulekana Mwamuyaya ndi Mulungu. Mitembo yawo inawonongekera mchipululu. Mukuona? "Iwo anafa. Koma Ine ndine Mkate wa Moyo umene unachokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba." Iwo sankakhoza kuziwona izo. Iwo basi sakanakhoza kuziwona zimenezo.

266 Chabwino, mpingo unaiwala kale zimenezo. Iwo anavomereza uthenga waluntha, aluntha, umembala, chidziwitso, mmalo mwa vumbulutso la Choonadi cha Mawu.

267 Tsopano taonani apa, iwo amanena lero. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu anatituma ife kuti tipite mdziko lonse, ndi kukachiritsa odwala, ndi kukalalikira Uthenga, ndi kukatulutsa ziwanda? "Oh, oh, inde, ine ndikulingalira uko nkulondola, koma . . . " Inu mukuona?

268 Dona, poyankhula ndi ine tsiku lina, iye anati, "Chabwino, mipingo yonse ili mu chiyanjano."

269 Ine ndinati, "Palibe umodzi wa iyo uli mu chiyanjano ndi umzake." Pali Akatolika ayima apo. Ine ndinati, "Nanga bwanji inu? Ndinu wa Chimethodisti ndipo awo ndi Achikatolika, kodi inu muli mu chiyanjano ndi wina ndi mzake?" Ine ndinati, "Papa uyu anabwera kuti adzawayanjanitse iwo pamodzi, ndicho chinthu chabwino kwa anthu a mtundu umenewo."

270 Koma Mpingo wa Mulungu ulibe chochita ndi zimenezo, osati mpang'ono pomwe. Iwo unatuluka kuchokera ku mulu wonsewo. Uh-huh. Kulondola. Inde, bwana.

271 Inu mukufuna kuti muyanjanitse izo pamodzi, ndipo mmodzi amakhulupirira mu chinthu *chinachake* ndi chimzake; Amethodisti amatenga kukonkha, Abaptisti amatenga kumiza, ndipo awiri onsewo amakana Mzimu Woyera mu chidzalo

Chake cha mphamvu. Iwo anati, "Ife tinalandira Mzimu Woyera *pamene* ife tinakhulupirira."

272 Baibulo linati, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera *kuyambira* pamene inu munakhulupirira?" Pali kusiyana. Mukuona? Ndiko kulondola. Mukuona?

273 Ndipo iwo amati, "Ndife mpingo wa Katolika. Ife tinayamba molawirira. Ife tinachita *izi*." Amethodisti amati, "Ife maziko athu ndi Baibulo."

274 Yesu anati, "Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira." Tsopano kodi izo ziri kuti? Uh-huh. Mukuona? Eya. "Ntchito zimene ine ndikuzichita inu mudzazichita nanunso," cholengedwa chirichonse, munthu aliyense yemwe akhulupirira mwa Iye. Tsopano izo ziri kuti? Amenewo ndi Mawu Ake. "Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzalephera konse." Tsopano kodi izo ziri kuti? Mukuona? Oh, izo zimangosonyeza!

275 Ndi chiyani icho? Icho ndi chikhalidwe cha haibridi. Penyani kuno, inu mutenge njere ya chimanga yaikulu yomwe ili ya haibridi, ndipo inu mutenge chimanga cha haibridi icho, ndi chimanga chokongola. Koma inu muchibzale icho, kodi inu mumapeza chiyani? Phesi laling'ono limatulukira monga *chonchi,* ndipo limasanduka chikasu ndi kufera pansi. Umo ndi momwe chipembedzo chirichonse chimakhalira, pamene icho chiri cha haibridi, ndi mawu a munthu atasakanizidwa ndi Mawu a Mulungu. Icho chibwera mpaka ku zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo chimene Yesu ananena za kukhulupirira Mawu, ndipo iwo amasanduka achikasu, ndi kuti, "Ife sitingakhoze kuwalandira Iwo," ndi kubwerera mmbuyo.

276 Chimodzimodzi monga azondi ena onse aja anachitira pamene anawoloka ndi kukayang'ana pa Kenani. Iwo anabwera kumeneko ndi kumati, "Oh, ife tikuwoneka ngati ziwala pambali pa iwowo! Ife sitingakhoze kulimbana nawo iwo! Amaleki adzatero, onse awa, chimene iwo ati adzachite!" Ndipo iwo anabwerera mmbuyo.

277 Ndipo Kalebu ndi Yoswa, pokhala mtundu weniweni, ameni, ndi Mawu a Mulungu, anadziwa kuti Mulungu anati, "Ine ndakupatsani inu dziko limenelo." Iwo anati, "Ife tiri okhoza moposa kuti tilitenge ilo!"

278 Izo zimatengera kumene iwe unabadwirako. Ngati iwe ubadwa mwa Mawu a Mulungu, Mawu a Mulungu amakhala ndi uyambiriro mu Mpingo Wake. Ndicho chimene Iye anachifera. Ndicho cholinga Chake, kuti Iye adzakhoze kukhala wokhoza kupindula, kuti adzakhale nawo uyambiriro Wake ukugwira ntchito mu Mpingo Wake. Mulole Mawu a Mulungu aziwalapo, choyamba, ziribe kanthu momwe china chirichonse chikuwonekera. Ine sindikusamala ngati aluntha anena *izi, izo, zinazo,* izo ziribe kanthu kochita ndi Icho. Mawu a Mulungu

ananena chomwecho, ndipo ife tiri okhoza moposa kulitenga ilo!

279 "Ngati ine nditalalikira zimenezo mu tchalitchi changa," mtumiki anandiuzapo ine, anati, "Ine ndingakhale ndikulalikira kwa nsanamira foro mu tchalitchi."

280 Ine ndinati, "Ine ndingalalikire kwa zimenezo." Inde, bwana. Mawu a Mulungu ananena chomwecho. Ife tikhoza kuchita zimenezo. Mulungu anati tizichita zimenezo. Ameni!

281 Oh, eya, iwo amawiringulira kwa iwowokha pa izi. Mukuona? Ndi chifukwa chake iwo ali akhungu kwa Uthenga wa nthawi yotsiriza, masiku otsiriza ano, pamene Mulungu akuzitsimikizira Iyemwini. Iwo akuyesetsa kuti awuyike Iwo mu gulu la mtundu wina wa zamizimu, kapena zina, oh, (kodi ine ndingazitchule chiyani zimenezo?) zilubwelubwe, kapena chinachake pa dongosolo limenelo. Mwaona, iwo—iwo amayesa kuwupanga Iwo chinachake chimene Iwo usali.

282 Basi monga iwo anachitira pamene Iye anali kuno, pamene Yesu anali kuno, iwo ankamutcha Iye "Belezebule; wambwebwe," tsopano iwo akuti izo ziri mtundu wa kuwerenga maganizo. Mukuona? Pamene, iwo akudziwa kuti Iye ankakhoza kuima pamenepo ndi kuyang'ana pa anthu ndi kuzindikira zolingalira zawo zomwe zimene zinali mu mtima mwawo. Baibulo linanena chomwecho.

283 Chabwino, kodi Ahebri mutu wa 4, sanati, "Mawu a Mulungu ndi achangu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa-konsekonse, ndipo akhoza kuzindikira zolingalira zomwe za mmalingaliro"? Ndipo Iye anali Mawu amenewo. Ndipo pamene Mawu amenewo akhala uyambiriro mwa munthu, chinthu chomwecho chimachitika kachiwiri, pakuti iwo ndi Mawu! Ameni! . . . Muwone momwe inu mungaphunthwire pa izi kuyambira pano mpakana. Ndi zimenezo pamenepo zomveka mwangwiro. Mukuona? Chabwino.

284 Ndi chifukwa chake iwo ali akhungu, chimodzimodzi monga izo zinali mmasiku a Khristu ali pa dziko lapansi. Oh, mai! Iwo akumazandima mwanjira yomweyo. Iwo anati, "Iye ndi Belezebule. Bele- . . . " Iwo anawona kuti Iye ankakhoza kuchita izo, chotero iwo anati, "Iye ali basi . . . Iye anabadwa mwana wapathengo, ndi wokhala ngati munthu wosamvetsetseka. Iye wangokhala wogwidwa ndi mdierekezi wina. Iye—iye ndi Msamaria wa uko, ndipo iye ali ndi mdierekezi mwa iye. Ndi momwe iye amachitira izo."

285 Yesu anati, "Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha zimenezo," mwaona, kuwatcha Mawu a Mulungu, ntchito za Mulungu, mzimu woyipa. Iye anati, "Ine ndikukhululukirani inu chifukwa cha zimenezo. Koma tsiku lina Mzimu Woyera ukadzabwera, ndipo mawu amodzi mowutsutsa Iwo izo sizidzakhululukidwa konse, ngakhale mdziko lino

kapena mdziko liri nkudza, kapena tsiku lalikulu ilo. Izo sizidzakhululukidwa ayi." Chotero, inu mukuona, izo zinalembedwa mwachimvekere mu Lemba.

286 Chotero pamene anthu adzafika pa Tsiku limenelo, ziribe kanthu momwe aliri aluntha, ndi momwe chakulira chipembedzo chimene iwo alimo, izo ndi zoweruzidwa. Iwo ayenera kukhala ali! Iwo anachitira mwano Mzimu Woyera, powutcha Iwo "oyera-odzigudubuza" ndi chinachake chimzake chimene chinali ndi dzina losakoma, kapena chinachake chonga izo. Ndipo Mpingo wa Mulungu umayenera kuti uzipirira izo nthawi zonse.

287 Ngakhale Paulo, pamaso pa Agrippa, anati, "Mu njira imene izo zikutchedwa '*mpatuko*,'" chimene chimatanthauza "kupenga," "ndi momwe ine ndikumupembedzera Mulungu wa makolo athu." Sikolala wamkulu waluntha uja anafika pa malo amenewo, "mwa njira yomwe izo zimatchedwa 'mpatuko.'"

288 Chifukwa chiyani? Izo zinaululidwa kwa iye. Lawi la Moto lija litapachikika patsogolo pake, linati, "Ine ndine Yesu, Mulungu wamkulu yemwe anali mu chipululu muja ndi Mose. Ine ndine Iye, ndipo nkovuta kuti iwe uzimenyana ndi zisonga."

289 Ndiye Paulo ataima pamenepo, anadziwa kuti moyo unali pa ngozi, iye anati, "Momwe izo zikutchedwa 'mpatuko,' ndi momwe ine ndikumupembedzera Mulungu wa makolo athu." Izo zinkanenedwa chomwecho. Chifukwa izo zinaululidwa kwa iye chimene Choonadi chachikulu cha Khristu chinali.

Ndipo lero, anthu amati, "Ndi chipembedzo."

290 Ndi Yesu Khristu, Kubadwa kwatsopano, ataululidwa mwa inu, kuti Iye ali nawo uyambiriro, kuti Iye akhoze kumafotokozera Mawu Ake. Ndipo chirichonse chimene Iye anachilonjeza mmasiku otsiriza ano, Iye akhoza kuchibweretsa icho pochitika, kudzera mu Thupi Lake pamene Iye akugwira ntchito. Ameni! Ndizo basi ndendende Mawu a Mulungu akuwonetseredwa mthupi. Zindikirani. Chabwino.

291 Mofanana monga mmasiku a Khristu, Mulungu wagwirizira fungulo kwa vumbulutso ili la Khristu, Mwiniwake. Inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."— Mkonzi]. Masukulu azafioloje sangakhoze konse kulipeza Ilo. Yesu ananena chomwecho. Ngati inu mukufuna kuti muziwerenge izo tsopano, mu Mateyu Woyera 11:25 ndi 27. "Ine ndikukuthokozani Inu, O Atate, Mulungu wa miyamba ndi dziko lapansi, kuti Inu munazibisa izi kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo mwaziulula izo kwa makanda omwe angakhoze kuphunzira." Mukuona? Mukuona? Ine sindikusamala . . .

292 Tayang'anani pa iwo masikolala a tsiku limenelo, Ayuda amenewo, anthu abwino kwambiri, mabungwe awo a Afarisi, Asaduki, ndi Aherodia, ndi chirichonse chimene iwo angakhoze kukhala. Mukuona? Mabungwe awo onse aakulu, ndipo Yesu

anati, "Inu ndinu akhungu; inu mukutsogolera akhungu. Yesaya anayankhula bwino za inu, 'Inu muli nawo makutu, ndipo simungakhoze kumva; ndi maso, oti simungakhoze kupenya.' Chifukwa, Yesaya ananena izi mu Mzimu, chotero Mulungu wa Kumwamba wachititsa khungu maso anu. Inu mukuchita monga Eva anachitira, kuvomereza mbali yaluntha, ndipo osadziwa kanthu za Mzimu wa Mulungu. Chotero, kodi iwo onse sangagwere mu dzenje, awiri onsewo mtsogoleri ndi wakhungu, nayenso?" Mtsogoleri adzagwa limodzi ndi wakhungu, chifukwa iye ndi wakhungu nayenso. Mtsogoleri kugwa, ndizo wakhungu, akutsogolera wakhungu, iwo onse agwera mu dzenje.

293 Ndi Mulungu yekha akugwirizira fungulo ili! Iye anafotokozera chinthu chomwecho mu Lemba la mmbuyo kanthawi kapitako pamene ine ndinawerenga izo, pamene Iye anati, "Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine yani?"

294 Ndipo Petro anati, "Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo."

295 Iye anati, "Wodala ndiwe Simoni, mwana wa Yonasi. Thupi ndi mwazi sizinawululire konse izi kwa iwe. Atate Anga amene ali Kumwamba! Pa vumbulutso ili pano, lokhalo, Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga. Zipata za gehena sizidzagonjetsa konse pa iwo." Mukuona? Tsopano inu mukuona?

296 Chotero ndiye palibe sukulu, palibe azafioloje, palibe tiziphunzitso ta Baibulo pakati pa sukulu iliyonse, timene timadziwa chirichonse cha Izo. Iwo sangakhoze kudziwa kanthu za Izo. Ndi zosatheka kwa iwo kuti adziwe chirichonse cha izo. Mulungu anabisa zokhudzira, zodziwira Zimenezo, kwa aphunzitsi osankhidwa omwewo ndi china chirichonse.

297 Icho ndi chayekha, chomuchitikira munthu payekha, kuti Khristu wawululidwa kwa iwo.

298 Ndipo ngati iwe unena kuti, "Iye waululidwa kwa ine," ndiyeno Moyo umene Khristu ankawuwonetsera umu mu Baibulo, Moyo womwewo umene uli mwa Iye, sukudziwonetsera Wokha mwa iwe, ndiye kuti iwe wapeza vumbulutso lolakwika.

299 Ngati ine nditaika moyo wa dzungu mmoyo wa mtengo wa peyala, iwo ungamabale maungu. "Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo." Kulondola ndendende. Ndipo ngati choyamba...inu mukaika mtengo, nthambi ya manyumwa, ndipo iyo nkubala mulu wa manyumwa; mphukira yoyamba imene iwo uti utulutse, kubala manyumwa, yotsatira kubala mandimu, ndi ina yotsatira kubala mapeyala, yotsatira kubala maapulo, pali mtundu wina wa chikhalidwe chomezanitsidwa mmenemo, chimene chikudzibala moyo wake wake. Chipembedzo chirichonse chidzabala moyo wake wake. Koma ngati nthambi yapachiyambi ija idzayike konse mphukira ina, iyo ikanadzabala manyumwa monga iyo inachitira nthawi yoyamba.

300 Ndipo ngati Moyo—Moyo wa Yesu Khristu udzayika konse thupi lina la okhulupirira, ilo lidzabala chipatso chimene loyambalo linabala. Iwo adzalemba Bukhu la Machitidwe mmbuyo mwa ilo, chifukwa Ilo lidzakhala lofanana, Moyo wofanana. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Inu simungakhoze basi kuchoka kwa izo. Uwo ndi Moyo wa Khristu mwa inu, wabayidwira mwa inu, ndi Mzimu Woyera Iwoeni ukukhala Moyo Wake kudzera mwa inu.

301 "Atsogoleri akhungu kwa akhungu!" Zindikirani, Mulungu akugwirizira fungulo ili, yekha. Palibe wazafioloje angakhoze kukuuzani inu; Izo sizidziwika. Izo zinabisika kwa iwo. Iwo sadziwa kanthu za Izo.

302 Chotero masukulu, pamene inu munena kuti, "Ine ndiri ndi Ph., LL.D.," inu mukungopanga . . . Kwa ine, ndipo, ine ndikukhulupira, ndi kwa Mulungu ndi kwa wokhulupirira woona weniweni aliyense, izo zikutanthauza kuti inu basi mwatalikira utali wochuluka chomwecho, inu munangobwerera mmbuyo. Mulungu samadziwidwa ndi maphunziro. Iye samadziwika ndi momwe mungafotokozere Izo.

303 Mulungu amadziwika mophweka ndi vumbulutso la Yesu Khristu kwa munthu wosaphunzira kwambiri. Mukuona? Osati fioloje yanuyo. Ndi vumbulutso la Yesu Khristu. "Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga." Palibe mathanthwe ena amavomerezedwa, palibe zinthu zina zimavomerezedwa, palibe thanthwe lina la Chiroma, palibe thanthwe lina la Chiprotestanti, palibe sukulu ina, palibe kanthu kena, koma ndendende pa vumbulutso la Yesu Khristu kudzera mu Kubadwa kwatsopano. Iye amabadwira mmenemo, ndipo Iye amabayiramo Moyo Wake Womwe, ndipo moyo wanu umachokamo. Ndipo Moyo wa Khristu umadziwonetsera Wokha kudzera mwa inu, ndi mauyambiriro, kwa anthu; mwakuti iwo amawuwona Moyo womwewo, ndi ntchito, ndi zizindikiro, ndi zodabwitsa, zimene Iye ankachita, akuchita chinthu chomwecho kudzera mwa inu. Kunja kwa zimenezo, zina zonsezo sizimatchulidwako konse, nkomwe. Tapenyani vumbulutso lalikulu la Mulungu likufutukuka!

304 Pa kusowa kwa vumbulutso ili ndi chifukwa chake tiri nako kugawikana kosiyanasiyana kochuluka kwambiri pakati pathu, ndi zotonzana zochuluka kwambiri. Kugawikana kochuluka kwambiri pakati pathu, ndi chifukwa chakuti anthu akusowa vumbulutso limenelo. Mwaona, iwo akusowa vumbulutso limenelo, aphunzitsiwo.

305 Paulo, pambuyo pa vumbulutso lake lalikulu la Khristu, ananena, mu Akorinto Woyamba mutu wa 2. Mutsimikize kuti mukawerenge zimenezo pamene inu mukuzilemba pamenepo. Penyani! Oh! Iye anati, "Ine sindinabwere konse kwa inu ndi nzeru." Tayang'anani pa munthu uyo yemwe anali nazo nzeru,

kapena, tayang'anani pa munthu uyo yemwe anali ndi usikolala, "Ine sindinabwere kwa inu ndi mawu a mtundu umenewo." Akorinto Woyamba, mutu wa 2 wa Akorinto Woyamba. Oh, ine ndikukhumba . . .

306 Chabwino, tiyeni tingowerenga izo. Motani . . . Kodi inu mungakhoze kupirira miniti ndipo tiyeni tingowerenga ndime yokha kapena ziwiri? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ine ndikungofuna kuti ndiwerenge izo kuchitira kuti—inu musati- . . . Izo zingawapangitse ngakhale anthu pa tepi kuti atsegule kwa izo, mulimonse, ndiwapatse iwo mwayi.

307 Akorinto Woyamba, mutu wa 2. Mvetserani kwa mtumwi wamkulu uyu pano, Paulo, wantchito waluntha wa Mulungu. Tiyeni tiyang'ane apa.

> . . . ine, Paulo, *pamene ine* ndinabwera *kwa inu, sindinabwere ndi kuthyathyalika kwa mayankhulidwe . . . a nzeru, kufotokozera* kwa *inu umboni wa Mulungu*. Ine sindinanene konse ine—ndine Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti*. Mukuona?
>
> *Pakuti ine* ndiri *wotsimikiza kuti ndisadziwe chirichonse pakati panu, kupatula Yesu Khristu, ndi iye wopachikidwayo.*
>
> *Ndipo ine ndinali ndi inu mu chifowoko, ndi mmantha, ndi mu kunjenjemera kochuluka.*
>
> *. . . kuyankhula kwanga ndi—ndipo* kulangiza *kwanga sikunali ndi mawu okopa a luntha la munthu, koma mwa chiwonetsero cha Mzimu ndi* mphamvu . . . *cha mphamvu.*

308 Pamenepo, onani, umenewo ndiwo Uthenga. Mukuona? Yesu anati, "Pitani inu mdziko lonse ndipo kalalikireni Uthenga." Sananene kuti, "Pitani mukaphunzitse." Iye anati, "Pitani mukalalikire." Mwa kuyankhula kwina, "Kawonetsereni mphamvu, ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo." Kuphunzitsa kokha sikumachita izo. Izo zimatengera Mzimu weniweni Pawokha kuwonetsera zizindikiro izi. Mukuona? Mvetserani kwa izi.

> *Kuti chikhulupiriro chanu chisati chiziyima mu nzeru za munthu, koma mu mphamvu ya Mulungu.*

309 Oh, mai! Onani, kuti zimusinthe munthu! Osati mu zimene ine ndingakhoze kuzifotokoza mophotchola, ndi kuti, "Iye sali yemweyo," pamene Iye ali yemweyo. Ngati ine ndingachite zimenezo, izo zisonyeza, kwa ine, izo—izo . . . Ndithudi, munthu akandiuza ine zimenezo, zingasonyeze kwa ine kuti iye alibe vumbulutso, vumbulutso lofutukuka patatu la Mulungu. Mukuona? Tsopano, ndipo . . .

> *Momwe ndinali* mwa chifooko . . . *pakati pa* inu *amene muli angwiro: komabe osati* ndi *nzeru ya mdziko,* koma

*ya akalonga a dziko lino, amene akufika posakhala kanthu:*

*Koma ife tikuyankhula nzeru za Mulungu mu*. . . *chinsinsi,* (mwaona, chinsinsi chofutukuka patatu cha Mulungu) *ngakhale nzeru zobisika, zimene Mulungu anazikonzeratu lisanakhalepo dziko kwa ulemelero wathu:*

*Chimene palibe wina wa akalonga a dziko lino ankazidziwa:* palibe wa ansembe, rebbi—marabbi. . . (mundikhululukire ine). . . kapena chirichonse, anadziwa chirichonse cha izo; *pakuti akanati iwo azidziwe izo, iwo sakanati amupachike* ayi *Ambuye wa ulemelero*.

310 Inu mukuti, "Inu mukulakwitsa za marabbi ndi alaliki pamenepo." Ndani anamupachika Iye? Uh-huh.

311 Oh, pang'ono ndi pang'ono ndi pang'ono, ife tikhoza kumapita. Kumawerenga izo, onani, kupitiriza, tisunge nthawi, chifukwa ife tangotsala ndi. . . Sitinachedwe panobe, koma ife tangotsala ndi zochuluka pano zoti tinene ngati Ambuye ati atithandize ife. Tsopano, posowa izi, tsopano. . .

312 Ndipo Paulo, mwamuna waluntha wamkulu uyu, sanayesere konse kuti afotokoze mbalume zake zazikulu zafioloje pa anthu. Iye modzichepetsa anawavomereza Mawu a Ambuye, ndipo iye ankawakhala moyo Mawu mwakuti Iwo ankafotokozeka kudzera mwa iye. Iye ankakhala moyo—mwaumulungu chomwecho mpaka iwo ankamuwona Yesu Khristu mwa iye, mochuluka kwambiri, mpaka iwo ankafuna mpango wake, kuti awutenge iwo ndi kukawuyika iwo pa odwala. Ndi umenewo Moyo wa Khristu.

313 Tsopano penyani ena amati, "Oh, chabwino, inu mukuona, Eliya anachita zimenezo, nthawi yaitali kalelo, anagoneka ndodo yake; koma, oh, amenewo anali masiku a Eliya." Tsopano, dziko linkaganiza zimenezo. Ansembe aluntha ndi zinthu, ndi mipingo ya tsiku limenelo, inkaganiza zimenezo.

314 Koma kwa okhulupirira amenewo, iwo ankadziwa mosiyana. Iwo ankaliwona vumbulutso la Khristu limene linali mwa Eliya, chinthu chomwecho chinali mwa Paulo, akufotokozera mtundu womwewo wa Moyo, chifukwa iye anali mneneri. Mukuona? Iye amaneneratu zinthu zimene zimadzachitika ndendende mwanjira yomwe izo zimachitikira, ndipo iwo ankadziwa kuti icho chinali chizindikiritso cha Mulungu cha mneneri. Ndipo iwo amadziwa kuti iye anali mneneri wa Mulungu. Iwe sukanakhoza kuwagwedeza iwo kwa icho, nkomwe. Ngakhale pamene iwo anamuwona Petro akuneneratu zinthu zimenezo zimene zinadzafika pochitika, iwo anati, "Mungolola mthunzi wake udutse pa ine." Ameni! Umenewo ndiwo Mpingo. Awo

ndi omwe akuzikhulupirira izo. Inde, bwana. Izo zinaululidwa ndi . . .

315 Nchifukwa chiyani Paulo anati, "Chifukwa ine—ine ndiri ndi Ph., LL.D., zina zotero, iwo andikhulupirira ine? Ayi," iye anati, "Ine ndinaiwala zinthu zonsezo, nzeru ya munthu," anati, "ndinachita kufa, ndipo ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake, ndicho chimene ine ndikubwerapo kwa inu, ndi chiwonetsero cha mphamvu ya Mulungu"?

316 Kodi chimenecho chinali chiyani? Kumupangitsa Yesu Khristu kukhala yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ntchito zomwezo zimene Yesu ankachita, Paulo amachita zomwezo. Ndipo iwo anamuwona Mulungu, Atate wamkulu amene anali atawonetsera mu chitsamba chonyeka, anali atawonetsera Izo kwa Paulo, ndipo apa Izo zinali zikuwonetseredwa.

317 Ndipo Iye ali yemweyo mu m'badwo uliwonse. Makhalidwe a Mulungu ofutukuka patatu, "dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Chiyani? Muwomboli; mu Mpingo Wake; mauyambiriro mu Ufumu wakudza. Ameni! Inu mukuziwona zimenezo? Mwangwiro basi monga izo zingakhoze kukhalira!

318 Oh, zindikirani! Mzimu Woyera ndiwo Mvumbulutsi yekhayo wa vumbulutso Lauzimu la Khristu. Palibe sukulu imene ingakhoze kuchita zimenezo. Palibe sikolala angakhoze kuchita zimenezo. Palibe munthu, kaya ndi wophunzira chotani, wazaumulungu chotani, kapena china chirichonse, palibe munthu yemwe angakhoze kuchita zimenezo.

319 Ine ndikhoza kuluma mwamphamvu apa. Ndi angati ali Akhristu, obadwa mwatsopano; kwezani mmwamba manja anu, odzazidwa ndi Mzimu Woyera? Chabwino. Pano ife tikupita ndiye. Chabwino. Zindikirani.

320 Ndipo Iye adzachita izo kwa okonzedweratu okha. Ndizo ndendende. "Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza, ndipo palibe munthu angakhoze kudza kupatula Atate atamupereka iye kwa Ine choyamba." Mukuona?

321 Tayang'anani pa ansembe amenewo, akuti, "Munthu uyu ndi Belezebule. Iye ndi wambwebwe. Iye ndi mdierekezi."

322 Ndipo mkazi wachikulire wamng'ono uja akuyenda mozungulira kumeneko, akukhala ndi amuna sikisi; iye anali atakhala ndi faivi, ndipo anali ndi wasikisi panthawiyo. Ndipo Yesu anati, "Pita ukamutenge mwamuna wako, ubwere kuno."

Iye anati, "Ine ndiribe mwamuna."

323 Anati, "Inde, iwe uli nawo sikisi. Iwe wakhalapo nawo faivi, ndipo mmodzi yemwe iwe ukukhala naye tsopano si mwamuna wako."

Iye anati, "Bwana!" Chiyani? Kuwala kumeneko kunagunda Mbewu imeneyo.

324 Pamene Iko kunawagunda ansembe aja, iwo anati, “Munthu uyu ndi wambwebwe.” Mwaona, munalibemo Moyo mmenemo. Ahaibridi, kungofika mpaka pa bungwe, koma nkufa kuyambira pamenepo mpakana.

325 Koma mkazi uyu sanali wa haibridi. Anati, “Bwana, ine ndazindikira!” Ine ndikukhoza kuwona maso ake aakulu okongola akuwala monga chomwecho, misozi ikuyenderera pa matsaya ake. Anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri. Ine ndikuyembekezera Mesiya. Ndipo pamene Mesiya ameneyo adzadza, Iye adzachita chinthu chomwechi ichi. Iye adzatiuza ife zinthu zimenezi.”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

326 O Ambuye! Iye anasiya mtsuko wake. “Ali kuno Iye! Bwerani, mudzamuwone Mwamuna yemwe wandiuza ine zinthu.” Chinali chiyani cimenecho? Kuwala kuja kunagunda Mbewu imeneyo. Moyo umenewo unali mmenemo. Iwo unatulukira.

Chinthu chomwecho lero!

327 Koma wazafioloje adzanena kuti, “Tsopano dikirani miniti yokha. Ine ndikafufuza ngati *Wakuti-ndi-wakuti*, Abusa a Moody anatero, kapena . . . ”

328 Abusa a Moody ali ndi chiyani chochita ndi izi, tsiku lino? Abusa a Moody anakhala moyo mu tsiku lawo, koma osati tsopano. Ndithudi. Luther anakhala moyo mu tsiku lake, koma osati mu tsiku la Wesley. Wesley anakhala moyo mu tsiku lake, osati mu tsiku la Pentekoste. Pentekoste anakhala moyo mu tsiku lawo, koma iwo ali mtunda wautali kudzafika kwa Ichi mu ora lino. Ife tiri mu ora lotsiriza. Zedidi.

329 Mabungwe awo, ndi ziphakasa, zikutsimikizira kuti Iwo sali mmenemo. Mawu sanayambe atsimikiziridwapo molondola; mu mphamvu Yake yokha. Mbewu, zipembedzo . . . Ndipo iwo akanadzapanga chipembedzo, ndiye nkudzayika maudzu a mbewu zakale za bwamtete izo mkati limodzi ndi tirigu weniweni uyo; kuferatu pomwepo. Mbewu inapita mmaudzu a bwamtete, kulondola, minga zobiriwira ndi kamfiti, uh-huh, mwaona, zinabwerera mmbuyo kwa izo. Iye anafera pomwepo. Ndiye iwo anawupha mundawo ndi kuyambanso kachiwiri, anabzala Mbewu zina zenizeni, ndipo zina za izo zinatulukira, izo zinatsamwitsa Izo.

330 Komano, Mulungu anati, mmasiku otsiriza ano Iye akanati adzawabweretse anthu otsukidwa mu Magazi Ake, ndipo iwo anakonzedweratu kuti adzakhalepo kumeneko. Iwo ayenera kuti akakhalepo kumeneko. Mulungu ananena chomwecho. Ndipo Iwo akanati adzaulule . . . Ndipo chizindikiro kumene, “Ine ndidza- . . . ” Malaki 4, ndi zomwe iye akanati adzachite, “kubwezeretsa kachiwiri,” kubweretsanso, mmasiku otsiriza, zinthu zazikulu izi zimene Iye analonjeza, izo zikanati

zidzabweretse vumbulutso. Ndi chiyani akuti...Kodi iye akudzachita chiyani, Malaki 4? Anali woti adzabwezeretse Chikhulupiriro cha atate, kwa ana. Mukuona? Ndiko kulondola, kuti adzabwezeretse chinthu chomwecho, Lawi la Moto lomwelo, kudzakhala powonekera; zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo, Yesu yemweyo; kumupanga Iye yemweyo, kumulalikira Iye yemweyo, kumutsimikizira Iye yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

331 "Ine ndidzabwezeretsa," atero Ambuye, "zaka zonse zimene mbozi ya Methodisti, ndi mbozi ya anoni, ndi Baptisti, ndi Katolika; ndi mbozi zonse izo zinadya icho—Chikhulupiriro chimenecho mpaka pansi," mpaka icho nkukhala chitsa cha chipembedzo pamene palibe mbewu zimene zatsalira mmenemo. "Koma ine ndidzabwezeretsa kachiwiri," atero Ambuye, "zaka zonse." Chiyani? "Zizindikiro zonse ndi zodabwitsa zimene iwo azisiya. Ine ndidzazitenga izo nkuzibwezeretsanso kwa Mtengo wapachiyambi uja kachiwiri, ndipo ine ndidzazibwezeretsa Izo," atero Ambuye. Mneneri ameneyo anali mneneri wotsimikiziridwa. Mawu ake ayenera kufika pochitika. Ameni.

332 Mzimu Woyera, wokha, ndiwo Wowulula wa vumbulutso Laumulungu la Khristu, ndipo izo zakhala zikuchitika mmibadwo yonse. Kumbukirani, mibadwo yonse! Kodi Mawu a Ambuye ankabwera kwa ndani? Mneneri, yekha. Ndiko kulondola. Ndi kulondola uko? Ndipo mneneri ankayenera kuti atsimikiziridwe, choyamba. Osati chifukwa iye wanena kuti iye ndi mneneri; chifukwa iye anabadwa ali mneneri, ndipo anatsimikiziridwa kuti ndi mneneri, ndipo chirichonse chimene iye anena chikamakhala ndendende pa Mawu ndipo nkufika pomachitika, ndiye china chirichonse chisiyeni chizipita. Mukuona? Izo zinali, Mawu a Ambuye ankabwera mwa Mzimu Woyera wokha. Baibulo linati, "Amuna akale, ankasunthidwa ndi Mzimu Woyera, mwaona, ankalemba Mawu."

333 Taonani. Yohane M'batizi sakanamudziwa nkomwe Yesu ngati ukanati usakhale Mzimu Woyera utamulozera Iye. Uko nkulondola? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

334 Yohane M'batizi, mneneri wamkulu uja yemwe anatulukira, ndipo anati, "Alipo Mmodzi waima pakati panu pakali pano. Ndipo Munthu wamba waima pano penapake, ameneyo ndi Mwanawankhosa wa Mulungu." Yohane anati, "Ndiye ine ndinachitira umboni. Ine ndikuchitira umboni. Ine ndinawona Mzimu wa Mulungu, Mzimu Woyera, ukutsika kuchokera Kumwamba monga nkhunda, ndipo Iwo unapita pa Iye. Ndipo Liwu linati, 'Uyu ndiye Mwana Wanga wokondedwa mwa Yemwe Ine ndiri wokondweretsedwa.'"

Kodi chinali chiyani icho? Mzimu Woyera unati, "Ine ndimulozera Iye."

335 Ndiyo njira yokhayo yomwe iwe ungamudziwire Iye lero, njira yokhayo yomwe iwe ungapezere vumbulutso lofutukuka patatu la Mulungu, ndi mwa Mzimu Woyera. Ndipo njira yokhayo yomwe izo zingakhoze kukhalira, ndi kuti iwe unakonzedweratu kuti udzaziwone izo. Ngati izo sizitero, iwe sudzaziwona konse izo. Ngati iwe sunakonzedweretu kuti udzaziwone izo, iwe sudzaziwona konse izo; chifukwa Kuwala kumeneko kukhoza kuthwanima ndipo iwe ukhoza kuchokapo ndi kumakaziseka izo, ndi kukazifotokoza izo mophotchola, pogwiritsa ntchito kumvetsetsa kwina kwaluntha. Pamene Mulungu yemweyo, Mwiniwake, akudziwonetsera Yekha ndi kumazitsimikizira izo, mwaona, koma, ngati izo siziri pa iwe kuti uziwone izo, inu simudzaziwona izo.

336 Mulungu sanangoti, “Ine ndidzamusankha mmodzi *uyu,* ndi kumusankha mmodzi *uyo,*” koma Iye anadziwa mwa Kwake. . . Chifukwa chimene Iye akanakhoza kukonzeratu, chifukwa Iye ndi wopandamalire, ndipo Iye—Iye amadziwa chirichonse. . . Iye ndi wopandamalire, chotero ndiye Iye anadziwa chirichonse. Iye anadziwa mapeto, ndipo amakhoza kudziwa mapeto kuchokera ku chiyambi. Iye ndi Mulungu. Ngati Iye sangakhoze kuzichita izo, Iye si Mulungu. Inde, bwana. Iye ndi wopandamalire. Chabwino.

337 Yohane sakanati amudziwe nkomwe Iye, ayi, bwana, ukanati Mzimu Woyera usamulozere. Mukuona momwe Mulungu amabisira chinsinsi Chake kwa apamwamba, ophunzira ndi chirichonse? Penyani, mmodzi aliyense wa anthu amenewo. . . mu kuphweka amaululira izo kwa yemwe Iye anamukonzeratu kuti adzaziwone izo. Penyani apa! Ena ataima pafupi ndipo sanaiwone nkomwe nkhunda, iwo sanamve nkomwe Liwu lirilonse, pakuti izo zinali zitangotumizidwira kwa Mbewu yokonzedweratu imeneyo. Kukonzedweratu! Ndithudi, anali atakonzedweratu!

338 Bwanji, Yesaya, zaka seveni handiredi ndi thwelovu Iye asanabadwe, mu Mzimu, anakwera pamwamba pa zomverera zaumunthu izi, ndipo anati, “Pali Liwu la wina wofuula mchipululu, ‘Konzani njira ya Ambuye, ndipo pangani Yake. . .’”

339 Ndiye, ngati Yesaya akanakhoza kuwona izo, kodi Malaki sakanakhoza kuchiwona chinthu chomwecho za mneneri wotsiriza wokonzedweratu, kusindikiza kwa aneneri onse a Chipangano Chakale, wamkulu uja. . . mneneri wamkulu uja ataima pamapeto a m’badwo? Mukuona? Iye akunena kuti anakonzedweratu. Ndithudi, iye anatero. Malaki anamuwona iye, aponso.

340 Yesu anati, “Ngati inu mungakhoze kuzilandira izo, uyu ndi iye yemwe ananenedwera, ‘Ine ndituma mtumiki Wanga patsogolo pa nkhope Yanga,’ Malaki 3, ‘kuti adzakonzeketsere

njira patsogolo Panga.'" Mukuona? Zedi, iye anakonzedweratu kuti adzawone uthenga umenewo. Nzosadabwitsa iye amakhoza kuyang'ana patali ndi kuyiwona Nkhunda imeneyo ikutsika, Kuwala kuja kumene kunali mchipululu ndi Israeli, kukubwera, kumasunthira pansi.

341 Mulungu Mwiniwake, akuti, "Uyu ndiye Mwana Wanga wokondedwa mwa Yemwe Ine ndikukondwera kuti ndizikhalamo." Mulungu ndi munthu kudzakhala Mmodzi.

342 "Ine ndikuchitira umboni," Yohane anati, "Ine ndinamuwona Iye, wobalidwa yekhayo wa Atate. Ine ndine mboni wa zimenezo." Ameni!

343 Ndi zimenezotu. Kuphweka! Ndi mlaliki wokalamba, bambo ake; bambo ake anali wazafioloje wamkulu, inu mukudziwa, iye anabwera kuchokera ku sukulu. Zinkawoneka ngati iye akanabwerera ku chipembedzo cha abambo ake. Icho sichikanati chidzakhale chifuniro cha Mulungu.

344 Pamene Mulungu anamukhudza iye pa kubadwa kwake mmbuyo umo, ndipo iye analandira Mzimu Woyera miyezi itatu iye asanabadwe. Inde, bwana. Pamene Maria anapita kumeneko, ndipo Yohane wamng'ono anali usinkhu wa miyezi sikisi, mu chiberekero cha amayi ake, ndipo anali asanati nkomwe... Akatumba aang'ono awo anali asanasunthe nkomwe apobe. Ndipo Maria ankachita mantha... Akatumba aang'onowo anali akukula, koma iye sanali kumverera moyo uliwonse, Elizabeti, mayi ake, kani. Ndipo pamene Maria anabwera kumeneko ndi kudzamugwira iye, ndi kudzamukumbatira iye, anaika mikono yake, anaika manja ake pa iye. Mukuona? Ndipo anati, "Mulungu wayankhula ndi ine, ndipo ine ndikhala ndi mwana, nanenso."

"Kodi iwe ndi Yosefe mwakwatirana?"

"Ayi."

"Maria, izi zingakhale motani?"

345 "Mzimu Woyera udzandiphimba ine, ndipo pamenepo adzalengedwa mwa ine. Ndipo ine ndidzamutcha Dzina Lake 'Yesu.' Iye adzakhala Mwana wa Mulungu."

346 Ndipo mwamsanga pamene mawu oti 'Yesu' anayankhulidwa, Yohane wamng'ono anayamba kulumpha, ndi kufuula, ndi kulumpha kuzungulira mu chiberekero cha amayi ake.

347 Iye anati, "Wodala akhale Ambuye Mulungu! Pakuti akuchokera kuti amake a Ambuye wanga?" Amake a Ambuye wanga! Oh, mai! "Akuchokera kuti amake a Ambuye wanga? Pakuti, mwamsanga pamene kulonjera kwanu kunabwera mmakutu anga, mwana wanga analumpha mu chiberekero, mwa chimwemwe."

348 Nzosadabwitsa iye sanafune seminare iliyonse, chinachake choti chimulowetse iye mu chiphunzitso ndi chinachake, chimzake. Iye anali ndi ntchito yofunikira. Iye anali mwamuna wa mchipululu, anapita ku chipululu ndipo anakayembekezera. Mulungu anamuwuza iye kunja uko, anati, tsopano, ndi kuwulula kwa iye. Oh, ndi limenelo vumbulutso lanu kachiwiri! "Ndipo Ine ndikuuza iwe Yemwe Iye ali. Iwe ndi mneneri. Mawu ali kwa iwe. Iwe ukudziwa yemwe iwe uli. Iwe uyenera kuti ubwere." Izo zikuyankha funso la Lamlungu lapitali. Mukuona? "Iwe ukudziwa yemwe iwe uli, Yohane. Udzikhalitse wekha chete; usati unene kanthu. Pita kunja uko. Ndipo pamene iwe ukamuwone Mmodzi uyu, pakakhala pali chizindikiro chikubwera kuchokera Kumwamba, monga Kuwala, nkhunda idzabwera kumeneko. Ameneyo adzakhala Iye pamene iwe udzamuwone Iye."

349 Ndi chifukwa chake, pamene Yesu ankatuluka mmadzi, Yohane anayang'ana mokweza ndipo iye anayiwona nkhunda ija ikutsikira pansi, iye anati, "Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu! Ndi Uyo pamenepo! Iye ndi Mmodzi Yemwe ati adzachotse tchimo la mdziko."

350 Yesu anayenda molunjika mmadzimo, kupita kwa iye. Maso awiri amenewo a Yohane anakomana ndi maso awiri awo a Yesu. Iwo anali asuwani achiwiri, mwa thupi. Maria ndi Elizabeti anali asuwani oyamba. Maso awo anagundana wina ndi mzake. Pamenepo panali Mulungu ndi mneneri Wake, ameni, ataima pamenepo.

351 Yohane anati, "Ine ndikusowa kuti ndibatizidwe ndi Inu. Bwanji Inu mukubwera kwa ine?"

352 Yesu anati, "Balola kuti izo zikhale chomwecho tsopano, koma, kumbukira, kuti tikuyenera ife kuti tikwaniritse chirungamo chonse."

353 Nchifukwa chiyani Yohane anachita zimenezo? Chifukwa Iye anali Nsembe. Yohane anali mneneri, iye ankadziwa; ndipo Nsembe imayenera kuti itsukidwe Iyo isanati iperekedwe. Oh! Oh! Ndipo iye anamulolera Iye, ndipo iye anamubatiza Iye.

354 Ndipo pamene iye anatero, taonani, Miyamba munatseguka, oh, mai, ndipo nkhunda ija inatsikira pansi pa Iye, ndipo Liwu linati, "Uyu ndiye Mwana Wanga wokondedwa mwa Yemwe Ine ndikukondwera kukhalamo." King James amati "mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhalamo." Chotero izo zangokhala mwanjira iliyonse yomwe iwe ukufuna kuzitembenuzira izo, chinthu chofanana, "kukhalamo," kapena . . . "Uyu ndi Mwana Wanga wokondedwa mwa Yemwe Ine ndikondwera kukhala," kapena, "kuti ndizikhalamo," mulimonse momwe inu mukufuna kuti munenere izo, ndi chinthu chomwecho. Chabwino.

355 Ife tikuwona ndiye izo zinaululidwa kwa iye. Ena ataima pamenepo sanamve kanthu za zimenezo. Mzimu Woyera, wokha, umawulula izo.

356 Zofanana pamene Iye akudziulula Yekha kwa Paulo, Mbewu ina yokonzedweratu.

357 Uko kunali Paulo akuyendayenda, iye mwina akanati, "Ngati ndikangolipeza gulu limenelo, ine ndikawakhadzula iwo mzidutswa, chifukwa ndine Dokotala Saulo. Ine ndinabwera pansi pa Gamalieli. Ine ndinabwera kuchokera ku Moody Bible. . ." kapena inayake, mukuona. "Ine, ndine sikolala. Ine ndikudziwa zimene ine ndikukamba. Ine ndikalikhadzula mzidutswa gulu ilo la oyera odzigudubuza. Ndipo ine ndikukuuzani inu, bambo aakulu oyera, inu mungondipatsa ine chilolezo kuti ndipite kumusi uko, ndipo ine ndikammanga wina aliyense wa opanga phokoso amenewo kumusi uko. Chinthu chonse ichi cha machiritso Auzimu, ife tikaziletsa izo."

Anaika izo mthumba lake, anati, "Ine ndiri pa njira yanga wa kumeneko."

358 Ndipo tsiku limenelo, mai, pafupifupi leveni koloko masana, ku—Kuwala kunawalira mu nkhope yake, ndipo iye anagwera pansi.

359 Bwanji? Iye anali Mbewu yokonzedweratu. Mulungu anati, "Ine ndamusankha iye. Eya. Ndipo ine ndikamusonyeza iye zinthu zazikulu zomwe iye azunzike nazo chifukwa cha Dzina Langa. Ine ndimutumiza iye kwa Amitundu, ndi kukamuchititsa iye manyazi mwanjira iliyonse imene ingakhoze kukhalapo—kuti achititsidwe manyazi, komabe iye akatenga Dzina Langa."

360 Paulo anapita kumeneko, ndiye, mpaka iye atafika podula zinthu zake zonse zachipembedzo mwa iye, uko kuseri kwa chipululu, kwa zaka zitatu ndi theka. Kumusi uko mu Arabi, mpaka iye anaphunzira Mawu, ndipo Mawu anasanduka iye. Ndipo iye anadzakhala wamndende; apa iye anabwereranso mu unyolo wa chikondi! "Zondichitikira zanga zonse za ku seminare zatha! Ndine wamndende kwa Yesu Khristu. Ameni! Filimoni, m'bale wanga, ine ndine wamndende wa Yesu Khristu. Ine ndikhoza kungoyankhula ndi kunena zimene Iye andiuza ine."

361 Mulungu akusowa amndende lero omwe mungadziyike nokha mu undende ku chifuniro Chake, ku Mawu Ake.

362 Ndicho chimene Paulo anali. Ziribe kanthu kuchuluka kwa luntha lomwe analiphunzira, iye anali atamudziwa Mulungu mwa vumbulutso. Inde, bwana. Aluntha anapita njira yonse kutali kwa chochitikacho pamenepo, pamene vumbulutso linabwera; chimene, pa thanthwelo Mpingo unamangidwapo. Inde, bwana. Zindikirani, iye anali Mbewu yokonzedweratu.

363 Mzimu Woyera, basi, umakusonyeza iwe Yemwe Iye ali. Palibepo munthu; iwo adzakupangani inu "Atate, Mwana, ndi

Mzimu Woyera," ndi china chirichonse, kunja kwa zimenezo. Mukuona? Koma Mzimu Woyera udzamuwulula Iye monga Ambuye Mulungu wa Kumwamba anawonetseredwa, kuti izo ziri, oh, Iye!

364 Tsopano zindikirani. Osati aneneri, osati mafumu, osati kanthu kalikonse; koma apa, kwa nthawi yoyamba, Mulungu anawululidwa mwa Khristu, mwa chidzalo cha Umulungu mthupi, mu mnofu wa munthu. Ilo ndiro vumbulutso. Oh, mai! Ndikuimbirani inu ndime tsopano:

> Mafuko akusweka, Israeli akuwuka, (Kodi akutero?)
> Zizindikiro zimene aneneri ananeneratu;
> Amitundu (mpingo mu chipembedzo,) masiku awo atha, ndi zowopsya zachuluka;
> "Bwererani, O omwazika, kwanu." (Inu mwathamangitsidwa kwa iwo.)
>
> Tsiku la chiwombolo layandikira,
> Mitima ya amuna ikulephera mwa mantha;

365 Nthabwala zawo zonse za Hollywood sizikuphimba zimenezo. Monga mnyamata wamng'ono akuliza muluzu, akudutsa cha kumanda usiku. Mukuona?

> Dzazidwani ndi Mzimu, nyali zanu muzikonze ziwale,
> Yang'anani mmwamba! Chiwombolo chanu chayandikira.
>
> Aneneri abodza akunama, Mawu a Mulungu akuwakana,
> Kuti Yesu Khristu ndi Mulungu wathu; (Ndiko kulondola.)
> M'badwo uwu ukukana vumbulutso la Mulungu,
> Koma ife tikuyenda komwe atumwi anayendako.
>
> Tsiku la chiwombolo layandikira,
> Mitima ya amuna ikulephera mwa mantha;
> Dzazidwani ndi Mzimu, nyali zanu muzikonze ziwale,
> Yang'anani mmwamba! Chiwombolo chanu chayandikira.

366 Pezani vumbulutso, m'bale. M'badwo uno, ukukana vumbulutso la Mulungu! Mukuona? Aneneri abodza akuchita zimenezo. "Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo." Iwo ali—iwo ndi haibridi. Iwo abalidwira mu bungwe; mmalo mwa Mawu a Mulungu, vumbulutso la Mulungu akudziulula Yekha kupyolera mwa Khristu, Yemwe ali Mawu. Oh, mai!

367 Ife tikanakhoza kuimira apa, koma ngati . . . kudzazitenganso pamene ine ndidzabwerereneso, ngati inu mukufuna kutero. Tsopano pali . . . Inu mukufuna tipitirire, izo ziri ndi inu. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino. Pang'ono chabe . . . Ine ndifulumira, chotero, koma nditenga nthawi yokwanira kuti inu . . . Inu mukakhale nayo nthawi ina yopuma, zikatha izi. Chabwino.

Zofanana, zindikirani, Mbewu yokonzedweratu imeneyo!

368 Mzimu Woyera, wokha, umakusonyezani inu Yemwe Iye ali; palibe aneneri, kapena mafumu Ake. Ndipo pano Mulungu akuwonetseredwa mthupi. Pano pali chidzalo. Iye akuwululidwa mwathunthu ndipo akupangidwa kudziwika kwa dziko lapansi. Oh, mai!

369 Tayang'anani pa Phiri la Chiwalitsiro, pamene umboni wa Mulungu Mwiniwake, "Uyu ndiye Mwana Wanga wokondedwa. Mvereni inu Iye!" Apo panaima Mose akuimira lamulo. Apo panaima Eliya akuimira aneneri. Koma Iye . . . Iwo anapita kale, ndipo Iye anati, "Uyu ndiye Mwana Wanga wokondedwa. Mvereni Iye!" Panali atatu anaimiridwa pamenepo; lamulo, aneneri, ndi Mo- . . . ndi Khristu. Ndipo Iye anati, "*Uyu* ndiye Iye." Mulungu, mwathunthu; osati kuwonetseredwa mwa aneneri, osati kuwonetseredwa mwa lamulo; koma kuwonetseredwa mwa Khristu, Iye ali.

370 Khristu ndi yemwe ali ndi chifundo. Lamulo limakuika iwe mu ndende, koma silimakhoza kukutulutsamo iwe. Aneneri ndiwo chirungamo cha Mulungu, kuti adzakutsutseni inu ndi kukuphani inu chifukwa cha icho. Ndiko kulondola. Koma Yesu anali chikondi cha Mulungu ndi vumbulutso, kuti adziwitse, kwa Mbewu yokonzedweratu, kuti Iye anakuitananani inu. "Uyu ndiye Iye. Mvereni Iye!"

371 Kudziwa! Chidzalo cha Umulungu chikupangidwa kudziwika. Chinsinsi ichi cha chobisika tsopano chiri kuwululidwa, kuti Mulungu akuwonetseredwa. Mulungu ndi munthu akukhala Mmodzi, Mwamuna wodzozedwayo, Khristu! Kodi *Khristu* amatanthauza chiyani? "Iye wodzozedwa Uyo," Wodzozedwa amene anadzozedwa ndi chidzalo cha Umulungu mthupi. Oh, mai! Anthu angakaikire bwanji zimenezo?

372 Pamene nthawiyina, mwakagawo, Mose anali naye Iye; mwakagawo, Davide anali naye Iye; oh, mai, koma pano Iye akuwonetseredwa mwamphumphu, Umulungu Mwiniwake ataima pa dziko lapansi. Mulungu, mu chidzalo Chake, kuti adzafere tchimo la anthu, kuti Iye adzakhoze kubweretsa kwa Mpingo Wake Moyo woyeretsedwa; kuti Iye adzakhoze kukhala nawo uyambiriro, mwa chidzalo, mu Mpingo Wake, kuti adzawonetsere lonjezo lirilonse mmasiku otsiriza ano, zomwe Iye analonjezera masiku otsiriza. Mukuona? Chimene chinali . . .

373 Mvetserani tsopano. Kodi inu muli? Tsopano ingodzitsinani nokha pang'ono tsopano. Penyani.

374 Kodi Yesu anawonetseredwera chiyani? Kuti adzamuwonetse Mulungu. Iye anali Mulungu. Iye ankayenera kukhala ali; palibe munthu akanakhoza kufa, palibe mneneri akanakhoza kufa. Iye anali Mulungu. Iye anali Mulungu wa aneneri. Iye anali aneneri. Iye anali mafumu. Iye anali mbiriyakale. Iye anali Yemwe anali woti akudza. Iye amene anali, Iye amene ali, ndi Iye yemwe ayenera kukhala mu tsiku lino; yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye anawonetseredwera pa cholinga chimenecho.

375 Ndipo kudzera mu cholinga chimenecho Iye anapindulapo Mpingo, kuti Iye, chidzalo cha Mulungu, adzakhoze kubweretsa pochitika Mawu olonjezedwa aliwonse a Mulungu mmasiku otsiriza ano; pamene Iye atenga uyambiriro, uyambiriro mu Mpingo, udindo, malo Ake mu Mpingo. Yesu anati, "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuchita iye adzazichitanso; ngakhale zochuluka kuposa izi iye adzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga." Mwaona, icho chinali cholinga Chake. Apo panali mawonetseredwe. Ndipo tsopano, lero, Iye akufuna kuti amupeze winawake yemwe angakhoze kuziwona izo chotero, kuti iwo angakhoze kuwalola Mawu. . .

376 Mwaona, Yesu chotero anaziwona izo chomwecho, anabadwira mwangwiro tsikulo, mpaka Mulungu amafotokoza kusuntha kulikonse kumene Iye anakupanga. Iye anali vumbulutso la Mulungu; Mulungu, atawululidwa.

377 Tsopano Iye anawuyeretsa, ndi Mzimu Wake ndi Magazi, Mpingo, kuti Iye akakhoze kupanga lonjezo lirilonse mu tsiku lotsiriza lino kukhala lowululidwa. Tsopano, onani, Iye amakhoza kubwerera mmbuyo ndi kukatola zimene anyamata ena awa anazisiya kuno, mmasiku otsiriza, ndipo mwa Mzimu Woyera Wake akuwulula chinsinsi chonse cha Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. Mwaona, Iye akudzifotokoza Yekha. Ndicho cholinga Chake. Ndi chifukwa chake Iye anafa. Ndiko kufutukuka kwachiwiri kwa mawonetseredwe ofutukuka patatu Ake. Choyamba, kuti adzifotokoze Yekha mwa Khristu, kenako nkudzifotokoza Yekha kwa Mpingo. Ndipo chinthu chomwecho, Khristu anali Mawu, ndipo Mpingo umakhala Mawu pamene iwo ukuwalola Mawu kuti azidutsa mwa iwo.

378 Koma pamene iwo avomereza chipembedzo chahaibridi, Mawu angadutse bwanji mwa iwo? Iwo wagunda pansi, ndiye izo zimayambitsa kugundana kwa moto ndi kuphulitsa fyuzi. Mukuona?

379 Koma pamene nyetse ikuyenderera mwaufulu, Mawu a Mulungu, Iwo amadzifotokoza Okha. "Ntchito zimene Ine ndikuchita mudzakhala, inunso." Ndipo mmasiku otsiriza izo zidzafika pochitika: "Taonani ine ndidzakutumizirani inu

Eliya mneneri, ndipo iye adzatembenuzira mitima ya—ya ana kubwerera ku Chikhulupiriro cha atate."

380 Ndipo mmenemo, kudzakhala kuli nthawi imene Iye akanati adzadzifotokoze Yekha mu chidzalo cha Umulungu Wake, Umulungu kupyolera mu Mpingo Wake, kudzakhala ndi uyambiriro mu Mpingo uwu. Oh, mai! Chiyani? Munthu wodzozedwa; tsopano anthu odzozedwa; oh, mai, kuti abweretsenso Mkwatibwi wodzozedwa ndi Mkwati. Odzozedwa ndi (chiyani?) kulandira zimene Eva anazikana, ndi Adamu; kubwerereranso ndi kudzoza kwa Mawu, chifukwa Iye anati, "Mawu Anga ali Mzimu." Mwaona, kudzozedwa ndi Mawu. Zimene Eva anazikana, Iye akubwerereranso ndipo ife tikuzilandira.

381 Mukuona momwe chikhalidwe cha haibridi chimenecho, kachiwiri, ndendende basi zimene iye anamchititsa Eva.

382 Iye anamuuza Eva, "Iwe usachite *izi,* ndipo iwe usachita *izo*; ndipo iwe ukhoza kuchita *izi,* ndi *izo.*"

383 Ndipo Satana anati, "Oh! Iwe ukudziwa. . ." Koma iye anatembenuka ndipo anamvetsera kwa iye.

384 Koma Eva wa mu tsiku lotsiriza sadzachita zimenezo, chifukwa Iye anakonzedweratu kuti asadzachite zimenezo. Inde, bwana. Mulungu adzachita zimenezo. Iye akudziwa. Iye adzakhala naye iye. Iye anati Wake, banga. . ."Mpingo udzakhalapo wopanda banga kapena khwinya." Iwo udzaima pamenepo mu kukongola kwa Iye, Mawu Ake kukhala akuwonetseredwa.

385 Iye adzakhala chizindikiro kwa dziko lapansi. Iye adzakhala ch-. . .Iye adzakhala chinachake kwa dziko chimene dziko likhoza kuchiyang'ana ndi kuti, chabwino, dziko lonse kumanena kuti, "Aha, Iye ndi woyera wodzigudubuza. Iye ndi msuwani wachiwiri. Iye si wa mgulu lathu." Ine ndikudziwa. Ndicho chinthu chabwino, mwaona. Iye—iye ndi wa Gulu ili pamwamba *apa.*

386 Mwamuna ananena tsiku lina, kwa ine, ataima ndi kumayankhula, iye anati, "Chabwino, kodi ndiwe wa chipembedzo chiti?"

Ine ndinati, "Ndiribe."

"Chiyani?"

"Ndiribe." Ine ndinati, "Ine ndine wa mu Ufumu."

"Chabwino, mumajowina chotani mmenemo?"

"Simumajowina mmenemo. Mumabadwira mmenemo." Uh-huh.

"Ufumu umenewo ndi wuti?"

Ine ndinati, "Thupi lachinsinsi la Yesu Khristu."

387 "Mwa Mzimu umodzi ife timabatizidwira mu Thupi ili," kubadwa ndi Mzimu Wake, zikatero ife timakhala a mu Ufumu. Ndipo miyoyo yathu si ya Chimereka, ife si achi German, ife sitiri chirichonse; ife ndi Akhristu. Ife timakhazikika, ndipo timayenda mu Mzimu, akapolo a chikondi. Tinachoka ku zinthu za mdziko, ndi maufulu athu kwa dziko, ife tinawagulitsa ndipo tinagula Ngale iyi ya Mtengo Waukulu, ndipo tikuyenda ndi kulola Mzimu Woyera kuti uzidziwonetsera Wokha. Ndicho chimene Mpingo Wake weniweni uli. Ndicho chimene inu muli, kapena chimene ine ndiri, ngati ife titi tidzilole tokha kupita ndi kumamutumikira Mulungu, ndipo mwa Mawu Ake, ndipo osati mwa zimene kachikhulupiriro kena kamanena.

388 Zindikirani, Mwamuna wodzozedwa, Khristu Mwiniwake pano, O Mulungu, akupangidwa kudziwika. Koma tsopano, penyani, koma—koma tsopano (Wow!) Iye ali nawo uyambiriro. Mulungu atawonetseredwa kwathunthu, mwa Yesu Khristu, Chinsinsi chachikulu cha Mulungu cha vumbulutso Lake.

389 Kuwala kwakukulu uku kwa vumbulutso nthawizonse kwachititsa khungu nzeru za dziko lino.

390 Mmasiku a Yesu Khristu, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, iwo—iwo anali atawachititsa khungu iwo. Iwo anati, "Bwanji, inu mukudzipanga nokha Mulungu! Inu mukudzipanga nokha kufanana ndi Mulungu!" Iye sanali wongofanana ndi Mulungu; Iye anali Mulungu Mwiniwake. Mwaona, iwo samamvetsa zimenezo. Ndipo tiri chiyankhulire, ena a inu mukhoza . . .

391 Ine ndinawamvapo achikunja nthawi ina anandiuza ine kuti Yesu sananene konse kuti Iye anali Mwana wa Mulungu. Iye zedidi anatero. Iye ndithudi anatero. Kungoti inu simumalidziwa Baibulo lanu. Kodi Iye ananena chiyani kwa mkazi pa chitsime? Mukuona? Kodi Iye anamuuza chiyani iye?

392 "Ine ndikudziwa Mesiya akudza. Ndipo pamene Iye adzadza, Iye adzachita zinthu zimenezi."

Iye anati, "Ine ndine Iye, ndipo akuyankhula ndi iwe."

Ndipo kwa Paulo, nayenso, ndi ena osiyanasiyana.

Zindikirani. Koma tsopano Mpingo uli nawo uyambiriro.

393 Chinsinsi chachikulu cha Mulungu nthawizonse chachititsa khungu nzeru za mdziko. Iwo samakhoza kuzimvetsa izo. Iwo samazimvetsa basi izo. Satana samazimvetsa izo. Palibe ena onse a iwo amazimvetsa izo, koma iwo okha amene anali atakonzedweratu kuti adzazimvetse izo, momwe Mulungu ndi Khristu ali Mmodzi. Iwo amamupanga Iye atatu nthawizonse. Mukuona? Iwo ndithudi amatero.

394 Zindikirani, chotsatira, mwachiwiri, Khristu wowonetseredwa mwa inu, chiyembekezo cha ulemelero.

Mulungu wamkulu uja, wowonetseredwa mwa Khristu; tsopano Khristu akuwonetseredwa mwa inu.

Ife tifulumira.

395 Penyani! Chimene nthawiyina chinali chinsinsi chachikulu cha Mulungu, chinsinsi chachikulu chobisika mmalingaliro Ake, tsopano chikuikidwa mmitima ya wokhulupirira, limenelo ndiro, Thupi la Khristu. Chimene nthawiyina chinali chinsinsi chachikulu cha Mulungu mmalingaliro Ake, asanaikidwe maziko a dziko lapansi, tsopano chikupangidwa kuti chiwonetseredwe. Taganizani za zimenezo, mzanga. Oh, oh, ine ndiri . . .

396 Ine ndikutsimikiza ife sitiri, ife sitikuzimvetsa izo. Chabwino, ine—ine sindingakhoze kuziwona izo mwanjira yomwe ine ndiyenera kuchitira, ndipo—ndipo ine ndikutsimikiza inu simukutero. Mukuona?

397 Koma chinsinsi chachikulu cha Mulungu, chimene Mulungu Wamuyaya anali nacho ngati chinsinsi, tsopano chakhala chikufutukuka mwa Yesu Khristu, kenako chikuperekedwa kwa Mpingo Wake. Chimene nthawiyina chinali mmalingaliro a Mulungu tsopano chiri mu Thupi la Khristu. Yesu kupanga chikondi kwa Mpingo, Mkwatibwi Wake, kunong'oneza zinsinsi kwa Iye.

398 Inu mukudziwa momwe inu mumamuuzira mkazi wanu zinthu, inu mukudziwa, mtsikana wamng'ono yemwe inu muti mumukwatire. Inu mumamukonda iye mochuluka kwambiri, inu mumangomuwuza iye zinsinsi, ndi kumufikitsa iye pafupi ndi inu, ndi kumakukonda iwe ndi chirichonse. Inu mukudziwa momwe izo zimakhalira.

399 Ndicho chimene Mulungu, Khristu, akuchita kwa Mpingo. Mukuona? Iye akumulola Iye kuti azidziwa zinsinsi, zinsinsi basi. Osati odzifunitsa awa; ine ndikutanthauza Mkazi Wake (Mukuona? Chabwino, tsopano penyani.) akudziwa, pakukhala nalo vumbulutso la chinsinsi Chake kukhala chikudziwika kwa iwo, mwa chisomo Chake! Momwe chisomo cha Mulungu! Anthu, ine ndikudziwa zimenezo . . . ine ndikuyembekeza kuti inu simukuganiza kuti izi zikumveka zopita kwa munthu winawake, kwa—gulu la anthu, kapena *izi, izo;* koma chinsinsi chimene Mulungu akugawana nawo Mpingo wonse, ngati iwo angachilandire icho. Mukuona? Izo sizikutanthauza ine ndekha kapena inu nokha. Izo zikutanthauza Mpingo, kuti Iye—Iye akuyesetsa kuti alowemo.

400 Ndipo inu mukuti, "Chabwino, bwanji iwo sakuchilandira icho?" Iwo sangakhoze kuchilandira icho. Iye anati, kachiwiri, Iye ananena zinthu izi. "Ndipo iwo angakhoze bwanji?" Chifukwa Yesaya anati iwo sangakhoze kuziwona izo. Mukuona? Ndipo Iye nthawizonse amati . . .

401 Mneneri Paulo anati, "Mmasiku otsiriza anthu akanati adzakhale ammutu, amalingaliro-apamwamba, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu, okuswa pangano, onenera amzawo zabodza, osadzigwira ndi onyoza iwo amene ali abwino; ammutu, amalingaliro-apamwamba, mwaona; okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma nkumakana Mphamvu yake; kwa oterewo chokaniko. Pakuti uwu ndi mtundu umene umapita nyumba ndi nyumba, ndi kumatsogolera akazi opusa, otsogozedwa ndi kusilira kosiyanasiyana," ndi makabudula, ndi tsitsi lodula, ndi china chirichonse. "Otsogozedwa ndi zisiliro zosiyanasiyana, ndi kumati, 'Ndi zabwino. Oh, iwo ndi openga kumeneko. Musakhale nawo. . .'" Mukuona? "Osakhoza konse kuti adze ku chidziwitso cha Choonadi. Ndipo amuna awa amatsutsa Izo, monga Ayane ndi Ayambre anamutsutsa Mose," okhoza kupanga mpingo, ndi kupanga gulu la anthu. Inde, bwana.

402 "Koma kupusa kwawo kudzachita kuwonetseredwa," pamene Yesu azidzamutenga Mkwatibwi Wake ndi kumukhazika Iye pamwamba apa, ndi kuti, *"Uyu* ndiye Iye," ndipo kutali Iye nkumapita limodzi ndi Iye. Ndiko kulondola. Ndipo kupusa kwawo kudzachita kudziwika.

403 Taonani zimenezo, kukhala nalo vumbulutso la chinsinsi ichi chikudziwitsidwa kwa iwo mwa chisomo Chake! Penyani! Pamene vumbulutso lalikulu ili, chinsinsi chowululidwa, chikupangidwa kudziwika kwa inu, ndiye inu mumanyoza zinthu zonse za mdziko.

404 Tsopano ine ndati ndibwerérenso kachiwiri. Ine ndikhoza kungonena izo, ine ndikulozera kwa izo, chifukwa cha tepi, ndi iwo amene akupita kwina; tepi iyi ikupita ku dziko lonse. Mukuona?

405 Inu akazi amene mumadzinenera kuti muli nawo ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo opanda ulemu kuti muzililola tsitsi lanu kumakula; pamene Baibulo limatsutsa izo ndipo linati la mkazi. . .mwamuna ali nawo ufulu kuti amusiye mkazi wake mwa chilekano ngati iye adula tsitsi lake. Ndi wovomerezedwa pamaso pa Mulungu, kuti achite choncho. Baibulo linati, ngati iye adula tsitsi lake, iye akunyozetsa mutu wake. Ndipo ndi chawamba; basi, inu mukudziwa, chimene chinthu chirichonse chawamba chakale chimakhalira, kuti mkazi ngakhale kuti apemphere ndi tsitsi lodula. Mukuona?

406 Kuvala akabudula, ndi zazifupi izi, ndi zinthu! Baibulo linati, "Mkazi aliyense yemwe ati," (oh, inu mukuti. . .) "amene avala chovala chimene chiri choyenera kwa mwamuna, ndi themberero kwa Mulungu," nyansi, zakuda, monga bafa yonunkha yachikale kwinakwake. Mukuona? Oh, mai! Nyasi mmphuno za Mulungu! Ndiyeno inu nkuyesa kuti muzipemphera kapena kupereka mapemphero mu chinthu

chotero chonga chimenecho? Mulungu amazikana zimenezo, amachikankhira kwina. Ndiko kulondola.

407 "Chabwino," inu mukuti, "tsopano dikirani miniti, M'bale Branham, inu mukuyankhula za Chipangano Chakale."

408 Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndiro vumbulutso lathunthu la Mulungu. Mulungu akayankhula konse chirichonse, Iye sangakhoze konse kuchisintha icho. Iye nthawizonse amachikulitsa icho, osati kuchisintha icho. Lamulo linakulitsidwa, osati kusinthidwa. Linakulitsidwa!

409 "'Yense yemwe achita chigololo adzakhala wochimwira imfa,' koma yense," tsopano litakulitsidwa, "ayang'ana pa mkazi ndi kumusilira iye!" Iye sanasinthe konse lamulo. Iye analikulitsa ilo.

410 "'Muzikumbukira tsiku la sabata; muzilisunga ilo mopatulika,'" tsiku limodzi mu sabata; tsopano Iye analikulitsa ilo, "mpumulo" umabwera kuchokera pa kusunga Mzimu wa Mulungu. "Lemba pa lemba, ndi mzere pa mzere; pano pang'ono, ndi apo pang'ono. Ndi kugwiritsitsa icho chimene chiri chabwino. Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ine ndidzayankhula kwa anthu awa. Ndipo umenewo ndiwo mpumulo. Ndiko kupumula kochokera ku Kukhalapo kwa Ambuye."

411 Ndipobe iwo sanakhoze kumvera Izo, ndipo anagwedeza mitu yawo ndipo anayenda nkuchokapo, chifukwa cha zipembedzo zawo. Uh-huh. "Uku ndiko kutsitsimutsa," mwaona, kulikulitsa tsiku la sabata; kwa inu Asabata, ndi ena otero. Oh, mai! Iye sakusintha. Iye analikulitsa ilo. Gehena watambasula zipata zake kuti awalandire iwo.

412 Tsopano, inu mukhoza kuwona tsopano, Uthenga wa nthawi yotsiriza, chifukwa chimene Iwo ukukanidwa. Mungakhoze inu? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Tsopano, palibe chipembedzo, koma vumbulutso la chinsinsi Chake. Mukuona, palibe chipembedzo. Vumbulutso! Mulungu samadziwika ndi chipembedzo. Iye amadziwika ndi vumbulutso.

413 Mukuona! Mulungu mu Thupi Lake, Khristu; ndipo Khristu mu Thupi Lake, Mkwatibwi. Oh-oh-oh, mai! Mulungu kukhala akuwonetseredwa mwa Khristu; Khristu kukhala akuwonetseredwa mwa Mkwatibwi! Ndipo monga Mulungu anatenga kuchokera mu thupi la Adamu, mkazi, ndipo iye anagwa; ndiye Mulungu watenga kuchokera mu Thupi la Khristu, mnofu Wake, Thupi Lake, lomwe liri Mawu Ake, ndipo akumutulutsapo Mkwatibwi yemwe sadzagwa ndi chipembedzo kapena kachikhulupiriro. Ayi, bwana. Koma Iye akubwerera ndi Mawu a Mulungu angwiro, osaipitsidwa kukhala akuwonetseredwa.

414 Ine ndikuyembekeza mwamuna aliyense yemwe angakamvetsere tepi iyi, ndi mkazi aliyense, akamvetsa izo. Mukuona?

415 Iye ndi Eva wachiwiri, koma Iye sakuswa ayi ndi—ndi kuipitsa zovala Zake za ungwiro ndi chiyero, kwa Mwamuna Wake. Iye adzakhalabe ndi Mawu Ake mosasamala zimene aliyense anena. Inu mukhoza kukhala nako kayendetsedwe konse ka zipembedzo kamene inu mukukafuna, ndi zigwirizano zonse.

416 Ndipo iwo adzabweretsa chisautso, posakhalitsapa, ndipo adzatseka mipingo yonse. Inu muziwona zimenezo. Ndipo matchalitchi ngati awa omwe siali chipembedzo, iwo adzawagwiritsa iwo nchito ngati mosungira zinthu, chirichonse. Ndipo ngati munthu aliyense apita ndi kukapempherera wina aliyense yemwe sali wa nkayendetsedwe ka zachuma, adzawomberedwa pomwepo. Izo ziripo kale. Mtumiki wa Chilutera uja, mkulu wa iwo, ananena chomwecho. Ndipo izo ziri komwe kuno, inu mukhoza kuziwerenga izo komwe kuno mmagazini anu. Kulondola.

417 Sizikupangitsa kusiyana kulikonse ndi zimene iwo akunena, Mpingo umenewo udzaima moona mu kumenyana uku. Iye anatsimikizira kale izo mmbuyo kutaliko, ndipo Iye adzachita izo kachiwiri mu nkhope ya chirichonse. Ndi Mawu a Mulungu. Ndipo iwo, mayendetsedwe onse a zipembedzo ndi china chirichonse zidzakhala zitapita. Iye adzakhala ali Pamenepo wopanda banga kapena khwinya. Ndiko kulondola. Iye adzaima pamenepo.

418 Zindikirani, Mulungu anadziwonetsera Yekha mthupi Lake, Khristu. Tsopano inu mukuona kufutukuka patatu, chinthu chokongola?

419 Khristu mu Thupi Lake, Mpingo, akutsimikizira Mawu Ake olonjezedwa, monga Mulungu anachitira kupyolera mwa Khristu.

420 "Ndani anganditsutse Ine za tchimo? Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate, ndiye ndi pati Ine—ndi pati pamene Ine ndalephera? Tsopano anyamata inu mukuti inu mukuchita zimenezo, inu chipembedzo pano, tsopano ndisonyezeni Ine. Eya. Ndisonyezeni Ine pamene Ine ndalephera kuti ndikhale Mesiya. Sonyezani pamene Ine ndalephera, pa chizindikiro chimodzi chimene Mulungu anati Mesiya akanati adzachite, chimene ine sindinakwaniritse icho," Iye anati. Mukuona? Mulungu mu thupi Lake.

421 Tsopano Khristu, "Ntchito zimene Ine ndikuchita mudzazichita inunso." Mwaona, mwaona, Mulungu yemweyo. Mukuona? "Ntchito zimene Ine ndikuchita mudzazichita inunso; zochuluka kuposa izi, pakuti ine ndikupita kwa Atate Anga," Mpingo udzakhala motalika pang'ono mu Kuwala, mwaona.

Kutsimikizira Mawu Ake olonjezedwa. Monga Mulungu anachitira malonjezo Ake mu thupi la Khristu, chomwechonso Khristu akuchita ntchito Zake zomwezo mu Thupi la Khristu, Mpingo, mwaona, tsopano akupanga chinsinsi Chake kudziwika kwa Mtengo wa Mkwatibwi Wake mu tsiku lotsiriza, kubala zipatso zimene zinali mu Mtengo pachiyambi.

422 Penyani, mtengo ukuika nthambi, Chilutera. Kodi iyo inachita chiyani? Pamene mtengo unayamba kukula, apa panadzabwera chipatso chikubwera mmwamba ndi iwo. Nchiani chinachitika? Iwo anawupanga chipembedzo iwo. Chotero wotengulira anabwerapo, Atate, Mwiniwamunda, ndipo anadzaudulapo iwo, akuti, "Ndi wakufa."

423 Mmwamba munabwera Achiwesile; anachita bwino kubwerapo. Kodi iwo anachita chiyani? Chipatso chinabwereranso kukakhala mtengo kachiwiri, chotero Iye anaidula nthambiyo, iwo wafa.

424 Ndisonyezeni inu umodzi, mpingo umodzi . . . ine ndikufuna kuti ndidziwe. Ine ndiri ndi zaka sarte firii za mbiriyakale ya mpingo. Ndisonyezeni ine nthawi imodzi, malo amodzi, kumene mpingo uliwonse unayamba wachita bungwe umene sunafe pomwepo. Ndisonyezeni ine malo amodzi pomwe unayamba wauka kachiwiri, kunja kwa chiwerengero chabe ndi zinthu, osati chitsitsimutso. Mukuona? Palibepo. Ayi, bwana. Iwo wonse wapita.

425 Chotero kodi Mwiniwamunda anachita chiyani? Anabwera pamenepo ndipo anadzawudulira iwo. Mukuona? Iwo unkabala chipatso cha chipembedzo; mandimu pa mtengo wa lalanje, chotero Iye anawudulira iwo, mwaona. Unkabala izo, unkapitirira.

426 Koma kodi mtima wa mtengowo uli pati? Pakati pomwe. Ndipo Iye anayidulira iyo mpaka pansi, mpaka pamwamba pomwe . . .

427 Iye ali nayo Mbewu pansi apa ku muzu. Monga mtengo umene wabzalidwa mmphepete mwa mitsinje ya madzi, iye amene amatenga malamulo a Mulungu ndi chikondi mu mtima mwake. "Ndipo iye adzakhala monga mtengo," Masalmo 1, "wobzalidwa mmphepete mwa mitsinje ya madzi; masamba ake sadzanyala; mu nyengo yake iyo idzabala chipatso chake." Ndipo pano izo ziri molondola . . .

428 Ndi kodi chipatso chimacha mwamsanga pati? Pamwamba pa mtengo. Chifukwa chiyani? Kuwala kumakhala pamenepo. Ameni! Ndiko kulondola. Ndipo pamwamba pomwe pa mtengo, mmasiku otsiriza ano, Iye akubweretsapo Mtengo wa Mkwatibwi.

429 Tsopano kumbukirani, Iye ndi Mtengo wa Moyo umenewo, motsutsana ndi "mbewu ya serpenti," inu mwaona. Iye ndi Mbewu imeneyo, "Mbewu ya mkazi," Mtengo wa Moyo mmunda.

"Ndipo kuwopa kuti angaike manja awo ndi kuwusuntha Mtengo uwu, iwo akanati adye Mtengo umenewo ndi kukhala moyo kwanthawizonse." Ndipo Iye ndi Mtengo wokhawo umene ungakhoze kudyedwa, kuti iwe uzikhala moyo kwanthawizonse. Mawu Ake ndi Moyo. Ndipo awo pokhala Mawu ndiye, Mawu a Mulungu amene Eva anawakana mmunda wa Edeni; ndiye pano pali Khristu, Mawu, kukhala akuwonetseredwa.

430 Ndipo pamene Iye anabwera pa dziko lapansi, Iye anali Mtengo wa Moyo. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndipo Roma, kodi iwo anachita chiyani? Iye ankayenera kuti akhapidwe. Ndipo Iye anaikidwa pa mtengo wa chamanyazi, "wotembereredwa ndi iye amene apachikidwa pa mtengo," kukhala themberero chifukwa cha mtundu wa anthu.

431 Ndipo tsopano kupyolera mu zimenezo, Iye akuwubweretsa Mtengo wa Mkwatibwi, umene uti udzakhale Mtengo wa Moyo utabwezeretsedwanso kwa Iye, monga Mwamuna ndi Mkazake mmunda wa Edeni, (oh, ulemelero kwa Mulungu) mwa Mawu omwewo ndi Mulungu yemweyo kukhala akuwonetseredwa mwa Mwamuna ndi Mkazake, Mtengo wa Mkwatibwi womwewo utabwerera kachiwiri.

432 Zindikirani, kuzipangitsa izo kudziwika! Momwe. . .Mai, pangokhala zochuluka basi pano, ife tikhoza kumangopitirira nazo. Zindikirani, Mtengo uwu, wa Thupi la Khristu, mmunda. Kupanga, tsopano akupanga chinsinsi Chake kudziwika kwa Mtengo wa Mkwatibwi uwu.

433 Penyani, wowomboledwa ndi Khristu, Adamu wachiwiri. Inu mukukhulupirira kuti Iye anali? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Kubwereranso Kwawo, ku Edeni, ndi mkazi Wake wakugwa atawomboledwa kubwerera Kwawo kachiwiri. Ameneyo ndi Khristu mu Mpingo lero, akumutenga Mkazi Wake abwerere. Mukuona chinsinsi chofutukuka patatu tsopano? ["Ameni."] Mulungu kuwonetseredwa mwa Khristu; Khristu kuwonetseredwa mu Mpingo; zonse palimodzi, kuti amubwezeretsenso Adamu wapachiyambi ndi Eva kachiwiri, mwamuna ndi mkazi, omwe ali mmodzi, opangidwa kuchokera mu Magazi ofanana ndi Mzimu wofanana, ndi china chirichonse.

434 Mpingo ndiwo Magazi a Khristu, mwa Mzimu, chifukwa a—Moyo umakhala mu Magazi. Umenewo ndi ubatizo wa Mzimu Woyera umene umatibatiza ife kulowa mu Thupi Lake, umene umalizindikira Thupi Lake lokha, Mnofu Wake, Mawu Ake. [M'bale Branham akusisita Baibulo lake—Mkonzi].

435 Chipembedzo sichingatero, sichingazikhudze konse zimenezo. Ilo ndi vumbulutso. Iye akuzidziwa zimenezo. Chomwechonso Eva ankadziwa izo, koma iye anagwa; koma uyu akudziwa zimenezo, ndipo sagwa ayi. Iye ndi wodzozedwa! Aleluya! Psyii! Iye anadzozedwa kuti asadzagwe. Iye salephera.

Iye anakonzedweratu kwa izo. “Wodala ndi munthu yemwe Mulungu samamuwerengera tchimo.” Atumiki inu mukudziwa zimene ine ndikuzikamba, pamene pali madazeni angapo a inu mwakhala pano. Mukuona? “Wodala ndi munthu yemwe Mulungu samamuwerengera tchimo,” Davide.

436 Zindikirani, kuwombola abwerere, ndi Iye, akupita Kwawo; kubwerera ku Moyo Wamuyaya mu thupi laumunthu, kumadya, kumamwa, kumakhala moyo kwanthawizonse. Yesaya anati, “Iwo adzamanga manyumba ndi kumakhala mmenemo, kubzala minda ya mpesa ndi kumadya chipatso. Iwo sadzamanga ndipo wina nkuyitenga iyo.” Ana sadzaitenga iyo, koma iwo azidzakhala kumeneko ndi mphukira zawo. Iye azikamanga iyo ndi kumakhala mmenemo. Ameni. “Iye samakamanga, ndipo wina nkudya; iye akumanga ndi kumadya, mwiniwake.” Ameni! Ndi chiyani icho? Mkwatibwi Wake kubwereranso ndi Iye, owomboledwa kubwerera kwa Adamu wapachiyambi ndi Eva kachiwiri, pakuti imfa yasiyidwa mmbuyo. Iwo akuyang’ana mmbuyo pa mtanda ndi kuwona imfa kuti yalipiridwa kale.

437 Ndipo tsopano, mwa chikhulupiriro, ife tawukitsidwa ndi Iye, tikukhala mmalo Ammwambamwamba pakali pano, tikuyang’ana mmbuyo ku chimene chinatiwombola ife; kuyembekezera Mwamuna kuti abwere, kuti tidzagube wopita Kwathu ndi Iye.

438 Cholinga chofutukuka patatu cha Mulungu, chowonetseredwa mwa Adamu ndi Eva, ndi mneneri aliyense, ndipo kutsika kudutsa mibadwo, ndi Iye amene ali nkudza; Iye amene anali, Iye amene ali, ndi Iye—Iye amene ali nkudza. Mawonetseredwe onse, vumbulutso la Mawu a Mulungu, Adamu ndi Eva kubwerera Kwawo kachiwiri, owomboledwa, Mulungu kudzipangitsa Yekha kudziwika!

439 Kumeneko Iye adzakakhala pa Mpandowachifumu wa Davide, (Nkulondola uko?) ndipo adzakhala nawo, adzalamulira mafuko onse ndi ndodo ya chitsulo. Padzakhala pali m—mtengo pa mbali iliyonse, ndipo fuko lirilonse limene likubwera mmenemo, kuchiritsa uku kudzakhala kwa. . .masamba awa adzakhala a kuchiritsa kwa mafuko. Mafumu azidzabweretsa ulemu wawo mmenemo. Simudzakhala kanthu kamene kangadetse, kapena chirichonse chiti chidzalowemo konse. Ndipo Phiri la Zioni lidzakhala nako Kuwala pa ilo, usana wonse ndi usiku, ndipo owomboledwa azidzayenda mu Kuwala kumeneko. Oh, aleluya!

440 Kuganiza, kuti si nthano ayi, si lingaliro lina la zafioloje. Ndi vumbulutso la Yesu Khristu, mwa Mawu Ake, amene akuwala moposa, izo zakhala zoona mmibadwo yonse. Ndipo Izo ndi zoona mu m’badwo uno. Izo ndi zoona pano tsopano. Izo ndi zoona ndi ine, Izo ndi zoona ndi inu, ndi mwamuna aliyense ndi mkazi amene wagwira vumbulutso ili. Ameni.

441 Ndipo kumuwona Mulungu Mwiniwake akudzipangitsa Yekha kudziwika, ndi kumadzigunditsa Yekha kudzera mmoyo, kuti ndinu wamndende kwa Iye tsopano. Inu ndinu wamndende Wake wa chikondi. Dziko likhoza kuseka, kuwaselewula iwo, kumati, "Tiyeko tulukani." Inu mukanakhoza kupitako, koma ndinu wamndende. Mukuona? Akazi ena akhoza kumachita mwachi Hollywood, koma osati inu. Ndinu wamndende. Ameni. Mwaona, ndinu wamndende kwa Khristu. Amuna ena akhoza kumasuta ndi kumamwa ndi kumapitirira, ngati iwo akufuna kutero, ndi kumadzitcha okha Akhristu, madikoni, ndipo ngakhale alaliki, koma osati inu. Ndinu wamndende, wamndende ku Mawu. Inde, bwana. Inde, bwana.

442 Kupangitsa chinsinsi Chake kudziwika kwa Mtengo wa Mkwatibwi Wake; wowomboledwa ndi Khristu, Adamu wachiwiri; akubwereranso Kwawo, kuti akabwezeretsedwenso ku Edeni wapachiyambi, mfulu kwa imfa, matenda, chisoni, manyazi, akubwereranso ndi Moyo Wamuyaya.

443 Ndiye, mvetserani, anthu ochuluka kwambiri ali nalo lingaliro lolakwika. A—a. . .Kuwatembenuzira anthu ku Chikhristu, ndi kwa boma lake, si lingaliro la Mulungu nkomwe. Inu mukuti, "Ife timapanga otembenuka kupita ku Chikhristu mwa boma Lake." Si ndizo ayi. "Chabwino, iwo sakuyenera kuti azimwa. Iwo sakuyenera kuti azinama." Inu mukudziwa kuti Achimuhamadi akhoza kukuposani inu? Inu mukudziwa achikunja mu Afrika, anthu akuda amenewo, ndipo iwo ali nawo malamulo pakati pa mafuko awo amene angawale moposa chirichonse chimene inu mungakhoze kuchibweretsa mu Chikhristu.

444 Bwanji, ine ndinapitako ku fuko ilo la Shangani kumeneko. Ngati mtsikana wamng'ono sakwatiwa pofika usinkhu winawake, iye ayenera kuchokapo—kuchoka mu fukolo, kuchotsa utoto wa fuko lake. Iye amapita mu mzinda; iye amangokakhala woyendayenda. Ndipo ngati iye. . .Iye asanakwatiwe, iye amayenera kuti ayesedwe unamwali wake. Iye akapezeka ali wolakwa pa kuchita chigololo ndi mwamuna wina, iye. . .iye amayenera kuti anene yemwe uyo anali, ndipo iwo awiri onse amaphedwa, limodzi. Uh-huh. Oh, iwo akhoza—iwo akhoza kuposa zomwe zikutchedwa izi. . .

445 Bwanji ngati inu mutachita izo mwa otchedwa Akhristu? Magawo nainte-naini pa handiredi a iwo akanati afe dzuwa lisanatuluke. Ndiko kulondola. Ndi kulondola, onse amuna ndi akazi. Inu mukudziwa uko ndi kulondola.

"Chiyani?" Inu mukuti, "Chabwino, ndine wangwiro!"

446 "Aliyense yemwe ayang'ana pa mkazi namukhumbira iye wachita kale chigololo ndi iye mu mtima mwake." Tsopano nanga bwanji zimenezo? Nanga bwanji inu, mlongo, yemwe inu munadzipereka nokha kwa mwamuna ameneyo monga

chomwecho? Ndinu wolakwa basi ngati kuti inu munazichita izo. Mukuona?

447 "Oh, koma izo zonse nzabwino." Abusa amawopa kuti azinena zimenezo, chifukwa chiyani? Likulu lawo la chipembedzo liwathamangitsira iye panja ngati ayamba kumalunjika pa izo. Iwo ndi haibridi. Iwo samatenga Mawu. Mawu anati izo ndi zoona. Yesu anati ndi zoona, ndipo Iye ndi Mutu.

448 Tsopano zindikirani, Mulungu akudzipangitsa Yekha kudziwika. Ayi, ife sitimayenera kuti tizipanga otembenukira ku Chikhristu mwa boma; koma mwa vumbulutso, Khristu mwa inu, monga Mulungu anali mwa Khristu. Monga Mulungu anali mwa Khristu, Khristu mwa inu! Pamene, zimene Mulungu anachita mwa Khristu, Khristu akuzichita mwa inu! Ndi zizindikiro zimene Mulungu anazichita mwa Khristu, Khristu akuzichita mwa inu! Oh, kodi zimenezo si zokongola? Uh! Oh, mai! Ine ndikuzikonda zimenezo.

449 Yesu anati, "Pa tsiku limenelo," limenelo ndi tsiku lino. "Pa tsiku limenelo," pamene vumbulutso ili lidzakhala likudziwitsidwa, "inu mudzadziwa kuti ine ndiri mwa Atate, ndipo Atate ali mwa Ine; Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine." Pamene vumbulutso lidzakhala likuwonetseredwa, "Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndi Atate tiri Mmodzi; Ine ndiri mwa Atate, ndipo Atate ali mwa Ine." Ndiye pamene vumbulutso lidzabwera, ndiye ndi, "Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine." Ndi zimenezotu. Mukuona kuchuluka, kufutukuka patatu-. . .Kwa chiyani? Kuti abwezeretse izo. Ife tiyenera kuti tikhale. . .

Monga Yesu anali Mawu a Mulungu, Iye anatsimikizira zomwezo.

450 Ngati Iye—ngati Iye akanati asakhale Mawu, Iye sakanati awonetsere Mawu, Iye akanakhala wazafioloje wina wamkulu. Ameneyo akanakhala mesiya weniweni yemwe dziko linali kumuyembekezera. Mukuona? Inde, bwana, ameneyo akanakhala iye.

451 Ndizo zimene iwo akuziyembekezera lero, wina—wina—wina angakhoze kumuposa Billy Graham, kapena winawake angakhoze kupikisana ndi bungwe lawo, kubwera ndi kudzawasonyeza Achibaptisti awo kuti iwo sakudziwa pamene iwo ayima. Ndithudi. Iwo akuyembekezera zimenezo. Koma Mpingo ukuyembekezera kudzichepetsa ndi zizindikiro za Mulungu wamoyo, Khristu.

452 Yesu sanali wazamulungu wamkulu. Iye anali m'mphawi wamba, mwana wa ampalamatabwa, amatchedwa-chomwecho. Mukuona? Iye ankayendayenda, koma Mulungu. . .Iye anati, "Ena a inu mundisonyeze Ine chimene Baibulo limanena kuti Ine ndidzachita, chimene ine sindinachiwonetsere."

453 Chotero Mpingo ukhoza kuchita chinthu chomwecho lero. Chimene Khristu anachita, chomwecho Mpingo ukuchita tsopano. “Tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate, ndipo Atate ali mwa Ine; Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine.” Mukuona? Pamenepo inu mukupita, mukuguba kupita ku Zioni, wa (kuti?) ku Ufumu! “Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa inu.”

454 Ndipo penyani apa. Apa, izo ndi zokongola. Ine sindikufuna kuti inu muziphonye izi. Tsopano aliyense, ndipo anthu inu pa tepi, kunja uko mu nkhalango ndi kulikonse kumene inu mukumva Izi, tsopano mvetserani.

455 “Ndipo monga Atate anditumа Ine, chomwechonso Ine ndikukutumani inu,” Yesu anatero. Mukuona? Tsopano penyani. Atate amene anamutuma Iye anapita mwa Iye, kuti akadzitsimikizire Yekha kuti akulondola, pakuti Iye anali Mawu. Ndipo Yesu yemweyo amene akukutumani inu, akupita ndi inu ndi mwa inu, kuti akamutsimikizire Mulungu yemweyo. “Monga Atate anditumа Ine, ndipo Ine ndikukhala moyo ndi Atate; chomwechonso Ine ndikukutumani inu, ndipo inu mukakhala moyo ndi Ine.” Iye ndi chiyani? Iye ndi Mawu. Inu mumakhala moyo ndi Mawu. Oh, momwe ine ndikanafunira kutenga mutu pamenepo, ndi kulalikira tsopano kwa pafupifupi maora angapo pa izo, mwaona, pa zimenezo, momwe Iye anali...pa zimenezo. Zindikirani, zindikirani, “Ndipo Atate amene ananditumа Ine,” amapita ndi Iye. Atate amene amamutuma...Yesu amene amatituma ife amalowa mkati.

456 “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silindiwona Ine kenanso, komabe inu muzindiwona Ine, pakuti Ine,” puronauni yaumwini, “Ine,” Munthuyo, Yesu, “ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a dziko lapansi. Ntchito zimene Ine ndikuchita mudzazichita inunso.” Tsopano bwererani ndipo mukawone zimene Iye ankachita, ndiye muwone zimene inu mukuchita, ndiye mudzifanizitse nokha.

457 “Ndipo monga zinali mmasiku a Nowa, chomwechonso zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu. Ndipo monga masiku a Loti,” pamene Billy Graham wamakono ndi Oral Roberts anapita uko ku Sodomu ndi kukalalikira kwa Achisodomu awo, ndipo anawachititsa khungu maso awo, mwaona, ndi Uthenga. Mngelo Mmodzi anatsalira mmbuyo, Mtumiki ndi Abrahamu ndi gulu Losankhidwa, ndipo kodi Iye anachita chizindikiro cha mtundu wanji? Mukuona? Ndipo kodi Abrahamu anamutcha chiyani Iye? Elohim, Mulungu atawonetseredwa mu thupi. Yesu akudzisonyeza kuti Iye Mwiniwake, Mulungu mwa Iye, adzakhala akudziwonetsera mwa Mkwatibwi Wake mmasiku otsiriza! Oh, mai, mai! Basi palibe mapeto kwa izo; vumbulutso basi la Mulungu! Ndi

Lamuyaya, limangomasuntha mopitirira ndi mopitirira ndi mopitirira.

458 Zindikirani, ndiye, Mmodzi wonga Adamu woyamba ndi Eva, tchimo lisanawalekanitse iwo mu imfa; tsopano Khristu, Adamu wachiwiri, mu Moyo, akumuwombola Mkwatibwi Wake kuchoka ku imfa; ndipo tsopano ali paulendo Wake kubwerera ku Edeni wapachiyambi, kumubwezeretsanso Mkwatibwi Wake mu chiyanjano, kubwererana ndi Mulungu, monga Mwamuna ndi Mkazake, mmunda wa Edeni, Khristu ndi Mkwatibwi Wake.

459 Ndipo Mulungu, pa tsiku limenelo, "Ufumu udzaperekedwa kwa Atate; Iye akakhoze kukhala zonse mu zonse." "Pamene iye akadali chiyankhulire, ine ndidzamva." Davide, Khristu, Davide atakhala pa Mpandowachifumu, Mfumu pa mtundu wonse wa anthu. "Ndipo iwo akadali nkuganiza, ine ndizidzadziwa chimene iwo ali kuchiganizira. Iwo asanati ayambe kuyankhula, ine ndizidzawayankha iwo. Nkhandwe ndi mwanawankhosa zizidzadya limodzi. Mkango uzidzadya nsipu monga ng'ombe, ndipo izo zizidzadyera limodzi ndi kumagona pansi. Izo sizimadzapwetekana ngakhale kuwononganana mu Phiri Langa lonse lopatulika," kubwerera ndendende ku Edeni kachiwiri, mwamphamvu momwe izo zingakhoze kumapitira!

460 Ndi chimenecho cholinga Chake chofutukuka patatu. O Mulungu, tithandizeni ife kuti tizidziwe izo! Tithandizeni ife kuti tizidziwe izo!

461 Mvetserani mwatcheru tsopano kachiwiri pamene ife tikupitirira, kubwerera ku Edeni wapachiyambi.

462 Ndiye pamene ife tibadwa ndi Iye, ife timadzazidwa ndi Iye. Mwaona, moyo wanu, Moyo Wake umakhala mwa inu. Ndiye, zochita zathu zonse ziyenera kumafotokozera Iye.

463 Monga kutenga—kutenga moyo kuchokera mu mtengo wina ndi kukawuyika iwo mu umzake. Kutenga moyo kuchokera mu mtengo wa peyala ndi kuika mu mtengo wa apulo, iwo uzibala mapeyala. Iwo uyenera kutero, chifukwa utomoni, moyo mwa iwo, nyongolosi ndi mtengo wa peyala. Chabwino.

Ndiye, zochita zathu zonse ziyenera kumafotokozera Iye.

464 Ife tiri nalo Dzina Lake. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ife tiyenera kunyamula Dzina Lake.

465 Ndipo kumbukirani, ife tiri tsopano, monga Mkwatibwi Wake, titapatsidwa pakati ndi Mzimu Wake. Oh, mai! Mpingo, wobala ana, mwaona, wapatsidwa pakati ndi Mzimu Wake ndi Dzina Lake; ukubala Dzina Lake, ukubala Moyo Wake; kumabweretsa zizindikiro za Moyo Wake, mwa umboni ndi uyambiriro, umboni wa chiwukitsiro Chake; kusonyeza kuti Iye si wakufa, koma wamoyo kwanthawizonse. Uwu ndi Moyo Wamuyaya, ndipo watsimikiziridwa, kutsimikizira kwa dziko kuti ife tiri amoyo mwa Iye. Psyii!

466 Iwe umadziwa bwanji, chifukwa ndiwe membala wa mpingo? Chifukwa, Khristu akukhala moyo kudzera mwa iwe, wopatsidwa pakati kwambiri ndi Mzimu Wake kuti iwe—ndiwe wamndende kwa china chirichonse. Iwe watsekeredwa, oh, mai, ku Uthenga, watsekeredwa ku Mawu, ndipo ana onse amene iwe ungakhoze kuwabala ndi amenewo, chifukwa ndiwe wamndende.

467 Iwe sungakhoze kuchita chigololo; ndiwe wopatsidwa kale pakati. Ulemelero! Iye sangakhoze kukugwira. Chiberekero cha moyo chinatsekedwa kwa china chirichonse. Ndiwe Wake kale, mwa kukonzedweratu. Mbewu imeneyo yabwera ku Moyo; palibe dziko lingakhoze kulowa mkati. Oh! Oh, momwe ife tikufunira tikanakhala pa izi kwa pafupifupi ora! Ine ndikutsimikiza inu mukumvetsa. Mukuona? Khristu, ndi Ake okha, zatsirizidwa kale. Mbewu inali mmenemo. Mbewu inali, kale. Ndi liti limene iyo inaikidwa mmenemo? "Asanaikidwe maziko a dziko lapansi, anatikonzeratu ife ku Moyo Wamuyaya." Ndipo mwamsanga pamene kupereka Moyo kuyenderera, Mbewu imeneyo itakhala pamenepo. . .Mbewu zina zomwe zingabwere mmenemo, sizingakhoze kugwira, sizingakhoze basi kuchita izo, mofanana. Koma pamene Mbewu iyo inabwera mmenemo, mwamsanga iyo inatseka chiberekerocho; mbewu zina zonse zinatulutsidwamo, mwaona, monga chomwecho.

468 Ndipo iwe unadzakhala wamndende, wotchingiridwa, mwa Khristu. Khristu mwa iwe, Moyo Wake ukubweretsa umboni Wake, zizindikiro Zake. Oh, mai, mai, mai! Taonani, kubweretsa zizindikiro Zake za Moyo monga umboni wa chiwukitsiro Chake, kutsimikizira kwa dziko Moyo Wamuyaya umenewo, kutsimikizira kwa dziko kuti ife tiri amoyo mwa Iye. Ndipo taganizani za zimenezo, amoyo ndi Mulungu, Muwomboli wathu, Yemwe anatilenga ife kwa cholinga chomwecho kumene, Mpingo, ndi Moyo Wake wolenga mwa ife.

469 Ndiko kuti, Mose akanakhoza kunena, mwa Mawu a Mulungu, "Pakhale chakuti," ndipo apo panabwera ntchentche. Mulungu yemwe angakhoze kupanga ntchentche akhoza kupanga agologolo. Mukuona?

470 Iye akhoza kuchita chirichonse chimene Iye akufuna. Iye akhoza kulenga. Iye akhoza kuchita chirichonse. Iye ndi Mulungu. Mulungu yemwe yemweyo, Moyo wolenga uja, inu mukuona, umene uli mwa inu, ukhoza. . .Ndinu wamndende; inu simungakhoze kuyankhula izo mpaka Iye atanena kuti yankhula izo. Koma, pamene inu mwayankhula, ndi Mawu a Mulungu. Iye wazitsimikizira izo kuti ziri chomwecho. China chirichonse ndi cholondola, ndipo Iye amadziwa, pamene izo zayankhulidwa, izo ziyenera kukhala chomwecho. Mukuona?

471 Mose anatenga ndodo yake, ndipo anati, "Apo pabwere achule," chifukwa Mulungu anati, "Apo pabwere achule." Iye

anangowafalitsira iwo kunja. Ndiko kulondola. Ndipo achule anali mu chirichonse, paliponse panali achule. Kodi iwo anachokera kuti? Palibe yemwe akudziwa. Iwo kunali kulibeko uko poyamba. Koma Mlengi, Mulungu, akugwira ntchito kudzera mwa munthu, analenga zinthu, mitundu yamoyo.

472 Mulungu yemweyo amene anapanga chule woyamba akhoza kupanga chule wachiwiri. Iye amapanga achule onse. Oh, mai! Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Anapanga gologolo woyamba, akupanga gologolo wachiwiri, akupanga gologolo aliyense; akhoza kupanga agologolo pamene palibepo agologolo. Iye akhoza kuchita chirichonse chimene Iye akufuna kuchichita! Iye ndi Mulungu! Iye ndi Mulungu! Moyo Wake! Oh, mai! Pamene ine ndilingalira za zimenezo, zimandipangitsa ine tsemwe! Uh-huh.

473 Oh, kukhala moyo ndi Iye, kumapita Kwathu ndi Iye, kukakhala moyo ndi Iye! Kumapita Kwathu ndi Iye kumakakhala ndi Iye kwanthawizonse, kumakhala nawo Moyo Wamuyaya!

474 Ichi ndi chinsinsi chachikulu cha Mulungu cha chikondi chofotokozedwa, kuti Mulungu ndi munthu anadzakhala mmodzi. Mukuona? Chinthu chonsecho ndi Mulungu ndi munthu, mmodzi. Mulungu ndi munthu anali mmodzi, uko; ndipo Mulungu ndi munthu ndi mmodzi, kuno. Mukuona? Ndi chiyani chimenecho? Kudzazidwa ndi Mzimu Wake, Iye kukhala nawo uyambiriro. Uko kunali kupindula kwa Mulungu, ndicho cholinga cha Mulungu kuti achite zimenezo: kuti Iye adzakhoze kukhala ali mwa Khristu; ndi Khristu mwa ife; ndi tonse ife pamodzi, mmodzi. Mzimu Woyera, chinthu chomwe chomwecho; Iwo unaulula izo kwa Khristu, ukuwulula izo kuno; Mphamvu yolenga yauzimu. Oh, mai!

475 Mulungu yemweyo yemwe anakhoza—yemwe anakhoza kunena izi zonse mwa Mose, "Apo pabwere achule," Mmodzi yemweyo anakhoza kuima pajapa, "Apo madzi awa asanduke vinyo." Mukuona? Ameni. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Iye ndi Mulungu yemweyo, Mmodzi yemweyo.

476 Iye samasintha basi. Ndi Mulungu mwa munthu. Ndiwo mawonetseredwe Ake. Ndicho chimene Iye akuwulula. Ndicho chimene Iye akuyesera kuti azichita, ndipo Mawu a Mulungu kumene akuwulula Izo. Zikusonyeza kuti munthu sangakhoze kulenga; Mulungu ndiye Mlengi. Ndipo uyo si munthu aponso; ndi Mulungu Mlengi, mwa munthu, umene uli Mpingo Wake tsopano. Ameni!

477 Kupita Kwawo Kumwamba, kukakhala ndi Iye, nthawizonse. Mulungu akufotokoza chikondi Chamuyaya kwa Mpingo.

478 Mvetserani, mvetserani mwatcheru tsopano. Ine ndikufuna kuti inu musalephere kuzimvetsa izi. Palibe mpingo wina, palibe chizindikiro china, palibe chiyanjano china, palibe boma lina, palibe umboni wina, palibe kachikhulupiriro kena, palibe chipembedzo, chiri cholandiridwa kunja kwa Ichi. Mulungu samalandira kanthu kenanso koma zimenezo, "Khristu mwa inu, chiyembekezo cha Ulemelero," chinthu chokhacho chimene Mulungu amachizindikira. Palibe chiyanjano, palibe mpingo, palibe kachikhulupiriro, palibe chipembedzo, palibe kanthu; china chirichonse ndi chakufa. Nsanza zake ziyenera kuti zidulidwe nkuchotsedwapo, kusazidwa nkuchichotsa kwa chinthucho, kuti Khristu akhoze kumakhala moyo ali ndi uyambiriro mwa inu.

479 Osati kulozera mmbuyo! Ine ndiri ndi mwendo umodzi apa, umene umati, "Ndi bungwe langa." Umenewo uyenera kuti udulidwe, aponso. "Ine ndiri ndi *wakuti-ndi-wakuti* wanga pano. *Uyu* amanena izi. Mayi anga andiuza ine kuti ndine woyera wodzigudubuza." Izo ziyenera kuti zidulidwepo, nazonso. Mukuona? "Chabwino, ine ndikudziwa amuna anga akufuna kuti ine ndizivala zazifupi izi." Zimenezo ziyenera kuti zidulidwepo, nazonso. Mukuona? Izo ziyenera kuti zidulidwepo ndi kutengulidwa mpaka apo mungokhala inu ndi Khristu, yekha. Mukuona? Uh!

480 Taganizani! Mwa Kukhalapo kwamoyo kwa Khristu wamoyo mwa Mawu amoyo; oh, Khristu wamoyo, Kukhalapo kwamoyo, Mawu amoyo! Penyani! Mwa umunthu Wake Womwe, kutsimikizira kwayekha kumawutsimikizira Mpingo Wake.

481 Osati mamembala! Iye sanachitepo konse zimenezo, masiku a Mose. Iye sanachite konse izo mmasiku a wina aliyense; pa mapeto a dziko lapansi, pamene izo zinafika pamalo pamene kunali chiwonongeko. Masiku a Loti, siunali umembala. Zinali kutsimikiziridwa kwa payekha, Mulungu mu thupi, mwaona, kutsimikiziridwa kwa payekha.

482 Kumbukirani! Taganizani za zimenezo, kuti, anthu obadwa ndi Mzimu Wake, mu tsiku monga ili, mu m'badwo wa chipembedzo wawukulu uwu umene ife tiri kukhalamo, ndipo Mulungu wamoyo akumatenga Mawu Ake amoyo ndi—ndi kumawatsimikizira iwo, yekhayekha, Moyo uwu umene uli mu Mawu, nyongolosi imene ili mu Mbewu! Ndipo Mawu ndi Mbewu imene wofetsa anapita kukafetsa. Ndipo Moyo ndi Khristu, mu Mawu, yekhayekha mwa inu; akutsimikizira chinachake chimene inu simungakhoze kuchichita, akudzitsimikizira Yekha kuti si inuyo, koma ndi Iyeyo. Ndipo inu mukukhala mmodzi, wa—wa—kapolo wa chikondi kwa Iye, kuti mukhale Mkwatibwi.

483 Mathokozo akhale kwa Mulungu wamoyo Yemwe analenga kumwamba ndi dziko lapansi ndi zonse zimene ziri mkatimo!

Nzosadabwitsa, “Iye ndi Alfa ndi Omega, Chiyambi ndi Mapeto; Iye yemwe anali, yemwe alipo, ndipo adzadza; Muzu, ndi Mphukira ya Davide; Nyenyezi ya Nthanda ndi yowala.” Iye ali zonse-mu-zonse.

484 Kukhalapo Kwake, mwa munthu payekha, ndi kutsimikiziridwa kwapayekha kwa Iyemwini akudzifotokoza Iyemwini, Mawu amoyo amene alonjezedwera kwa tsikuli, akudzifotokoza Iwoeni kudzera mwa inu, kutsimikizira kwa vumbulutso lalikulu la Mulungu. Tayang’anani, mwa aliyense payekha payekha, osati mwa chigulu! Aliyense payekha payekha; osati mu chigulu! Kuzindikiritsa Kwake ndi kwa aliyense payekha. Inu mukumvetsa zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Osati ndi Amethodisti, osati ndi Abaptisti, osati Apresbateria, osati Achilutera, osati Achipentekoste, koma monga aliyense payekha!

485 “Ine ndidzatenga mmodzi, ndi kusiya mmodzi; Ine ndidzawalekanitsa iwo.” Ndiko kulondola. “Iwo adzakhala ali awiri mmunda; Ine ndidzamtenga mmodzi ndi kumusiya mmodzi. Adzakhala awiri pa bedi, ndipo Ine ndidzamtenga mmodzi ndi kumusiya mmodzi.”

486 Si chigulu ayi. Iko ndi kutsimikizidwira kwa aliyense payekha kwa mwana wopatsidwa pakati ndi Mulungu, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, wodzipereka kwambiri kwa Mulungu kuti iye samasamala za china chirichonse. Ndipo Mzimu Woyera ukukhala Moyo Wake, ukututuma kupyolera mwa iye, kusonyeza kutsimikiziridwa kwa aliyense payekha—aliyense payekha kwa Mawu, Iwoeni, akudzifotokoza Okha kwa anthu ndi kwa dziko lapansi.

487 Dziko lingakhoze bwanji mwakhungu kumayenda cholambalala ndi chinachake chonga icho? Mofanana basi monga Akatolika ankayenda momulambalala Patreki Woyera ndipo sanamuzindikire iye mpaka iye atafa. Chinthu chomwecho iwo anachita ndi Marteni Woyera, sanazizindikire izo. Chinthu chomwecho iwo achichita mu mibadwo yonseyo.

488 Chinthu chomwecho chimene iwo anachita ndi Joan waku Arc. Mpingo wa Katolika unamuwotcha iye, ngati mfiti, chifukwa iye anali wauzimu. Pafupifupi zaka handiredi fifite kenako, anafukula thupi la ansembe amenewo ndipo anawaponyera iwo mkati, kuti aziwachitira kudzitunduza.

489 Izo zikumapita mowalambalala iwo, ndipo iwo samazizindikira izo mpaka izo zitapita. Izo zimangotenga Mbewu yokonzedweratu imene Mulungu anaikonzeratu asanaikidwe maziko a dziko lapansi. Chinthu chomwecho chinadzabwera kudzadutsa mmasiku a Nowa, chinthu chomwecho chinabwera kudzadutsa mmasiku a Mose, masiku a Eliya, masiku a aneneri, masiku a Yesu, mpaka mmusi kumadutsa ndi mpaka mu ora ili lomwe. Munthu

wopatsidwa pakati ndi Mbewu ya Mulungu, Mawu mkatimo akudziwonetsera Wokha, odzipereka kwambiri ku chifuniro cha Mulungu kuti Mawu, ndipo Mawu okha, azidziwonetsera Wokha mwa munthu uyu, wamndende, kwa aliyense payekha.

490 Osati kumati, "Mpingo wanga . . ." Tsopano, "mpingo wanga" ulibe kanthu kochita ndi izi.

491 Ndi aliyense payekha, munthu mmodzi! Gehena yense ikutsutsa Kuphunzitsa uku. Gehena yonse ikutsutsa Choonadi ichi, koma icho ndi Choonadi.

492 Yesu sananene konse, "Tsopano, Petro, iwe ndi Yohane, ndi anthu ena onse, inu muli nalo vumbulutso, tsopano mpingo wonse ndi wopulumutsidwa." Ayi.

493 Izo zinali kwa iye, payekha. "Ine ndikuti kwa iwe, iwe," osati kwa iwo, "kwa iwe, iwe ndiwe Petro; pa thanthwe ili ine ndidzamangapo Mpingo Wanga." Ndipo mawu akuti *Petro*, amatanthauza "mwala." *Mwala* umatanthauza "iye wovomerezedwayo," kapena, "iye wopatulidwayo."

494 Pa mwala winawake, pa chinthu chinachake; mwaona, oyitanidwa-atuluke, Mpingo woyitanidwa utuluke; pa *mwala* uwu, pa ili "vumbulutsolo." "Thupi ndi mwazi sizinaulule konse izi kwa iwe. Koma pa vumbulutso ili, gulu loyitanidwa-lituluke, Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga mwa iwo. Ndipo zipata zonse za gehena sizidzakhoza konse kuwulaka iwo."

495 "Palibe tsitsi limodzi la mmutu mwanu liti lidzatayike. Inu ndinu Anga! Ine ndidzakuwukitsani inu mu tsiku lotsiriza, ndinamupatsa iye Moyo Wamuyaya, ndipo ndidzamuwukitsa iye pa masiku otsiriza." Ndi zimenezotu apo, vumbulutso. Osati iwo; koma "iye," aliyense payekha! Osati gulu; aliyense payekha! Gehena yense imatsutsana ndi zimenezo.

496 Koma chinsinsi Chake chimawululidwa kokha kwa Mkwatibwi Wake wokondedwa. Ndi iye yekha angakhoze kuziwona izo.

497 Iye anati, "Yesaya anayankhula bwino za inu, inu achinyengo, inu njoka mu udzu. Inu mumapita kunja uku ndi kukati, 'Oh, aneneri oyera aakulu! Ife tiyenera tikaike chizindikiro pa manda awo. Ife tikawapukute iwo.'" Iye anati, "Inu ndi omwe munakawaika iwo mmenemo." Kodi Iye ananena zimenezo?

498 Chinthu chomwecho Iye ananena kwa mipingo ya Chikatolika mmasiku awo, pamene iwo anatumizidwira aneneri Akale—chipangano Chakale iwo asanakhale ndi Nicaea, Roma kumeneko, ndi osankhidwa. Aneneri akale amenewo anabwera uko, akudya zokumba ndi zinthu zochokera mu nthaka, opanda ngakhale kuvala zovala, ali ndi chikopa cha nkhosa mozikuta pa iwo, ndi kumayesera kuti aziyima ndi Choonadi icho cha Baibulo. Koma mpingo wa Katolika unkafuna lingaliro

lake laluntha. Ndiye iwo anatulukamo . . . Uko kunadzabwera Ireniasi Woyera, Polekapu, Marteni, ena onse a iwo. Ndipo kodi iwo anachita chiyani? Iwo anawaika iwo mmanda, Joan waku Arc, Patreki Woyera, ndi ena onse a iwo. Iwo anawaika iwo mmenemo, tsopano anadzabwerera mmbuyo ndi kudzayeretsa makomawo monga iwo anachitira ndi Joan waku Arc. Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anawaika iwo mmenemo!

499 Ndiye ine ndikuti, monga Mzimu Wake ukukutchani inu, "Makoma oyeretsedwa! Inu achinyengo, mumadzitcha nokha chinachake, pamene inu mukutenga lingaliro laluntha la munthu, ndi kumawasiya Mawu azipita. Mmalo moti mupatsidwe pakati ndi Mbewu ya Mulungu, Mawu mwa inu, inu mwatenga haibridi iliyonse." Nzosadabwitsa iye wakhala monga "hule," chifukwa iye "akuchita ziwerewere zauzimu," kuwaphunzitsa anthu zinthu za munthu ndipo osati zinthu za Mulungu.

500 Koma Iye anati, "Musawope ayi, gulu lapang'ono, ndi chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu Ufumu." Ndiko kulondola. Ndithudi. Pamenepo ife tiri nazo izo.

501 Baibulo, mu Chivumbulutso, linati, "Mzinda waukulu uwu unkalamulira pa mafumu onse a padziko lapansi." Linati iye anati "hule." Ndi chiyani chimenecho? Mkazi yemwe amadzitcha kuti ndi dona ndipo nkumachita chiwerewere. "Iye anali ndi chikho mdzanja lake," chopangira toasti, kwa dziko lapansi, "cha . . . chodzaza ndi zonyansa za themberero la ziwerewere zake." Ndipo anali nawo ana aakazi, mipingo ya Chiprotestanti, omwe wina aliyense amachokera kwa iye ndi ziphunzitso zake zomwezo zabodza, maubatizo omwewo, ndi pa kugwirana manja, mmalo mwa ubatizo wa Mzimu Woyera; ndi chiphunzitso chawo chabodza cha "Atate, Mwana, Mzimu Woyera," ndi zonse zimenezo, mmalo motenga Dzina la Mkwatibwi . . . Mkwati, ndi zina zotero.

Inu mukuti, "Izo sizikupanga kusiyana kulikonse." Izo zikupanga.

502 Ngati nditalemba dzina langa pa cheke, ndi kuti, "m'busa," kwa "mtumiki," kapena zina zotero, icho sichingakhoze kulandiritsa kalikonse. Ndiko kulondola. Icho chikakanidwa ku banki. Uh-huh. Zindikirani. Chabwino.

503 Koma chinsinsi chonse ichi chiri kuululidwa basi, monga Iye analonjezera kwa Mkwatibwi Wake. Gehena ikutsutsana nacho Choonadi ichi, cha vumbulutso la chinsinsi ichi. Koma Mkwatibwi akuima pa ilo. Ndi Iyeyo wayima.

504 Nchifukwa chiyani inu mukuchita njala, Mpingo, nchifukwa chiyani inu mukuchita ludzu? Ndi Atate akuyesetsa kuti awululire chinsinsi chobisika ichi kwa inu. Koma inu mukulola zinthu zochuluka kwambiri kuti zichotse icho mwa inu. Inu mukulola ntchito yanu, inu mukulola mkazi wanu, inu

mukulola mwamuna wanu, inu mukulola ana anu, inu mukulola zosamalira za mdziko, inu mukulola m'busa wina, inu mukulola munthu winawake kuti achotse icho mwa inu, pamene inu mukudziwa mwanjira imeneyo pansi mu mtima mwanu inu mukuchita ludzu, mukuchita njala. Ndi Mulungu akuyesetsa kuti awululire izo kwa inu, mwaona, vumbulutso. Tsiku lotsiriza liri pano. Zindikirani tsopano.

505 Tiyeni tiyang'ane mmbuyo kachiwiri. Ine sindingakhoze kuzidutsa zonse izi. Mukuona? Ine ndikungofuna kuti inu muyang'ane pano miniti yokha tsopano, ndipo ife titseka mu maminiti pang'ono okha. Inu mukhala muli . . . Mungondipatsa ine tcheru chanu chosagawanika kwa miniti.

506 Zindikirani, Akolose, ndime ya 18 pano. Mu Bukhu la Akolose, ndime ya 18.

> Tsopano *iye ali mutu wa* mpingo, thupi: *yemwe ali chiyambi, woyamba kubadwa kwa akufa; kuti mu— kuti mu zinthu zonse iye akakhoze kukhala nawo* mauyambiriro.

507 "Iye ndiye Mutu wa Mpingo, umene uli Thupi Lake, ndipo Iye akufuna mauyambiriro." Mvetserani tsopano, mvetserani mwatcheru pamene ife tiri kupita. Chiyani? Iye ali woti akhale Mutu wa Thupi, Thupi la Mkwatibwi Wake, limene liri lotengedwa kuchokera kwa Iye; mnofu ndi fupa, monga mwa Adamu, mwaona, Mkwatibwi.

508 "Wobadwa kwa akufa," mwaona, ndiwo, obadwa kwa akufa, tchimo la kusakhulupirira.

509 Nchiyani chinamupha Eva? Kusakhulupirira. Nkulondola uko? Kusakhulupirira kwawo mu chiyani? Mwa, chifukwa cha- . . . kusakhulupirira mwa Mulungu? Ayi. Iye anali nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Zedidi. Kodi iye anati, "Kulibeko Mulungu"? Ayi, bwana. Iye sanali wachikunja. "Chabwino," iye anati, "inu mukudziwa, ine sindikukhulupirira Mawu Ake nkomwe"? Oh, ayi. Iye amakhulupirira onse koma kanthu kamodzi kakang'ono. Mukuona?

510 Tsopano kodi Baibulo silinanene, uko mu Bukhu la Chivumbulutso, Yesu ananena Mwiniwake, "Ine—Ine Yesu ndamutuma mngelo Wanga kuti adzachitire umboni zinthu izi kwa inu"? "Yense yemwe ati adzachotse Mawu amodzi kwa Iwo, kapena kudzawonjezera mawu amodzi kwa Iwo." Ndipo ngati kupweteka kwa mtima konse uku ndi chisoni zinabwera chifukwa mkazi anakaikira Mawu amodzi a Mulungu, kodi Iye angakulolenì inu mmbuyo muno kuti muzikaikira Mawu amodzi? Iye angakhale wosalungama. Uh-huh. Mukuona? Mwaona, zimenezo sizingakhale zolondola. Adzatsutsidwa . . .

511 Pano pali munthu mmodzi ataima, ndipo iye anayambitsa kupweteka kwa mtima konse uku chifukwa cha mawu amodzi atakaikiridwa; ndiye iye akupitirira ndi kumatenga

zaka za kujayira ndi chirichonse, ndi Baibulo ndi zina zotero, ndi ena amene anapereka miyoyo yawo chifukwa cha izo; ndiye nkudzati, "Oh, inu mukhoza kupitirira ndi kumakadya izo. Izo zonse ziri bwino, Ine ndikulolani inu mubwerere, mulimonse"? Oh! Mulungu samalemekeza munthu, koma...?...Mukuona? Mukuona? Mulungu samalemekeza munthu. Tsopano zindikirani.

512 Zindikirani tsopano. "Iye ndiye Mutu wa Thupilo" amene anabadwa kuchokera ku tchimo, la kusakhulupirira mu Mawu a Mulungu. Izo zik-. . .izo zikuchotsapo chipembedzo chirichonse, kachikhulupiriro kalikonse, mwaona. Kusakhulupirira mu Mawu; omwe ali Iyemwini, Mawu a Moyo. Mukuona? Mawu, okha, ali nawo Moyo. Mawu ena aliwonse ndi haibridi. Ziribe kanthu mochuluka bwanji iwo akuwoneka ngati Iwo, iwo si Mawu.

513 Mawu amabala Moyo Wake Womwe, umene Eva anasinthanitsa ndi nzeru zayekha. Mukuona momwe mpingo wachitira, lero? Kupyolera mu kumvetsa kwa munthu wina. Mose anali nako kumvetsa kwakukulu kwa Mulungu mpaka iye atakomana ndi chisamba chonyeka, atatero iye anawona kulephera kwake. Chisamba chonyeka chinali ndi chimene Mose ankachisowa. Mawu ali nacho chimene chipembedzo chikusowa.

"Iye, Mutu, ndiye zipatso zoyamba za chiwukitsiro."

514 Ife tipita ku ili, "vumbulutso"; kanthawi kakatali pang'ono, ngati inu mutanene chomwecho. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino. Chabwino, kulondola, pang'ono pokha tsopano.

515 "Iye ndiye zipatso zoyamba za chiwukitsiro." Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Tapenyani. Ndiye, kodi Iye ndi chiyani? "Iye ndiye Mutu wa Thupi, umene uli Mpingo Wake, Mkwatibwi." Uh-huh.

516 Ndiye, Thupi la Mkwatibwi liyenera kumatsatira Mutu, pakuti ilo ndi gawo la chiwukitsiro Chake ndi gawo la chinsinsicho. Ndi zosatheka kuti ilo lisapite. Oh, mai! Ilo ndi gawo la chinsinsi cha Mulungu, momwe Mulungu anadziululira Yekha kuno ndi kuliwukitsa ilo ndi Mawu, chotero Iye akuwuwulula Mpingo Wake ndi kuwuwukitsa Iwo ndi Mawu omwewo. Iwo ndi gawo la chinsinsi Chake chofutukuka patatu.

517 Monga Mutu unatengedwa kuchokera mmanda, chotero liyenera Thupi kumutsatira Iye kubwerera ku Edeni. Kumene, Mutu wa banja, Mwamuna, Mkwati; Mkwatibwi pokhala Thupi la Mkwati, liyenera kutsatira, Mkwatibwi, chifukwa ndiye Mutu. Ndipo Mutu waululidwa, ndipo wabwerera ndi Moyo Wamuyaya; ndipo Thupi liyenera kutsatira iwo, chifukwa iwo ali Mwamuna ndi Mkazake kachiwiri. Ameni! Ndipo bola ngati inu mwapatsidwa pakati ndi Mawu omwewo, amene ali Thupi

Lake; inu mwatenga Thupi Lake, nkudzakhala mwa Iye, pamene inu munatenga Mawu. Osati kachikhulupiriro; Mawu! Oh, mai!

518 Kodi zimenezo sizikanapanga mutu wa madzulo ano, kuti tipeze popitirira napo? Huh? Mai, kodi zimenezo sizikanakhala zodabwitsa? Mukuona? Tangolingalirani za zimenezo tsopano, chimene izo ziri.

519 Chotero, Thupi silingakhoze kuzindikira . . . Inu musalephere izi. Thupilo, chotero, silingakhoze kuzindikira utsogoleri wina uliwonse koma Mawu. Chifukwa, m—Mutu walumikizana ndi Thupi, ndipo Mutu ndi Mawu, ndipo ndi Mawu omwewo, Mutu umodzi! Chotero, zipembedzo, ndi abambo oyera, ndi china chirichonse, ndi ndowe zakufa. Ulipo Mutu umodzi, ndiwo Khristu. Thupi limazindikira chinthu chimodzi chokha, Mawu!

520 Tsopano ndisonyezeni ine pamene winawake anabatizidwira, mu Thupi, mu dzina la "Atate, Mwana, Mzimu Woyera"? Ndipo kodi inu mukuzindikira chiyani? Mwaona, ine ndikuzindikira kuti ndikuyankhula kwa zikwi, pa tepi, inu mukudziwa, ndipo ife tiri nawo utumiki wa pa tepi kuzungulira dziko lapansi. Kodi inu mumabatizidwa mu dzina liti? "Pakuti palibe dzina lina linapatsidwa pansi pa Kumwamba," anatero Mawu, "limene munthu angakhoze kupulumutsidwa nalo." Ngati munabatizidwa, kuti mudzasonyeze chikhulupiriro chanu mwa Khristu, ndipo kenako nkudzatenga dzina la kachikhulupiriro, ndiye ndinu haibridi. Ngati sindinu ndendende monga mpingo uja ndi ndendende monga kuphunzitsa kwawo . . .

521 Ndiye, inu anthu Achikatolika, mwaona, inu mungakhoze bwanji kupita pansi pa ulamuliro wa papa tsopano, kumanena kuti iye ndi wolowa mmalo mwa kuloweza mmalo kwa utumwi, kuchokera kwa Khri- . . . kuchokera kwa Petro, ndipo papa uyu ndi mpingo uwu umaphunzitsa mosiyana kwambiri kwa Mawu oyambirira awa amene Mulungu anawazindikira, mwa zizindikiro ndi zodabwitsa, kuti ndiwo Mpingo Wake? Ndipo kuwawona Mawu omwewo akubweretsedwapo lero mu ungwiro Wake, akusonyeza chiwukitsiro chomwecho chimene Iye anali nacho uko, Mulungu akukhala moyo pakati pa anthu Ake, kumachita zinthu zomwezo, ndiye inu mungakhoze kuzindikira utsogoleri mu Roma?

522 Utsogoleri wathu uli Kumwamba. Ine sindikupita ku Roma; ine ndikupita Kumwamba pamene ine ndidzafa. Mukuona? Mukuona? Utsogoleri uli Kumwamba.

523 Ndipo Thupi liyenera kumatsatira Mutu, monga mkazi amamutsatira mwamuna wake. Pokhala kuti Adamu sananyengedwe, iye ankayenda ndi Eva. Eva ananyengedwa, iye anali mu kulakwa, kapena chiwukitsiro chonse cha Thupi lonse chikanatulukira pa tsiku la Ambuye Yesu pamene Iye

anatulukira kuchokera mmanda. Koma Iye ankayenera kuti amuwombole Iye, yemwe ali Thupi Lake. Iye ayenera kuti awomboledwe pofuna kuti adze kwa Iye. Kodi inu mukuziwona zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Oh mai! Mukuona, izo sizikanachitika nthawi imeneyo. Chiwombolo chikupitirirabe.

524 Tsopano inu mukuziwona Zisindikizo? Pamene Iye anali mu ntchito Yake ya umkhalapakati kumbuyo uko, akuwombola, koma tsiku lina Iye adzabwera kuti adzatenge Bukhu ili limene Iye analiwombola. Ndipo onse amene ali mu Bukhu ili adzakhala Iye, pakuti ameneyo ndi wokhulupirira, mawu a mu Bukhu, ndipo Mawu ndiwo Iye. Ndipo onse amene ali mmenemo, Iye akudzera Bukhu ili la Chiwombolo, omwe maina awo analembedwa mu Bukhulo asanaikidwe maziko a dziko lapansi, pamene Iye anaphedwa ngati Mwanawankhosa.

525 Ndipo pano Iye ali lero, mu Mawu Ake, akuwonetsera chinthu chomwecho chimene Iye anachichita kumeneko. Iye sangakhoze kuzindikira utsogoleri wina. Ayi, bwana. Kulibeko bishopu, kulibeko kanthu kena. Iye akuzindikira Mutu umodzi, ndiwo Khristu, ndipo Khristu ndiye Mawu. Oh, mai! Psyii! Ine ndikuzikonda zimenezo. Uh! Inde, bwana.

526 Monga Mutu unatengedwa kuchokera kumanda, chotero liyenera Thupi Lake kumamutsatira Iye mpaka mu Edeni. Chotero, Thupi silingakhoze kuzindikira utsogoleri wina uliwonse, koma Utsogoleri wa Mawu.

527 Palibe chipembedzo chingakhoze kuyika chirichonse kwa Iwo. "Pakuti aliyense yemwe adzachotse Mawu amodzi kuchokera kwa Iwo, kapena kudzawonjezera mawu amodzi kuchokera kwa Iwo, adzachotsedwa kwa Iwo." Ndinu akufa, haibridi, pomwe apo. Iye wabwerera kuno, umboni uwu uli mmanja mwake, "nyansi za ziwerewere zake, akuchita chigololo chauzimu," motsutsa Mawu omwe amene iye akudzinenera kuti akuwakhulupirira. Mukuona?

528 Chotero, ndi Mawu, kapena palibepo. Ndiko kulondola. Iye, Mawu! Inu mukudziwa bwanji kuti ndi kulondola? Iye, Mawu, akutsimikiziridwa. Mukuona? Iye, Mawu, atatsimikiziridwa bwinobwino, ndiwo Mutu, Mutu wa Mpingo. Iye ndi Mawu, Mutu. Iye akuzindikiridwa bwinobwino, kuzindikiritsidwa, kutsimikiziridwa, ndi Mzimu Wake Womwe kuti ali mu Mpingo Momwemo, munthuyo. Akudzisonyeza Mwiniwake, mu kutsimikiziridwa, ndi umboni wolunjika kwa Thupi lonse. Inu simukusowa tizikhulupiriro, pamenepo. Zipembedzo zawonongeka. Koma Mutu Iwoweni, ukuzindikiridwa mu Thupi mwa kuzindikiritsidwa kwa aliyense payekha, mwaona, kudzizindikiritsa Yekha, kutsimikizira Mutu kwa Thupilo. Ndiye, ife talumikizana pansi pa Mutu Umodzi wotsimikiziridwa, umene uli, Khristu, Mawu a Mulungu [Malo

osanjambulidwa pa tepi—Mkonzi]. osati pansi pa mpingo uliwonse.

529 Zikatero, Mutu wathu ndiwo Ufumu. "Ufumu wa Mulungu uli mkati mwa inu," linatero Baibulo, Yesu. Ufumu! Ife sitiri chipembedzo. Ife ndife a Ufumu, ndipo Ufumu ndiwo Mawu a Mulungu atapangidwa Mzimu ndi Moyo mu umoyo wathu womwe, kubweretsa pochitika lonjezo lirilonse mu tsiku lino, monga izo zinkachitikira mu tsiku lija pamene Mawu ndi Mulungu anali Mmodzi. Ndipo Mawu ndi Mulungu ali mmodzi mu Mpingo Wake lero, kuwapanga Iwo Mutu wa Thupi limene liri lowomboledwa, kuti zibweretse Uthenga mu tsiku lotsiriza; ndi kutengedwera mmwamba kuchokera kwa akufa, mu chiwukitsiro, kuti abwerere ndi kumubwezeretsa kachiwiri, monga Adamu ndi Eva, pachiyambi mmunda wa Edeni. Chinsinsi chofutukuka patatu cha Mulungu, Thupi Lake! Oh, mai!

Zindikirani mwatcheru tsopano, monga mu zoyimira, Israeli wakale. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

530 Kodi ine ndikutenga nthawi yochuluka pa zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Musandirole ine, musandirole ine ndipitirire mochuluka . . . Tsopano tamvetserani. Tsopano ife tiribe koma pafupifupi masamba ena twente. Mukuona? Mukuona? Koma tsopano ine . . . Pang'ono pokha tsopano, ndiyeno—ndiye ine ndikusiyani inu nonse mupite mpaka chirimwe chinacho, kapena nthawi ina, ngati Ambuye alola. Mukuona?

531 Tsopano tayang'anani. Zindikirani tsopano, olumikizidwa palimodzi pansi pa Mutu umodzi, mwa khalidwe lomwelo, choyimira cha Israeli wakale. Tsopano kodi inu mukuzimvetsa zimenezo? Monga Israeli wakale; Mulungu mmodzi, wotsimikiziridwa ndi Lawi la Moto, ndi kumadziwulula Yekha kupyolera mwa mneneri, kuti ali Mawu. Mulungu yemweyo, Lawi la Moto lomwelo, mwanjira yomweyo; Iye sangakhoze kusintha njira Zake. Kodi ndi . . . Zangwiro basi monga izo zingakhoze kukhalira. Sichoncho izo? Mukuona? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

532 Mulungu mmodzi! Kodi ndi Amulungu angati amene Israeli anali nawo? [Osonkhana akuti, "Mmodzi."—Mkonzi]. Kodi ndi angati amene Mkwatibwi ali nawo? ["Mmodzi."] Adzakhala alipo angati konse? ["Mmodzi."] Zedi. Zedi.

533 Mwaona, pansi pa utsogoleri wa Mzimu Woyera, umene unali Lawi la Moto mmasiku a Mose, mneneri wamkulu. Iye anali kutsogozedwa ndi Lawi la Moto. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino. Akupita ku dziko lolonjezedwa.

534 Ndipo mu m'badwo wa Chikhristu, munali Mulungu mmodzi yemwe anawonekera mu mawonekedwe a Lawi la Moto, kwa

mneneri wotchedwa Paulo, yemwe anatumidwa kwa Amitundu, kuti akatenge anthu atuluke a Dzina Lake. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

535 Ndipo mmasiku otsiriza, wabweranso mwa chikhalidwe chomwecho, akudzitsimikizira Yekha, mwaona, mwa chizindikiro chomwecho, zodabwitsa zomwezo, Lawi la Moto lomwelo, Uthenga womwewo, Mawu omwewo, mawonetseredwe omwewo.

536 Thupi Lake lizichita ntchito zimene Iye analonjeza, monga mu Marko 16, ndi mwina motero. Thupi Lake silinagwidwe mmanda, koma linazindikiridwa ndi Iye mu chiwukitsiro. Kodi inu mukumvetsetsa zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndiye, Thupi la ana Ake okhulupirira silidzagwidwa mmanda pamene Iye adzabwera, koma lidzazindikiridwa ndi Iye, chifukwa Iye anafera cholinga chakuti awukitse Mkwatibwi Wake, Thupi. Kuzindikiridwa, chifukwa ilo ndi Thupi Lake, chifukwa ndi Mawu. Ilo ndi lodzipereka kwathunthu kuchokera ku zinthu zachipembedzo, kwa Iye, ndipo Iye ndi Mawu. Mukuona? Ndipo ilo likuzindikiridwa ndi Iye chifukwa tsopano ife tiri nacho chipatso choyamba cha chiwukitsiro chathu, podziwa kuti ife tachoka ku imfa tapita ku Moyo, tadzakhala amndende Ake. Ndipo Mulungu, akutsimikizira kwa ife mwa Mutu waumunthu Wake kuti Iye ali yemweyo dzulo, ndi kwanthawizonse, pakuchita zinthu zomwe zomwezo kudzera mu Mpingo zimene Iye ankachita nthawi imeneyo, "Iye mwa ine, ndi Ine mwa Iye, mwa inu," inu mukudziwa, ndi zotero. Ndiko kulondola.

537 Thupi Lake silinagwidwe mmanda. Linazindikiridwa ndi Iye mu chiwukitsiro, mofanana monga Iye aliri tsopano, mvetserani, chimene chikutanthauza izi: Mawu Ake, chimene Iye ali, akhala akuyamba kuti aziwuka. Mawu, amene kumatsika kudutsa mu m'badwo wa Luther, Wesley, mwaona, ayamba kuwuka kupita ku mphamvu Yake; pamenepo Iwo anayamba kumasuntha, ndiye Iwo anasuntha pang'ono mowonjezera, tsopano Iwo akufika pakuti azindikiridwe. Mukuona? Penyani. Tsopano, akufika ku Moyo mu Thupi, ndiko kutsimikiziridwa kwakuti Mkwatulo uli pafupi. Pamene inu muwona Mutu ndi Thupi zikukhala Chimodzi, ndi chidzalo cha muyezo wa mawonetseredwe Ake, zikusonyeza kuti Thupi liri pafupi kuti lilandiridwe ku Mutu.

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka.

538 Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Iye wayamba kupereka Moyo kwa Thupi Lake, (chifukwa chiyani?) Uyo yemwe Iye wamuwombola. Ntchito ya kukhalira pakati yachitika, Iye akuwubweretsa Moyo Wake ku Thupi, mwa kutsimikiziridwa kwa Mkwatulo. Kumbukirani, tsopano, mu tsiku lotsiriza . . .

539 Ine—ine, ngati inu mungandilole, mungopirira nane pa izi kanthawi pang'ono pokha, tsopano—tsopano, izo zonse zikhala bwino. Ine sindikufuna kuti inu muphonye izi. Ine—ine, ndipo ine ndiyenera kuti—ine ndiyenera kuti nditenge tepi iyi tsopano, pokhala kuti ine ndinayambira cha penapake. Ndemanga yowonjezera yaikulu ina ndikufuna kuti ndiyipange, ngati ine ndingati ndisunthirepo pang'ono pa izo.

540 Tsopano zindikirani. Mvetserani kwa izi. Tsopano ndi chinthu chachikulu. Tsopano ndi pamene ife tikufuna kuti tiyang'anepo. Kumbukirani, mmasiku otsiriza, adzabwerera ndendende ndi kukatsimikizira tsiku loyamba; onani, Adamu ndi Eva, mwamuna ndi mkazake, opanda tchimo, Moyo; ndiye kugwako. Zindikirani, zindikirani mwatcheru.

Mugwedezeni iye. Uh-huh.

541 Zindikirani. Nchiyani chinayambitsa icho? Lusifara! Lusifara akuchita tsopano monga iye anachitira pa nthawi yoyamba.

542 Basi monga ufumu wa Amitundu unabweretsedwamo, ndi Mfumu Nebukadinezara, zinatsimikizira mtundu wa Amitundu mwa mneneri yemwe ankakhoza kutanthauzira malirime osadziwika, masomphenya, maloto. Ndipo izo zabwera mmusi kudzera mwa Amitundu, popanda chirichonse, Amedo-Persia basi, ndi chitsulo ndi zina zotero, ndipo kumapazi izo zikupita pakutha mwanjira yomweyo kachiwiri, ufumu wa Amitundu.

543 Zindikirani Lusifara, mmasiku otsiriza, akuchita monga iye anachitira poyamba. Kodi Lusifara anachita chiyani? Chinthu choyamba chimene Lusifara anachichita kuti alekanitse chiyanjano cha Mulungu ndi munthu, iye ankafuna kuti adzimangire iye ufumu wachigwirizano, wowala mokulirapo ndipo mwakuwoneka wotukuka mochulukira, ufumu wawukulu kuposa womwe Mikaeli, Khristu anali nawo.

544 Inu mwamva zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Tsopano, tsopano ngati inu mwaziphonya izi, mungokweza dzanja lanu, ine ndizinena izo kachiwiri, inu mwaona. Mukuona?

545 Lusifara, pachiyambi, cholinga chake mu mtima chinali kuti adzapindule chinthu chowalirapo ndi chokulirapo Kumwamba kuposa chimene Khristu anali nacho. Nkulondola uko? Mwa kuwoneka wotukuka kwambiri, wokongola kwambiri, wowala kwambiri, kuposa Ufumu wa Khristu. Kodi inu mukuganiza kuti ife tidzakakhala ndi magalimoto mu Zakachikwi, ndi ndege? Mukuona? Mwaona chimene Lusifara akuchita?

546 Tsopano, zipembedzo zazikulu zapamwamba zaluntha zikuchita chinthu chomwecho, akudzisonkhanitsa okha limodzi kuti azichita chinthu chomwecho. Mukuona? Iwo akusonkhana ndipo akudzipanga okha chipembedzo, wina aliyense akuyesetsa kuti amupose mzake. Ndipo tsopano iwo ali nako kuwala

kochuluka kwambiri, iwo sakudziwa choti azichita koma kuti ayanjanitse izo ndi mpingo wa Katolika. Mukuona? Lusifara kachiwiri akumanga ufumu wawukulupo, kuti awakankhire panja anthu amene samakhulupirira mu zipembedzo; ndipo ngakhale kutenga manyumba awo a tchalitchi ndi kuwapanga zipinda zosungira zinthu, ndipo azibusa a zoterozo kukhala opanda maufulu nkomwe.

547 Ndipo munthu yemwe ali munthu wotumidwa ndi Mulungu sangakhoze konse kukhala mu chipembedzo atatha kumvetsera Izi kapena kuziwona Izi, ngati iye—ngati iye ali nazo zokwanira kuti apite ndi kukayang'ana pa izo. Ndithudi. Mukuona? Ine sindikunena zimenezo motsutsa; ine ndikunena izo mwachoonadi, mwaona, atawona izo zikuwululidwa.

548 Zindikirani, mmasiku otsiriza ano, Lusifara akuchita chinthu chomwecho. Kodi inu mukukhoza kuziwona izi? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mdierekezi akuchita chinthu chomwecho, akumanga mpingo wa haibridi, haibridi ndi mamembala a haibridi, haibridi mwa chidziwitso mmalo mwa Mawu, ndi munthu waluntha mmalo mwa munthu wobadwa kachiwiri, kumanga ufumu waluntha umene uti uwale kuposa gulu laling'ono kwambiri la Khristu. Mukuona? Ndi chiyani chimene chinachititsa zimenezo? Angelo akugwa.

549 Baibulo linati anali angelo akugwa amene anamvetsera kwa Lusifara mmalo mwa Khristu, Yemwe iwo nthawiyina anali ake. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

550 Tsopano mvetserani mwatcheru, "angelo akugwa." Ndi angelo a mtundu wanji? Luther, Wesley, Katolika, Achipentekoste, amene sanasunge malo awo oyamba monga Angelo anachitira, ndipo agwera mu bungwe, monga kugwira kwakukulu kwa Lusifara ku Nicaea. Ndipo kodi iwo achita chiyani? Apanga bungwe gulu lalikulu la ecumenical la azitumiki, kuti akapange "chifano kwa chirombo," monga Baibulo linanenera. Ndipo akumanga chuma cha Chikhristu chimene chiti chidzatseke zitseko za mpingo uwu ndi ina yonga iwo. Mukumuona Lusifara pa ntchito yake?

551 Ine ndikuyetsetsa kuti ndikubweretsereni inu vumbulutso lofutukuka patatu, kapena chinsinsi cha Mulungu.

552 Kodi iwo anachita chiyani? Anadzigulitsa ku kulingalira kwa nzeru ndi maphunziro, monga Eva anachitira, angelo akugwa anachitira. Wesley anali munthu wa Mulungu; koma nchiyani chinamutsatira iye? Angelo okugwa anadzalowa mmenemo. Kodi angelo anali chiyani, poyamba? Zinthu zolengedwa za Mulungu, koma anagwa chifukwa chofuna nzeru za Lusifara, anagwa chifukwa chofuna Lusifara—nzeru za Lusifara. Ndipo inu mukuona chimene iwo anadzakhala? Angelo okugwa. Ndipo mabungwe, ochokera kwa amuna a Mulungu amene apita konsekonse kuti akakhazikitse Zoonadi mu dziko

lapansi; Choonadi icho chisanapitirire ndi kulengezedwa ndi kufika kwa vumbulutso lenileni la Khristu, angelo okugwa anabwera mmenemo ndipo anadzatenga nalamulira izo ndipo anapanga zipembedzo kuchokera mwa izo.

553 Ndi chifukwa chake vumbulutso la chinsinsi cha Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri chinkayenera kuti chifutukulidwe.

554 Tsopano inu mukuziwona izo? Zimene iwo anazisiya, ngati Luther akanapitirira nazo, izo zikanakhala ziri pano. Ngati Wesley akanati apitirire nazo, ngati Pentekoste ikanati ipitirire, kodi iwo akanachita chiyani?

555 Tsopano pali chinthu chimodzi chokha chimene chingakhoze kuchitika. Payenera kudzakhala Uthenga pa nthawi yotsiriza, pamene kulibe kanthu kalikonse kakukhoza kuwutsatira Iwo. Ndipo tsopano dziko la ecumenical lakhazikitsa ufumu woterowo kuti sipangakhoze kukhala chipembedzo ndipo palibe kanthu kalikonse kotsatira izo; inu mwina muli mu izo kapena inu simuli mu izo. Chipatso chiri pamwamba pa mtengo, ndipo Kuwala kukuwalira pa chipatso chokonzedweratu icho. Ndipo icho chikucha kukhala chipatso chonga Khristu, chikubweretsa kufewa komweko ndi kukoma, ndi Mzimu womwewo umene Iye anali nawo mwa Iye. Ndikuyembekeza inu mukuziona izo! Mukuona?

556 Ine—ine ndikuyesetsa kuyika zochuluka kwambiri mu tsiku limodzi. Ine ndikukutopetsani inu. [Osonkhana akuti, "Ayi."—Mkonzi].

557 Chotero, penyani, iwo anadzigulitsa ku kulingalira, anadzigulitsa ku kulingalira kwa chipembedzo. "Ngati nditangokhala wa *uwu*! A—ameya amapita ku mpingo umenewu." Mukuona? "Ngati ine nditakhala wa Methodisti, kapena wa Presbateria." Tangowonani kumene iwo apita. Tsopano, ine ndangofotokoza kumene, nthambi zimenezo zadulidwa. Izo zafa. Izo siziri zolumikizidwa ndi Khristu panonso; izo bwezi zikubweretsa Moyo womwewo. Izo sizinalumikizane ndi Iwo.

558 Koma izo ziri—izo ziri monga chipatso cha citrus. Chipatso cha citrus chirichonse chingakhale moyo pa mtengo wa citrus, koma chizibala chipatso chake chomwe. Inu mukaika chipatso cha manyumwa mu—mu mtengo wa lalanje, icho chizikhala moyo ndi mtengo wa lalanje, koma icho chizibala chipatso cha manyumwa. Inu mukaika mandimu mmenemo, iwo ndi chipatso cha citrus, iwo azibala mandimu owawasa akalewo, koma iwo azikhalira moyo pa moyo wakewo. Ndipo ndizo zimene zipembedzo zikuchita, mwa pansi pa dzina la mpingo.

559 Ndi Mkwatibwi yemwe ali Mtengo wapachiyambi, Mzimu wapachiyambi. Vumbulutso limachokera kwa Khristu, osati chipembedzo. Khristu! Zindikirani.

560 Kodi chipembedzo chikuyesera kumachita chiyani? Kudzikweza chokha, monga Lusifara. Iwo amangodzitcha okha "Mpingo, Mkwatibwi." Chimene, iwo ali mu Chivumbulutso 17, monga izo zikuyankhulidwa, mkwatibwi wabodza. Pamwamba pa gulu laling'ono la Khristu, Mkwatibwi; Lusifara akuganiza ndipo akudzikweza yekha pamwamba pa Mawu odzichepetsa a Choonadi cha Mulungu mwa chidziwitso cha vumbulutso, ndipo wadzikhazika yekha pogwiritsa ntchito maphunziro a seminare ndi fioloje mpaka iwo adzikweza okha pamwamba. Ndipo ngati iwe siuli wa mu gulu lawo, ndiye iwe ndi chamngalande.

561 Monga Lusifara anachitira pachiyambi, akunena kwa anthu ndendende basi chimene Lusifara ananena kwa Eva, "Ndithudi Mulungu adzatilandira ife! Ife timadyetsa osauka." Izo nzabwino. "Ndithudi Iye adzatilandira ife. Ife ndife chipembedzo chachikulu. Ife ndife mpingo wokongola. Bwanji, tayang'anani pa manyumba athu aakulu! Tayang'anani pa umembala wathu waukulu. Ife timafika mmamilioni. Ndithudi Mulungu sadzaliponyera pansi gulu limenelo."

562 Chinthu chomwecho chimene Kaini anachita, anabweretsa mmenemo zipatso zokongola kuchokera mu nthaka imene iye ankailima, ndi kuvutikira, ndi kugwira ntchito, ndi kubweretsamo zipatso, ndipo anawakana magazi onyozeka a mwanawankhosa.

563 Mulungu achite chifundo, kuti amuna ndi akazi asaganize kuti ine ndikunena izi kuti ndikweze chinachake, kapena vumbulutso lina landekha kapena chinachake. Ine ndikungokuwuzani inu Choonadi. Kodi inu simungakhoze kuwona zomwe iwo akuchita? Mukuona? Ine ndikuyankhula izo mokweza ndi mozaza, koma iwe uyenera kuwukhomerera msomali mpaka iwo utalimba, ngati iwo uti ukuchitire ubwino uliwonse, mwaona, mpaka iwe utaziwona izo. Mukuona?

564 Tsopano, akunena kwa anthu, "Ndithudi! Inu mukutanthauza kuti mundiuze ine kuti mpingo wathu waukulu wa Katolika, umene waima nthawi yonseyi, Methodisti yaikulu yathu, ndi yonse imeneyo? Tayang'anani pa makolo athu!" Mukuona? Koma iwo anaswa Mawu a Ambuye. Ndipo Eva anali wa Mulungu, mmodzi wa Ake, ndipo iye . . . iye anali chochokera mwa Adamu; ndipo chifukwa iye anakaikira Mawu amodzi a Mawu a Mulungu, izo zinachita izo.

565 Ndipo pano pali Lusifara pa ntchito yake kachiwiri, lero. Ndipo, kumbukirani, wotsutsakhristu si chikominisi. Wotsutsakhristu ndi woyandikana kwambiri ndi chinthu chenichenicho, mpaka, "Izo zikanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati izo zikanakhala zotheka," Yesu anatero, Mateyu 24, "Osankhidwa ngati kukanadzakhala kotheka." Lusifara, kachiwiri, Lusifara kachiwiri akuswa chiyanjano cha Mulungu mwa munthu, pa wake—powapatsa malire Mawu a Mulungu ndi

kulingalira kwakeko. Zimene iye akuganiza kuti ndi zolondola, ndipo zimene akuganizazo, iye akuswa nazo Mawu a Mulungu.

566 Ndipo chinthu chomwecho chimene iye anachichita mmasiku a Yesu. Ndipo Yesu anati, "Inu, ndi miyambo yanu, mwawapanga Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu."

567 Ndipo zipembedzo, mwa kulingalira kwawo kwachibungwe kwaluntha, kwapangitsa Mawu a Mulungu kukhala opanda mphamvu pa anthu. Ndiko kulondola. Iwo akulephera basi kuwawona Iwo. Ndiye iwo akumati, "Alikuti Mulungu wa Baibulo?" Iye ali pomwe pano. Iye ndi Baibulo, ndicho chimene Iye ali.

568 Zindikirani, tsopano, Lusifara akubwera mwa machenjerero, ndipo akudzaswa chiyanjano cha Mulungu kwa munthu, chimodzimodzi monga momwe iye anachitira mu Edeni, ndi mayesero aakulu a malonjezo a mphamvu-zawekha ndi kuzikweza. "Bwanji, iwe mwina ungakhale bishopu ngati iwe utangokhala ndi ife. Iwe mwina ungakhale woyang'anira boma. Bwanji iwe ukupita kwa chinachake chonga Icho?" Mwaona, ndicho Chipentekoste, Akatolika, ndi ena otero; mwaona, lonjezo lalikulu labodza, kwa munthu, kuti alandire mphamvu kunja kwa Mawu ndi lonjezo la Mulungu. Inu mudzalandira Mphamvu pamene Mzimu Woyera udzadza pa inu, osati pamene inu mudzakhala bishopu, kapena dikoni, kapena chirichonse chimene iye anali. Mukuona? Koma Lusifara ali pa ntchito yake panonso.

569 Kodi mpingo uno ukuzimvetsa izo? Kwezani dzanja lanu kuchitira kuti ine ndiwone zimenezo. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Chabwino, ine sindikhala ndi izo motalika panonso, ndiye.

Kusweka kuchoka, kuchoka ku Mawu a Mulungu! Mukuona?

570 Iye anachita chomwecho ku Nicaea, Roma. Inu mukudziwa chimene Konstantini anawapatsa iwo? Inu munadutsa Mibadwo ya Mpingo. Iye anapereka. . .Iwo anali wopanda kanthu, koma Khristu basi. Ndipo ankakhala ntimanyumba takale tating'ono kulikonse kumene iwo akanakhoza, pansi polimba ngati thanthwe. Inu mukudziwa zimenezo, ngati mutatenga *Bungwe la Nicaea* ndi *Pre-Nicaea Council,* ndi *Nicaea Fathers*, ndi zina zotero, ndi mbiriyakale mu mpingo. Iwo analibe kanthu. Koma pamene iwo anakhala ndi khonsolo iyi ndipo nalowetsamo zina zachikunja cha Chiroma mu Chikhristu, ndi kuikamo amuna oyera ndi mabishopu, ndi zina zotero, ndi mapapa, ndi mtundu wonse uwu wa zamkhutu, kodi Konstantini anawapatsa iwo chiyani? Ine ndikufunsa wazafioloje aliyense kuti andiuze ine. Iye anawapatsa iwo katundu. Iye anawapatsa iwo ufulu ndi zonse zimene iwo ankasowa.

571 Ndipo iwo anasinthanitsa Mawu a Mulungu pofuna nzeru ndi chitukuko cha munthu! Ndipo ndicho chinthu chomwecho

chimene Lusifara anachita nthawi imeneyo, iye anachita mmunda wa Edeni, ndipo iwo anafera apo pomwe. Mpingo wa Chipentekoste unafera ku Nicaea, Roma, koma kuti udzawukitsidwe mu Mtengo wa Mkwatibwi mmasiku otsiriza.

572 Zindikirani, Lusifara akubweramo, mochenjera, monga iye anachitira nthawi imeneyo, ndipo mwa mayesero ndi malonjezo abodza, a mphamvu zakunja, pambali pa Mawu a Mulungu. Iye anachita zomwezo ku Nicaea, Roma. Iye akuchita zomwezo lero ku Bungwe la Mdziko la mipingo ya Ecumenical.

573 "Tiyeni tonse tiyanjane limodzi," papa amatero. "Ine ndikufuna abale anga onse a ecumenical kunja uko kuti ayanjane ndi ine. Ife ndife mmodzi." Ndiko kulondola, mu mabungwe inu ndinu mmodzi. Koma izo ziribe chochita ndi Mkwatibwi wa Khristu; osati kanthu, m'bale. Inu simudzamutsuka konse Iye mu chirichonse chonga icho.

574 Tsopano izo zinalonjezedwa, mmasiku otsiriza, kuti Chikhulupiriro chapachiyambi mofanana . . . kuti chidzabwezeretsedwa kwa ana a Mulungu pa nthawi ya Mtengo wa Mkwatibwi. Malaki 4, Mulungu anati, "Dziko lisanawotchedwe ndi moto, taonani Ine ndidzakutumizirani inu Eliya mneneri, ndipo iye adzabwezeretsa Chikhulupiriro cha ana." Tsopano, uyo sanali Eliya woyamba kuti adze. Ayi, ayi.

575 Tsopano, ife sitimaphunzitsa pano za chovala cha Eliya ndi mabulangeti a Eliya, ndi zinthu zonse izo monga chomwecho. Ife timangophunzitsa Mawu a Mulungu. Mukuona? Ndicho chimene Iye ananena. Mwaona, ife tiri nawo mtundu wonse wa Eliya *uyu* ndi Eliya *uyo,* zimene ziri zamkutu. Ndizo—ndizo . . . Ife tikuzidziwa zimenezo. Ndizo . . . Ine sindikuyankhula za zimenezo, ndipo inu amene muli amalingaliro-auzimu mukumvetsetsa. Mwaona, popeza tachedwa, ora likufika pochedwa, ndipo sindingakhoze kuziyika izo zonse pa tepi iyi, ndithudi.

Tsopano, lonjezo mmasiku otsiriza. Tsopano ngati . . .

576 Yesu anati, mu—mu Mateyu, ine ndikukhulupirira, mutu wa 11 kapena mutu wa 6, ndi wa 11 . . . Ayi, ndi mutu wa 11 ndi pafupi ndime ya 6. Pamene Yohane anatumiza ophunzira ake kumeneko kuti akawone ngati Iye kwenikweni anali Iyeyo, Yesu anati, "Kodi inu munapita kukawona ndani? A—a—mphepo . . . bango lomwe likugwedezeka ndi mphepo? Kodi inu munapita uko kuti mukawone *chakuti-ndi-chakuti*?" Iye anati, "Kapena kodi inu munapita kuti mukamuwone mneneri?" Iye anati, "Woposa mneneri." Yohane anali woposa mneneri; iye anali mtumiki wa Pangano. Ndipo Iye anati, "Ngati inu mungakhoze kuzilandira izi, uyu ndi iye yemwe anayankhulidwa ndi aneneri, 'Ine ndidzatuma mtumiki Wanga patsogolo pa nkhope Yanga.'"

577 Tsopano, ndizo mu Malaki 3, osati Malaki 4. Chifukwa, Elisha yemwe anali woti adzadze mu Malaki 4, dziko linali

loti lidzawotchedwe ndi kutentha kwakukulu, ndipo olungama anali oti azidzayenda mu Zakachikwi pa maphulusa a oyipa. Mukuona? Chotero izo si ameneyo. Mukuona?

578 Tsopano tikuwona lonjezo liri kukwaniritsidwa. Khristu, Mutu woona ukupita mmenemo, ukubwera mwa Mkwatibwi Wake, kumadzachita ntchito zomwezo zimene Iye ankazichita pachiyambi, ndipo akukonzeketsera ndi kukwaniritsa Mawu Ake monga Iye anachitira, poyamba, mu Yohane 14:12, "Iye amene akhulupirira pa Ine ntchito zimene Ine ndikuzichita iye adzazichita nayenso." Ndiye, Mutu ndi Thupi zikukhala Mmodzi, mu ntchito ndi mu chizindikiro ndi mu Moyo, zotsimikiziridwa ndi Mulungu Mwiniwake kupyolera mu Mawu Ake olonjezedwera ku masiku otsiriza. Iye analonjeza izi mmasiku otsiriza. Tsopano, ngati ndinu auzimu, inu muzigwira izo.

579 Ndiye, ife tikhoza kuwona kuti Mgonero wa Chikwati uli pafupi. Tsopano, ngati ine sindidzakuwonaninso inu, kumbukirani, Mgonero wa Chikwati uli pafupi. Ndiyeno Ufumu malingana ndi lonjezo wakonzeka kuti uyambitsidwemo, Zakachikwi zopambana, kutengedwera mmwamba kwa Mpingo, ndi kuwononga kwa oyipa. Ndi dziko lapansi, pansi pa Chisindikizo cha Chisanu Ndi Chimodzi, kuti liyeretsedwe ndi ziphala zamoto, kudzachotsa chivundi chonse ndi tchimo la mdziko ndi kuliwumba ilo kachiwiri, ndi kubweretsapo Zakachikwi zatsopano zowala kwa m'badwo umene uli nkudza.

580 Pamene, ife tiwona zonse izi, vumbulutso lalikulu lofutukuka patatu: Mulungu mwa Khristu; Khristu mu Mpingo; Ufumu kudza. Adamu ndi Eva atawomboledwa kubwerera kumunda wa Edeni, mwa kuyimiridwa kwa Khristu ndi Mkwatibwi Wake, ndiyeno Ufumu ubwezeretsedwa molingana ndi lonjezo Lake. Mayamiko akhale kwa Mulungu! Tsopano, mwa vumbulutso la chinsinsi chofutukuka patatu, chinsinsi, ndi mwa Mawu otsimikiziridwa pawokha mwa Mutu Wake wapachiyambi!

581 Osati kuti, "Chabwino, ulemelero kwa Mulungu, ife timafuula; aleluya, ife timaimba." Izo si ndizo. Ine ndine mmishonare. Ine ndakhala ndiri ka seveni, mwakuchita, kuzungulira dziko lapansi. Mukuona? Ine ndawawonapo achikunja, adierekezi, ndi china chirichonse, akuvina ndi kufuula. Ine ndawonapo mitundu yonse ya mawonetseredwe achithupi. Ndizo zachithupithupi.

582 Koma ine ndikuyankhula za Mutu wa Khristu. Zindikirani, pokhala ozindikiritsidwa aliyense payekha ndi Mutu wapachiyambi, ife tiri nalo yankho kwa funso la mdierekezi. Ameni! Ulemelero! Ife tiri nalo yankho ku funso la mdierekezi. Iye, Khristu, wauka ndipo walipira mtengo, ndipo akuwuutsa Mutu . . . kapena Thupi.

583 Mdierekezi sangakhoze kupirira zimenezo. Ndi chifukwa chake maufumu achi ecumenical awa akukhazikitsidwa. Ndi chifukwa chake iwo onse akubwera mu chimene iwo akuchita tsopano. Mdierekezi, ndi chifukwa chake iye akuchita ukali momwe iye akuchitiramu. Uthakatu wake wakhala uli. . . machenjerero ake avundukulidwa ndi wowuka, Khristu wowukitsidwa mu Umutu pa Thupi Ili. Ulemelero!

584 Inu mukuganiza kuti ine ndasokonezeka? Ine sindinatero. Ife tiri nalo yankho la mdierekezi. "Si ine amene ndikukhala moyo, koma Khristu Mawu akukhala moyo mwa ine." Ilo si lingaliro langa; ndi Mphamvu Zake. Osati lingaliro langa; ndi Mawu Ake. Iye analonjeza zimenezo; ndi izi apa. Iye anati izo zikanadzakhala kuno, ndipo ndi izi apa. Ife tiri nalo yankho lake.

585 Khristu wawuka ndipo walipira mtengo wa chiwombolo chathu. Chimene Mulungu mwa Khristu anawonetsera, Iye anapereka thupi lija, ilo ndi Magazi; kuti mu Magazi mukakhoze kuchokera Moyo, ndipo thupilo nkuwomboledwapo, kuti—kuti Mulungu mu mnofu wowomboledwa uwu akakhoze kuwonetsera Mawu Ake a tsikuli monga Iye anachitira mu tsiku limenelo. Psyii! Ulemelero!

586 Inu mukuziona zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Oh, mai! Kodi ndiyimire pati? Muwone zimenezo. ["Tizipitirira!"]

587 Ndiye, ife tikuima olungamitsidwa mu Kukhalapo kwa Mulungu. Monga dontho la inki ikugwera mu a—a—mphika wodzaza bulitchi, inu simudzalipeza konse dontho la inki aponso. Ilo lapita kwinakwake. Ilo silidzabwerera konse kachiwiri. Ndipo pamene munthu awomboledwa moona, Mbewu yokonzedweratu iyo imene imawawona Iwo ndi kuwalandira Iwo, machimo ake awonongedwa. Iwo apita. Iwo alekanitsidwa. Iwo agwetseredwa mu inki ya—ya Magazi a Yesu Khristu, ndipo iwo sadzakumbukiridwa nkomwe. Mulungu amawaiwala iwo. Ndipo iye amaima monga mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu, mu Kukhalapo kwa Mulungu. Ameni ndi ameni! "Tsopano ife ndife ana a amuna a Mulungu." Osati ife *tidza*khala tiri; ife tiri! Tsopano ndife owomboledwa.

588 Ife tiri nalo yankho la Satana. Mulungu wadzitsimikizira Yekha. Mulungu akudzitsimikizira Yekha, kwa lonjezo Lake mu tsiku lino. Aleluya! Mutu uli pano. Ameni! Khristu, Ambuye wowuka, ali pano mu Mphamvu yomweyo ya chiwukitsiro Chake yomwe Iye nthawizonse anali, akudziwonetsera Yekha. Limenelo ndiro yankho la mdierekezi.

589 Ndi chifukwa chake pamene munthu uyu wakhala pano, anagwa ndi kufa tsiku lina, atakhala pano, ife tinakhoza kunena kuti, "Bwereranso, moyo!" Chifukwa, Mzimu Woyera unanena chomwecho.

590 Ndi chifukwa chake izo zinakhoza kuchita kwa mwana wamng'ono uja uko mu Mexico, yemwe anali atafa kwa pafupifupi maora fifitini, pamene masomphenya anabwera ndi kudzati, "Muitane iye abwerere ku, dea . . . moyo." Ndipo ndinati, "Mwana wamng'onoyo akhale moyo." Ndipo mwana yemwe madokotala analemba chikalata, anafa pa naini koloko mmawa umenewo, ndipo leveni koloko usiku umenewo anabwereranso ku moyo; ali moyo lero.

591 Ndi chiyani chimenecho? Osati anthu amenewo. Mutu ndi Thupi zadzakhala chimango chimodzi. Ndi Mulungu akuwonetseredwa mwa anthu Ake. Ndi chifukwa chake mwamuna ndi mkazake salinso konse awiri; iwo ndi mmodzi. Mulungu ndi Mpingo Wake ndi mmodzi, "Khristu mwa inu," vumbulutso lalikulu la Mulungu. Ulemelero kwa Mulungu! Ngakhale kutenga Dzina Lake; Dzina Lake ndi Yesu, Wodzozedwayo. Chifukwa chimene Iye akutchedwa Yesu, Iye ndi Wodzozedwayo. Ndi Thupi lodzozedwa la Khristu, kutsimikizira, kuwonetsera Mulungu monga thupi Lijalo linachitira. Ndipo thupi Lijalo linawombola chirichonse cha izi, matupi awa, ndipo kupyolera pamenepo Mulungu akugwira ntchito mawonetseredwe Ake ofutukuka patatu, kupita ku Ufumu. Atauka, analipira mtengo! Ndife owomboledwa. Mulungu watsimikizira zimenezo, wazitsimikizira izo. Mukuona?

592 Ndipo ife tikuima olungamitsidwa mwa Khristu, pamaso pa Iye. Chifukwa, Iye sangakhoze kupereka chiweruzo, pakuti Iye waliweruza kale Thupi limenelo, momwe ine ndiri gawo lake. Chiyani, ine ndiri bwanji gawo la ilo? *Pano* ndi Izi; Iwo uli mwa ine. "Ngati Anga . . . inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu, ndiye zimene inu munena . . . Afunseni Atate chirichonse mu Dzina Langa, icho chidzachitidwa, chifukwa Iwo uli pamenepo." Olungamitsidwa! Ulemelero kwa Mulungu!

593 Oh, ngati nditakhoza kulitengera dziko kuti liziwone zimenezo! Bwanji? Ndi zimenezotu pamenepo. Ndi limenelo Thupi la Khristu wamoyo, litaima lowomboledwa. Owomboledwa! Oh, mai!

594 Wolungamitsidwa pamaso Pake! Ndi chifukwa chiyani ife tiri olungamitsidwa? Ife ndife chigonjetso Chake. Mpingo ndiwo chigonjetso Chake. Ife tabwera mmasiku otsiriza ano ndi Uthenga waulemelero uwu, kudzasonyeza chigonjetso Chake. Iye anafera cholinga ichi, ndipo ife tiri chitsimikizo cha chigonjetso Chake. Ameni! Pamene ife tikumuwona Iye akutsika ndi kudzakhala moyo pakati pa Mpingo, ndicho chigonjetso Chake. Zikusonyeza kuti iye sakanakhoza kumusunga Iye mmanda, ngakhalenso iwo sangakhoze kutisunga ife. Ndiko kulondola. Ife ndi wa kumeneko moona. Ndipo ife tiri kale, mwakuyankhula kwina, owukitsidwa, chifukwa ife tinawuka kwa akufa, kusakhulupirira mu Mawu Ake, tachoka ku

tizikhulupiriro ta chipembedzo, tapita ku Mawu Amuyaya a Mulungu Wamuyaya; chimene chiri Iye, Mwiniwake, akugwira ntchito kupyolera mwa ife, kudziwonetsera Yekha kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

595 Ndiyeno Mawu akusunthirabe pansi mpaka mu Thupi, kuchokera ku Mutu. Ndi chiyani icho? Mawu omwewa. Palibe chimene chingakhoze kuwonjezeredwa kapena kuchotsedwa kwa Iwo. Chotero Mawu omwewo akusuntha kuchokera ku Mutu, pamene Tsiku likufika pafupi, kumatsika mpaka mu Thupi, kutsika mpaka mu Thupi, kutsimikizira kuti iwo ali Mmodzi. Iwo ndi Mwamuna ndi Mkazake. Iwo ali mnofu wa mnofu Wake, Mawu a Mawu Ake; Moyo wa Moyo Wake, Mzimu wa Mzimu Wake. Mukuona? Ameni! Inu mukuzidziwa bwanji zimenezo? Zikuchitira umboni womwewo, chipatso chomwecho, Mawu omwewo. Mukuona? kuwonetsera Khristu; Moyo womwewo, Mulungu yemweyo, Mzimu womwewo, Mawu omwewo, Bukhu lomwelo! Ameni! Zizindikiro zomwezo, "Zinthu zimene Ine ndikuchita mudzazichita inunso." Oh, aleluya! Mai!

596 Zindikirani, Mawu otsimikiziridwa mu Thupi Lake ndicho chigonjetso Chake chomwe ndi chifukwa cha imfa Yake. Mwaona, imfa, osati mu Mzimu; pamene Iye anafa, Iye anangofa mu thupi basi. Mzimu Wake unapita ku gehena ndipo unakalalikira kwa miyoyo ya mndende. Kulondola uko? Thupi lake, lokha, linafa, kenako Iye analiwukitsa ilo kachiwiri ndipo analifulumizitsa ilo. *Kufulumizitsa* kumatanthauza "kupangidwa wamoyo," mnofu Wake, umene unali thupi Lake. Ndipo ndiwo Mawu. Iwo akhala ali akufa kwa zaka, koma Iwo mwapang'onopang'ono anayamba kubwera mu kukonzanso, ndipo tsopano Iye akuima pa mapazi Ake!

597 Oh, momwe ine ndikukhumba ndikanakhala nayo nthawi kuti ndibwerere ku Ezekieli, ndi kukasololamo "mafupa owuma," aja ndi kukusonyezani inu. Iye anati, "Kodi mafupa awa angakhalenso moyo?"

Iye anati, "Nenera!"

598 Uneneri ungakhoze kubwera chotani? Kokha kupyolera mwa mneneri. Ndiwo Mawu a Ambuye. "Mverani inu, mafupa owuma, Mawu a Ambuye!" Ndipo minyewa, khungu zinabwera pa iwo, ndipo iwo anaimirira ankhondo amphamvu, ndipo anayamba kuguba waku Zioni. Ulemelero kwa Mulungu! Ndi Iyeyo. Ndi Iyeyo, chigonjetso.

> Owomboledwa a Ambuye adzabwera ku Zioni
> ndiye ndi chisangalalo,
> Mapiri Ake onse oyera, palibe chopweteka
> kapena chiti chidzawononge. (Huh.)

599 Iye akutsimikizira Moyo Wake wa chiwukitsiro ndiye pamene Iye akudzitsimikizira Yekha. Iye, Mkwatibwi,

ndi woyimapayekha kwa ena onsewo. Iye ndi Mkazi woyimapayekha, Mbalame yaikulu yamangamanga imene ili yosiyana ndi zina zonsezo. Inu mukukumbukira Baibulo pa zimenezo, "Mbalame yaikulu ya mangamanga." Koma, Iye anali nalo Dzina Lake, Iye anali nawo Moyo Wake. Pakuti . . .

600 Kodi iwo ankaipangitsa mangamanga bwanji mbalameyo? Izo zonse zimakhala zoyera, ndipo kenako iwo ankadulapo mutu wa mbalame imodzi ndi kutsanulira magazi pa mbalame inayo. Ndipo mbalame inayo imadzakhala yamangamanga ndi magazi ofiira, ndipo iyo inkakupiza mapiko ake monga *chonchi,* ndipo magazi ankafuula, "woyera, woyera, woyera," pamene iyo inali kusambitsa nthaka.

601 Chotero Khristu, Mzathu wakufa, anadzayika Magazi Ake, Magazi Ake ochokera mu Moyo Wake, kudzabwera mwa ife; kuko-. . .kunyamula Magazi Ake, akulira, "Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye!" Iyo ndi mbalame yowoneka-mwachirendo. Zedi, iyo ili. Koma Iye, Mkwatibwi, ali—akuzindikiritsidwa ndi Iye, ndipo Iye ndi woyimapayekha kwa ena onsewo. "Khalanibe inu kwa iye yekha utali wonse ngati inu nonse muli amoyo. Khalanibe inu kwa Iyeyekha, Mawu," popanda, popanda chigololo, popanda chisonyezo chimodzi cha chipembedzo, popanda chisonyezo chimodzi cha kachikhulupiriro, popanda chigololo konse. Mawu, ndipo Iye yekha!

602 "Pa Khristu thanthwe lolimba ine ndaima, maziko ena onse ndi mchenga wotitimira," anatero Eddie Perronet. Uh-huh.

603 Ndi zimenezo, Khristu, Mawu! Iye anali Mawu; Iye ndi Mawu. Ndipo Mpingo ukukhala Mawu, mwanjira ya Iyeyo kuwupangitsa Iwo kukhala gawo la Iye, ndipo ndiwo Mawu kachiwiri. Kuzindikiritsidwa pawokha ndi Iyeyo, chuma Chake yekha! Chuma Chake yekha! Iwo wawomboledwa ndi Iye, kudzera mwa Iye, kwa Iye, ndi kwa Iye yekha. Ndiko kulondola. Ndiye, chimene mdierekezi akuchitira ukali, ndi chakuti izo zikuwululidwa.

604 Ife tiri mu nthawi yowopsya. Kumbukirani, Lemba limati, pamene zinthu izi zidzayamba kuchitika, "nthawi siyidzakhalaponso." Iyo ikuzimirira kutali, pamene ife tikuwona mawonetseredwe.

605 "Zivomezi." Inu mukuona zikwi aja anaphedwa tsiku lina lija? "Zivomezi mmalo osiyanasiyana."

606 Anati, "Zowoneka zowopsya mmilengalenga, malawi a moto," monga, kumayandama pamenepo monga mbale zowuluka. Iwo sakudziwa chimene izo ziri. Mukuona? Iwo alibe lingaliro lirilonse.

607 Kodi inu munazindikira Angelo amene anatsika pansi, anafufuza Sodomu asanawonongedwe Sodomu? Inu mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—

Mkonzi]. Panali gulu la iwo amene anabwera kumeneko, atatu a Iwo. Mmodzi wa iwo anatsalira ndi Abrahamu. Inu mukukumbukira zimenezo? [“Ameni.”] Iko kunali Kuwala kochokera Kumwamba, kumene kunabwera pansi mu kufufuza kwa chiweruzo. Amene . . .

608 Taonani kumene iwo onse akupezeka. Cha ku Pentagon, ndi zinthu, iwo anazipeza izo. Ndicho chiweruzo cha dziko lapansi, Sodomu. Ndipo kuli Mmodzi yemwe akuimiridwa, adzaimiririridwa pakati pa mipingo, adzakhala ali Khristu Mwiniwake, akudzitsimikizira Yekha. Mukuona? “Zowoneka pa . . . mmiyamba mmwamba, ndi zizindikiro mdziko mmusi.” Ndithudi.

609 Kuzindikiritsidwa! Oh, mdierekezi akuchita ukali ndi zimenezi: Choonadi chowonetseredwa cha lonjezo la Mawu mwa Mkwatibwi yekha.

610 Iwo alibe yankho. Pamene Yesu anabwera, anachita chiyani Afarisi aja? Iye anati, “Ngati Ine ndikutulutsa ziwanda ndi chala cha Mulungu, kodi inu mumatulutsa izo ndi ndani?” Mukuona? Iye anaima yekha.

611 Ndipo Mpingo Wake ukuima wokha. Iwo suli wolumikizana ndi kanthu kena. Koma Iye anazindikiritsidwa ndi Mulungu, pokhala thupi limene Mulungu ankakhalamo; ndipo Mpingo ukuzindikiritsidwa ndi Thupi Lake, ukuchita chinthu chomwecho. Iye ndi Thupi Lake, Choonadi chowonetseredwa cha Mawu Ake olonjezedwa kwa masiku otsiriza. Ndipo Iye, ndipo Iye yekha, akuima pambali pa Iwo. Ndi chifukwa chake mdierekezi akuchita ukali, mabungwe aakulu awa, kuti akhazikitse chinachake kuti chimutsekereze Iye. Iwo sadzachita konse zimenezo. Iye adzatengedwera mmwamba, osati kutsekerezedwa mmwamba. Iye tsopano wawukitsidwa, ndipo ndi mphamvu ya Mawu otsimikizidwa olonjezedwera kwa Iye. Ameni!

612 Momwe Mkwatibwi akugwirira lonjezo limenelo! “Iye anandiuza Ine kuti Iye akanati adzabwerere ine. Ine ndikhulupirira zimenezo.” Uh-huh. Mukuona? Inde, bwana. Kuti akakomane ndi Mutu Wake, Muomboli Wake, Mwamuna Wake, Mfumu Yake, Ambuye Wake, Womkonda Wake, Mpulumutsi Wake, mmalo operekedwa okumaniranapo!

613 Iye ali nawo malo oti akomane ndi Iwo. Inu mukudziwa, Iye—Iye . . . Mkwati sasiya kanthu kalikonse. Iye ali nayo mphete, chomuzindikiritsa. Iye ali nawo mwinjiro umene Iye akuvala, chovala Chake. Mukuona? Ndipo Iye ali nawo malo operekedwa kuti akakomane naye Mkwatibwiyo, umo ndi mu mlengalenga. Chirichonse chaperekedwa kale chonse. Iye wakonza kale Mgonero wa Chikwati; alendo ayitanidwa kale, asankhidwa kale. Angelo onse ayima pozungulira, antchito Ake, ali tcheru. Oh, oh, oh, oh, oh!

Oh, padzakhala kukomana mu mlengalenga,
Mokoma muja, mokoma posachedwapa;
Ndidzakomana nanu, ndidzakomana nanu Kumeneko
Kwathu uko kuseri kwa mlengalenga;
Kuimba komwe sikunamvedwepo, sikunamvedwepo ndi makutu achivundi,
Zidzakhala zaulemelero, ine ndikunenetsa!
Ndipo Mwana kumene wa Mulungu, Iye adzakhala Mmodzi Wotsogolera, (Mawonetseredwe athunthu a Mulungu.)
Pa kukomana kumeneko mu mlengalenga. (Oh, mai!)

614 Penyani kutsimikizira Kwake tsopano.

Inu munamva—munamva nkhani ya Mose mu chitsamba,
Munamva za Davide wopanda mantha ndi legeni lake;
Munamva nkhani ikunenedwa ya Yosefe wolota,
Ya Daniele ndi mikango timaimba kawirikawiri.
Oh, alipo ambiri, ambiri ena otsimikiziridwa mu Baibulo,
Ndikukhumba kudzakomana nawo, ine ndikunenetsa!
Posachedwa Ambuye adzatikumanitsa nawo iwo,
Pa kukomana uko mu mlengalenga.

Pakuti padzakhala kukomana mu mlengalenga,
Mokoma muja, mokoma posachedwapa;
Ndipo ndidzakakomana nanu, kukakulonjerani inu Kumeneko
Kwathu uko kuseri kwa mlengaleng;
Kuimba koteroko kumene kunayamba kwamvekapo, kunamvekapo mmakutu a chivundi,
Zidzakhala zaulemelero, ine ndikunenetsa!
Ndipo Mwana kumene wa Mulungu adzakhala Mmodzi wotsogolera
Pa kukomana kumeneko mu mlengalenga. (Oh, mai!)

615 Kodi inu simukuikonda imeneyo? Tsopano cholinga chofutukuka patatu cha chinsinsi Chake chachikulu cha vumbulutso chaululidwa. Iye ndi Mmodzi wofunikayo. Ndiye Mmodziyo. Oh, mai! Tiyeni tiyimbe iyo. Ine sindingakhoze kulalikiranso. Ine ndikumverera bwino kwambiri, mwaona.

Oh, padzakhala kukomana mu mlengalenga,
Mokoma muja, mokoma posachedwapa;
Ndipo ndidzakakomana nanu, kudzakulonjerani inu Kumeneko
Kwathu uko kuseri kwa mlengalenga;
Kuimba koteroko kumene kunayamba kwamvekapo, kunamvekapo mmakutu a chivundi,
Zidzakhala zaulemelero, ine ndikunenetsa!
Ndipo Mwana kumene wa Mulungu Iye adzakhala Mmodzi wotsogolerayo,
Pa kukomana kumeneko mu mlengalenga.

616 Kodi inu mukupita? Ameni! Mwa chisomo cha Mulungu, mwa chisomo cha Mulungu! Mukuona? Oh, mai!

Munamvapo za Mose wamng'ono mu chitsamba,
Munamvapo za Davide wopanda mantha ndi legeni; (Izo zonse ndi zoyimira.)
Munamvapo nkhani ikunenedwa ya Yosefe wolota,
Ya Daniele ndi mikango timaimba kawirikawiri.
Oh, alipo ambiri, ambiri ena ochuluka mu Baibulo, (Amene ali Iye.)
Ndipo ndikukhumba kudzakomana nawo onse, ine ndikunenetsa!
Posachedwapa Ambuye adzatilola ife kuti tikumane nawo iwo
Pa kukomana mu. . .

617 Koma alipo Mmodzi wofunikirayo!

Oh, padzakhala kukomana mu mlengalenga,
Mokoma muja, mokoma posachedwapa;
Ine ndidzakakomana nanu, kukakulonjerani inu Kumeneko
Kwathu uko kuseri kwa mlengalenga;
Kuimba koteroko kumene kunayamba kwamvekapo, kunamvekapo mmakutu a chivundi,
Zidzakhala zaulemelero, ine ndikunenetsa!
Ndipo Mwana kumene wa Mulungu, Iye adzakhala Mmodzi wotsogolerayo
Pa kukomana mu mlengalenga.

618 Tsopano, ife tidzakakomana wina ndi mzake Kumeneko. Tiyeni tonse, Amethodisti, ndi Abaptisti, ndi chirichonse chimene inu muli, amene anabadwa kachiwiri ndi Mzimu wa Mulungu, tigwirane chanza wina ndi mzake pamene ife tikuyimba iyo.

Oh, padzakhala kukomana mu mlengalenga,
Mokoma muja, mokoma posachedwapa;
Ine ndidzakakomana nanu inu, kukakulonjerani inu Kumeneko
Kwathu uko kuseri kwa mlengalenga;
Kuimba koteroko kumene kunayamba kwamvekapo, kunamvekapo mmakutu a chivundi,
Zidzakhala zaulemelero, ine ndikunenetsa!
Pakuti Mwana wa Mulungu Kumene adzakhala Wotsogolerayo
Pa kukomana mu mlengalenga.

619 Oh, oh, oh! Oh, ndizo zodabwitsa, mwaona, mukuona chimene Iye ati adzakhale. Tsopano penyani.

620 Ife tiyenera kuti tingotseka, abwenzi. Ndi pafupifupi thuu koloko, mwaona, ndipo ife tidza—ife tidzakhala kuno pa mgonero. Ine ndangotsala ndi tsamba pambuyo pa tsamba la izi panobe, mwaona, chotero ife tingoyenera kuti titseke pa izi. Palibe mapeto kwa zimenezo.

621 Ndi vumbulutso. Izo ziri ngati Muyaya monga Mawu a Mulungu ali Amuyaya. Penyani, koma cholinga chofutukuka patatu cha chinsinsi chachikulu cha Mulungu chawululidwa! Mulungu anawonetseredwa mwa Khristu; Khristu akuwonetseredwa mu Mpingo; pofuna kuti amuwombole Eva wotayika abwerere ku chikhalidwe chapachiyambi mmunda wa Edeni. Oh, mai!

622 Oh, padzakhala nthawi zina zazikulu pa Tsiku limenelo! Eya. Ndi pomwepo. Ife tikukhulupirira zimenezo. Kodi inu simukukhulupirira izo? Ine ndimangoganiza za nyimbo imeneyo nthawi zonse ine ndikamaganiza za zimenezo.

623 Iye anadzitsimikizira Yekha mwa Daniele, ndi mwa Mose, ndi mwa Yeremia. Kodi iwo anali chiyani? Aneneri amene Mawu ankabwerako, mwaona, amuna aakulu amenewo. Mwaona, inu munamvapo nkhani ikunenedwa ya Yosefe wolota, inu mukuona, ndi Daniele mu khola la mikango, ndi ena onse awa, inu mukudziwa. Iwo, amene, kodi iwo anali chiyani? Aneneri. Mukuona? Koma Mmodzi wamkuluyo . . . Mulungu anali basi, moyembekezera, akudzifanizitsa mwa iwo.

624 Iye anadzifanizitsa Yekha mwa Adamu, akudziwa chimene chinali cholondola, koma anayenda napita kuti akamuwombole mkazi wake, chifukwa iye anali atalakwitsa. Khristu sankayenera kuti akhale tchimo, koma Iye anayenda napita ndipo anakatenga tchimo, kuti amuwombole mwana Wake wotayika. Mukuona? Mukuona? Iye anadzifanizitsa Yekha.

. . . ndi Mose mu chitsamba,

Ndipo munamva za Davide wopanda mantha ndi legeni;
Inu munamva nkhani ya Yosefe wolota, (Mneneri.)
Ndi ya Daniele ndi mikango ife timaimba kawirikawiri.
Oh, alipo ochuluka, ochuluka ena mu Baibulo,
Ndipo ine. . .

625 Iwo, iwo ndiwo Baibulo.

Ndipo ine. . .

Iwo onse anawonetseredwa mwa Iye, chonchobe. Mukuona? Popanda Iye, iwo onse apita. Mukuona? Ndipo ine ndiyenera kuti ndikhale gawo la Ilo, kuti ndikhale Iye. Ameni! Mukuona?

Ndikukhumba kudzakomana nawo, ine ndikunenetsa. (Ndiko kulondola.)
Koma Mwana Kumene wa Mulungu, Iye adzakhala Mmodzi wotsogolerayo
Pa kukomana mu mlengalenga.

626 Ahebri 11, amati, "Iwo sangakhoze kukhala angwiro popanda ife." Manja ndi mapazi sizingakhoze kukhala zangwiro popanga ubongo, chidziwitso, mutu, ndi zina zotero. Mukuona? Ndipo ife tonse tikupangidwa angwiro mwa Iye, "Chotero mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi," afulu ku Chiweruzo; tadutsa ku tchimo, kupita ku imfa. . . Ameni! "Mwana wa Mulungu Kumene adzakhala Mmodzi wotsogolerayo pa kukomana kumeneko mu mlengalenga." Kodi inu mukumukonda Iye?

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa. . .

627 Ambuye Yesu, kudzoza kwa Mzimu Woyera kubwere pa mipango iyi, Ambuye, ndipo kudzachiritse odwala. Zikhale chomwecho, monga iwo ayika iyo pamenepo. Ine ndikupemphera kuti Inu muchipange izo chomwecho, mu Dzina la Yesu. Ameni.

. . . mtengo wa Kalvare.

628 Tangoganizani, "Khristu, wowululidwa," mkati mwathu momwemo, pakali pano mwa ife. Kodi Iye anachita motani, Iye anawululidwa chotani? Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine. Kodi Iye anachita chiyani?

Nandigulira chipulumutso changa
Pa. . .

629 Ulemelero! Mngelo wamkulu uja wa Pangano, Mmodzi uja Yemwe anali ndi Mose mu chipululu, Mmodzi uja Yemwe anadza kwa Paulo pa njira yaku Damasiko, Mmodzi yemwe uja analoleza chithunzi Chake kuti chijambulidwe ndi ife; Mmodzi yemweyo amene anali mu chithunzi mu magazini ya *Life*

tsiku lina; Mawu omwewo, mwa Mulungu yemweyo, kupyolera mmipita yomweyo, mwanjira yomweyo, mwa lonjezo lomwelo! “Paliponse pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa, Ine ndiri pakati pawo pomwe.” Ndiye Iye ali pano. “Angelo a Mulungu amazungulira iwo amene amamuwopa Iye,” amene amangokakamira ku Mawu Ake. Palibe munthu yemwe angakhoze kuwalemekeza Mawu amenewo popanda kumuwopa Mulungu. Mukuona? Ndiye, pano Iye ali pano mmawa uno, ndi ife, pamene ife tikumupembedza Iye mu Mzimu.

630 Oh, titatha Uthenga wolimba ngati uwu, ine ndikuganiza ife tikungoyenera kuti timupembedze Iye pang’ono pokha mu Mzimu. Onani, ingotsekani maso anu ndipo tiyeni tiyimbe iyo kwa Iye kachiwiri, “Ine ndinkonda Iye, ine ndinkonda Iye,” basi pamene inu—inu mukukweza manja anu, monga, kwa Iye.

> Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
> Chifukwa . . . anayamba kundikonda ine
> Nagula chipulumutso changa
> Pa mtengo wa Kalvare.

Oh, mai, momwe ife timamukondera Iye!

> Chikhulupiriro mwa Atate, chikhulupiriro mwa Mwana,
> Chikhulupiriro mwa Mzimu Woyera, atatu awa ali Mmodzi;
> Ziwanda zidzanjenjemera, ndipo ochimwa adzawuka;
> Chikhulupiriro mwa Yehova chimagwedeza zonse.

631 Ameni! Ulemelero kwa Mulungu! Momwe ife tikumukondera Iye! Zingomupembedzani Iye mu mtima mwanu tsopano, muzingomukonda Iye, basi—tangoganizani momwe Iye wazichitira izo mokongola. Tapenyani chimene Iye watichitira ife. Zaka zonse izi za masomphenya, palibe amodzi anayamba alepherapo. Chirichonse chimene Iye anati chikanati chidzachitike, chinadzabwera ndendende basi momwe Iye ananenera izo.

632 Ine ndikukukondani inu. Musaiwale malamulo a Mulungu kwa inu, ana aang’ono, “Muzikondana wina ndi mzake.” Muzimkonda aliyense. Wabwino kapena woyipa, wochimwa kapena woyera, akondeni iwo, mulimonse. Ngati inu simukutero, ndiye mupemphere kuti Mulungu akuthandizeni inu, chifukwa Mulungu anamukonda wochimwa. Ndipo chikhalidwe cha Mulungu chiri mwa inu. Ngati munthuyo akulakwitsa, mukondeni iye, mulimonse. Musatenge nawo a machimo ake. Mukuona? Musatenge nawo a machimo ake. Koma mwa kukoma, osati mwa kuwawasa ndi kudzudzula, mwa kukoma muwuzeni iye za chiyembekezo cha Moyo chimene chiri mkati

mwa inu, kudzera mwa Yesu Khristu amene wawululidwa kwa inu mwa Mzimu Woyera.

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana wachisoni ndi watsoka;
Lidzakusangalatsa ndi kukutonthoza iwe,
Oh, litengeni Ilo (Musati muiwale tsopano.) kulikonse kumene mukupita.

Oh, lofunika . . . (Dzina limenelo!) . . . O . . .

633 Ife tiri nalo Dzina Lake. Ife timatchedwa ndi Dzina Lake.

Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chisangalalo cha Kumwamba;
Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chisangalalo cha Kumwamba.

634 Tsopano ndikupatsani inu chinsinsi chaching'ono, mpaka ine ndidzakomanenso nanu, muzikumbukira izi, pamene ife tikuima, muzikumbukira izi:

Pa Dzina la Yesu kugwada,
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka Iye korona, (Ife tidzakamuveka Iye korona!)
Pamene ulendo wathu udzatha.

Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) (O kukoma kwakeko!)
Chiyembekezo cha . . .

635 Chiyani? Vumbulutso lofutukuka patatu! Chiyembekezo ndi chisangalalo cha Kumwamba, kuwululidwa mwa Iye.

Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha . . .

636 Chiyani? Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chisangalalo cha Kumwamba, chirichonse chikuwonetseredwa mwa Khristu. Mulungu, Mpingo, china chirichonse, chikuwonetseredwa mwa Khristu. Baibulo ndiro Khristu. Baibulo ndiro Mawu olembedwa. Chimene, Iye ndi Mawu. Mawonetseredwe Ake ndi umboni wa Moyo ukubwera mu thupi la Mawu, kuti awawonetsere Iwo. Oh, kodi izo si zodabwitsa!

Tenga Dzina la Yesu ndi . . .

Tsopano mvetserani mwatcheru pano.

Monga chishango . . . (Musaiwale zimenezo tsopano.) . . . msampha uliwonse;
Pamene mayesero akuzingani, (Kodi muyenera muzichita chiyani?)

Muzingopuma Dzina Loyeralo mpemphero.

Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) O kukoma kwakeko! (O kukoma kwakeko!)
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba;
Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba.

637 Mosadziwa. . .Indedi, pokhala wauzimu, iwe umayang'ana zinthu zauzimu. Mosadziwa izi; Mulungu akudziwa izo. Koma ngati mutatembenuka ndi kuyang'ana pa wotchi, iyo ili pa dontho, thuu koloko, kutha kwa Chikoka Chachiwiri. Chikoka Chachitatu chiri pafupi! Mukuona?

Pa Dzina la Yesu kuwerama,
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka Iye korona,
Pamene ulendo wathu udzatha.

Dzina lofunika. . .

Chikoka Chachiwiri chawonetseredwa!

Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba;
Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba.

638 Kodi inu munazindikira Mzimu unaitenga nyimbo yomweyo ndi kuyikwezera iyo mmwamba pa liwu lokwera monga choncho? Chikoka chotsatira chiri pafupi! Ameni! Uh-huh.

Tenga Dzina la Yesu nawe,

Nthawi yatha kuposa momwe inu mukuganizira!

. . .wachisoni ndi watsoka;
Lidzakusangalatsa ndi kukutonthoza iwe,
Oh, litengeni Ilo kulikonse inu mukupita.

Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba;
Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe. . .

Tsopano ngati mayesero abwera, inu mumachita chiyani?

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Monga chishango ku msampha uliwonse;

Pamene mayesero . . . (Chinachake choti chikupange iwe kusakhulupirira tsopano.) . . . akuzinga,
Ingokumbukira, puma Dzina loyeralo mu pemphero.

Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba;
Dzina lofunika, (Dzina lofunika!) O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba.

639 Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, aliyense, molemekeza. Penyani tsopano.

Pa Dzina la Yesu kuwerama . . .

640 [Malirime ndi kutanthauzira zikuperekedwa—Mkonzi]. Tsopano ngati inu mukumvetsetsa, Mzimu wa Ambuye unagwera mu msonkhano, pa zinenero zosadziwika, kuyankhula izo kwa munthu mosadziwa; kuti atanthauzire izo munthu wina mosadziwa. Mawu a Ambuye! Inu mukukumbukira pamene mdani anali kubwera ndipo iwo sankadziwa chomwe iwo akanati achite? Mzimu wa Ambuye umagwera pa munthu, ndipo umawulula chimene chinali choti chichitidwe. Oh, mai!

641 Tingoweramitsa mitu yathu tsopano, modzichepetsa. Mulungu akudalitseni inu.

Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!
Mpaka tidzakomane pa mapazi a Yesu;
Mpaka tidzakomane!

Chabwino, abusa.

63-0728 Khristu Ndi Chinsinsi Cha Mulungu Woululidwa
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org